


KUZINDIKIRITSA ZA CHIPHUNZITSO CHA M'BAYIBULO CHOKHUDZA MULUNGU



Issachar
Glorifying God by making Him Known

Zamkatimu

1.1 - Mawu oyamba	4
1.2 - Mphamvu ya nkhani	6
1.3 - Zichitochito za mu bayibulo	8
1.4 - Zitsunzo za Mmagawo	12
2.1 - Kulengedwa	14
2.2 - Kulengedwa kwa munthu mu chifaniziro chake	16
2.3 - Nsanamila za kulenga	20
2.4 - Njira ya bayibulo yokhudzana ndi kulenga	23
3.1 - Kugwa – Adamu ndi Eva	25
3.2 - kugwa – Kayini ndi Abele	27
3.3 - Kugwa – Kuwukira komanso madzi osefukira	30
3.4 - Kugwa – Njira ya bayibulo yokhudzana ndi kulenga	31
4.1 - Isilayeli – Pangano ndi Abulahamum	33
4.2 - Isilayeli – Mose ndi Chilamulo	36
4.3 - Isilayeli – Davide ndi Ufumu	37
4.4 - Isilayeli – Aneneri ndi chiyembekezo	39
5.1 - Yesu – Mfumu yomwe ikudza	40
5.2 - Yesu – Kukonzedwanso kwa Isilayeli	43
5.3 - Yesu – Ziphunzitso ndi Machenjezo	45
5.4 - Yesu – Kupachikidwa pamtanda	47
6.1 - Chilengedwe chatsopano – Kuwukitsidwa kwa Yesu	48
6.2 - Chilengedwe chatsopano – Kutumizidwa kwa Mzimu Oyera	50
6.3 - Chilengedwe chatsopano - Nkhani ya uthenga wabwino	51
6.4 - Chilengedwe chatsopano – Kubwezeretsedwa kwa zinthu zonse	54
7.1 - Kuyikambanso nkhani – Uthenga okhudza Ufumu	
7.2 - Kuyikambanso nkhani – Nkhani yokhudza kachisi	56
7.3 - Kuyikambanso nkhani – Nkhani yokhudza pangano	59
7.4 - Kuyikambanso nkhani – Aefenso munkhani yonse ya mu bayibulo	62
8.1 - Kupanga phunziro lanu lokhudza Mulungu – Nkhani yokhudza Sabata	64
8.2 - Kupanga phunziro lanu lokhudza Mulungu – Nkhani yokhudza ndalama	67
8.3 - Kuzama	68
8.4 - Kukozaanso chilichonse mokhudzana ndi nkhani	72

1.1 - Mawu Oyamba

Awa ndi maphunziro ofuna kukuzindikilitsani njira yomwe mungawerengere baibulo yotchedwa “Kuzindikiritsa za chiphunzitso cha m’bayibulo chokhudza Mulungu.” Cholinga cheni cheni cha maphunzirowa ndi kufuna kuphunzira momwe mungalimvere bwino bayibulo. Maphunzirowa kwenikweni ndi a anthu amene ali adindo mumpingo, makamaka kwa omwe ali ndi udindo ophunzitsa ena zokhudzana ndi bayibulo. Komabe tili nacho chikhulupililo chakuti zikhoza kukhara chothandiza kwa mkhilisitu aliyense amene akufuna kukula m’chikhulupililo chake ndi kuphunzira kuti angazigwiritse ntchito motani zomwe bayibulo likunena pamoyo wake .

Maphunzirowa akonzedwa kuti adzichitika pagulu ndicholinga chakuti anthu akhoza kutenga nawo gawo pa zokambirana zokhuza maphunzirowa, kuti athe kuphunzira kuchokera kwa ena pamene tikuwunguza bayibulo limodzi, komanso ndi wina amene akhoza kukuthandizirani ndi kuwonetsetsa kuti mukutha kumvetsetsa zambiri m’maphunzirowa.

Kodi mukuyembekeza kuti mukwanilitse zotani m’maphunzirowa?

“Ife ndife okhumbitsitsa kulalikira mokhulupilika ndi kuphunzitsa zokhudza malemba powatenga malembawo kukhala ulamulilo wathu oyamba ndi otsiriza.”

Amenewa ndi mawu amene mipingo yambiri komanso zipembedzo zambiri zingakondwere nawo, ndipo ambiri mwa iwo ali ndi mawu ofananila mu mpango wa mawu okamba za chikhulupililo chawo. Funso ndi lakuti, Kodi zimenezi zikutanthanji? Zimenezi zizikuchititsani kuti mulingalile zokhudza m’mene inu mumalimvera bayibulo komanso za m’mene mukuyenera kulimvera ndi kukhalila moyo wanu malingana ndi zimene bayibulo limanena.

‘Bayibulo ndi mawu a Mulungu’. Umu mkutheka ndi mmene limawonedwera bayibulo pakati pa akhilisitu ambiri ndipo palibe amene angathe kutsutsana ndi lingalilo limeneli. Komabe zimenezi sizimatithandiza kwenikweni makamaka tikayamba kumadzifunsa mafunso okhudzana ulamuliro wake komanso mmene tingazigwiritse ntchito.

‘Mudzichita zomwe likunena’. Umu ndi mmene amalimvera bayibulo munthu amene amaliwona bayibulolo kukhala buku la malamulo operekedwa ndi Mulungu amene tikuyenera kuwamvera. Izi zikhoza kuchititsa zinthu kusokonekera kamba kakuti mbali yayikulu ya bayibulo mulibe zokhuza malamulo ndipo mbali zomwe zikukamba za malamulowo zimawoneka kuti zikutsutsana. Mwachitsanzo, tili ndi malamulo omveka bwino okamba za zakudya zomwe tikuyenera kudya ndi zomwe sitiyenera kudya makamaka mu buku la Levitiko pamene Yesu akukamba zosiyana ndi izi mu buku la Maliko chaputala cha 7.

Kodi timakhoza bwanji kuzindikira malamulo amene akukamba za ife komanso malamulo amene akukamba za m’bado umene ukudza ?

‘Mukungoyenera kutsata chipangano chatsopano, chakale sichikugwiranso ntchito’.

Munthu uyunso amalitenga bayibulo kukhala buku la malamulo ndipo iye amakhala osangalala kukhala ndi chidwi ndi nkhani zokhudza Yesu mkumapita chitsogolo. Izinsu

Chisangalala cha Kumwamba

1999

...the thought of being great
and important made me feel that
I had no earthly father and no
mother, the last time, the only time

100

...the ...
...the ...
...the ...
...the ...
...the ...

[illegible][illegible]

The following are some of the most common types of...
The first type is...
The second type is...
The third type is...
The fourth type is...
The fifth type is...
The sixth type is...
The seventh type is...
The eighth type is...
The ninth type is...
The tenth type is...

...the ...
...the ...
...the ...

This is a close-up photograph of a single, blank page from a notebook. The paper is white and features faint horizontal ruling lines. The right edge of the page shows the dark binding of the book. The lighting is soft, highlighting the texture of the paper.

zikhocha kukhala zosokoneza chifukwa Yesu amkawonetsa kuti amkasamala kwambiri zokhudza chipangano chakale. Kodi tisiye kutsata ziphunzito zina zofunika monga malamulo khumi? Ngati tikuwatenga malamulowa kukhara ofunikira kodi zikutanthawuza kuti nafe tikuyenera kusunga sabata m'mene Ayuda amachitira?

'Timakhulupilira zomwe likunena'. Munthu otereyu amalitenga bayibulo kukhala buku la malonjezano operekedwa ndi Mulungu amene tikhoza kuwalandira kudzera mu kukhulupilira. Izinso zimasokoneza pamene muyesera kusankha kuti kodi ndi malamulo ati amene Mulungu amkapanga kwa anthu ena ake munthawi ina yake, komanso ndi malamulo ati amene wina aliyense akuyenera kuwatsata. Mwachitsanzo, Masalimo 91 ndi yokonedwa ndi akhilisitu ambiri akafuna kuti Mulungu awateteze ku choipa chilichonse. Kodi zimenzi zikutanthawuza kuti Yakobo (yemwe anphedwa pomudula mutu) komanso overa ambiri amene anafa kamba ka kukhulupilira analibe chikhulupiliro chokwanira kuti akhoza kupeza nawo lonjezanoli?

'Ndi vumbulutso la Mulungu ku dziko lapansi'. Munthu otereyu amaliwona bayibulo kukhara njira yodziwira mmene Mulungu alili. Posonkhanitsa china chilichonse chimene bayibulo limakamba mu zinthu za mtundu wina wake, tikhoza kuyamba kukhara ndi zikhulupiliro ndipo tikhoza kugwiritsa ntchito zikhulupiliro zimenezi kuti timumvetsetse Mulungu ndi kudziwa zomwe iye amafuna kuti ife tichite mu dziko lino, mwa njira ina zikhocha kukhara zosavuta kuwerenga buku lokamba za kachitidwe ka zikhulupiliro kusiyana ndi kusonkhanitsa ntchito yonse yofunika, kuti tikwanitse kusonkhanitsa nkhani zonse za mu bayibulo. Kodi mukuganiza kuti zimenezi ndi zimene Mulungu amafuna?

'Bayibulo ndi nkhani yomwe imakhara ikudzitambasula yomwe ife tikuyitanidwa kuti titenge nawo gawo'. zimenezi mosakayikira ndizo zikutchedwa kuti chiphunzitsa cha m'bayibulo chokhudza Mulungu. Zikhocha kutenga chithu china chake mu nkhani zomwe zakambidwa mmwambamo koma ndi zosiyana ndi chilichonse mwa zinthuzo. Njirayi imaliwona bayibulo kukhara nkhani imodzi yayikulu, yomwe mbali iliyonse imawonjezera mu kukwanilitsa kwa zonse. Mbali iliyonse ya bayibulo ikhoza kumasulilidwa moyenera mukayiwona mmalo ake mu nkhani yonse.

Maphunzirowa akhazikika kwambiri pa kumvetsetsa 'nkhani yayikuluyo' ndi kuphunzira kuwerenga ndi kumasulira malemba molingana ndi nkhaniyi.

Mafunso okambirana:

- 1) Kodi bayibulo limatanthawuzanji kwa inu?
- 2) Kodi lakuthandizani motani pamoyo wanu m'mbuyomu?

1.2 - Mphamvu ya nkhani

Ngakhare kuti tikhoza kusazizindikira zimenezi koma zowona zake ndi zakuti aliyense mwa ife akukhara mu nkhani pakadali pano. Zimenezi zimatchedwa mmene munthu amaliwonera dziko. Imeneyi ndi nkhani yomwe takula nayo yomwe imatithandizira kuti tikhare ndi tanthawuzo pa dziko.

Mafunso monga: [Kodi ndinachokera kuti? Kodi ndi chifukwa chani ndili pano?](#)
Amapanga msanamira za mmene ife timaliwonera dziko.

Mu chikhaliidwe cha mayiko a ku ulaya (kumadzulo), amawona kuti dzikoli linachitika kamba ka ngozi ya za mumlengalenga, kulibe namalenga, komanso tinangopezeka mwa mwayi. Choncho palibe tanthawuzo lenileni kapena cholinga m'moyo uno. Aliyense mwa ife amakhara mfumu mwa iye yekha, ndi kuyesetsa kuchita chilichonse chomwe tingapange ndi cholinga chakuti tisangalare tisanatsikire ku imfa, ichi m'chifukwa chake nkhani zambiri za ku mayiko a kumadzulo zimakhara zokhuza anthu opeza wachikondi weniweni kapena kukhara kalonga kapena kukhara moyo osangalala.

Mu chikhaliidwe cha ku Afilika ndi ku mayiko a kummawa amawona Mulungu kukhara olenga, koma gawo la makolo akale ndi limene limamanga nthenje kwambiri, zimenezi zimachititsa kuti pakhare ubwino wa kufunikira kwa mabanja ndi ma ubale, ndinayamba ndamufunsapo mzimayi wa mtundu wa Isikosa kuti, 'Kodi akuwona kuti mtundu wa anthu unachokera kuti, ndipo iye anandiwuza zokhuza kholo leni leni la anthu a mtundu wa Isikosa. Mzimayiyu amazindikira pogwiritsa ntchito mtundu wake ndipo kuti udindo wake wagona pakuti adzithandiza ndi kutumikira anthu a mtundu wake amene ali ochuluka komanso ma ubale ake.

Nkhani yomwe tikukhalamo ndi chinthu chimene chimatilimbikitsa mu zimene timachita, mmene timawuwonera moyo komanso zomwe timayembekeza. Posachedwapa ndinalankhula ndi munthu wachipembezo cha chisilamu iye amawona kuti chilichonse chokhudza moyo chagona mmanja mwa Allah zomwe zikutanthawuza kuti amakana kuchitapo kanthu potsata malamulo okhudzana ndi nthenda yofalikira ya COVID -19 coronavirus, samkavala chotchinga pakamwa kapenanso kukhala motalikana ndi wina pachifukwa chakuti ikakhara nthawi yokuti munthu amwalire palibe chilichonse chomwe angathe kuchita. Nkhani zathu zimakhara ndi gawo pa miyoyo yathu.

Ichi ndi chimodzi mwa zinsinsi za mphamvu ya bayibulo. Bayibulotu ndi nkhani yomwe ifeyo tikuyitanidwa kuti titenge nawo gawo. Nkhaniyi ikulowera kwinakwake, mwanjira ina ili ndi mapeto a ulemelero oposa ndipo aliyense mwa ife ali ndi kuthekera kotenga nawo gawo.

Ntchito yathu monga olalikira ndi ophunzitsa zinthu zokhudza bayibulo ndi yakuti tisinthe nkhani ya munthu yokhudza mawonedwe ake a dziko ndi kuyikiza mwa iye nkhani ya bayibulo. Mwawonatu, ngati ndidzitenga ndekha kukhara mkhisisitu koma mkumapitiliza kukhara ndi malingaliro a kaganizidwe kanga kokhudza mawonedwe a dziko a anthu a mayiko a kumadzulo, palibe chenicheni chomwe chimasintha pamoyo wanga. Ndikhoza kumapita ku tchalichi, kukhara ndi amzanga atsopano komabe zinthu zenizeni zimene ndimazikhulupilira pa moyo wanga zikadali zomwe zija. Ndikukharabe ndi moyo odzikonda, wadyera, ndi wakufunitsitsa ma udindo. Ndi pokha pokha ife tikasintha kawonedwe kathu ka zinthu padziko mpamene moyo wathu umasintha zenizeni.

Pamene tikuwonjezera chidziwitso chathu ndi kudziyikiza mu nkhani yokhudza bayibulo mpamene umapezeka kuti ukukhara mmapenyedwe a umunthu weni weni, monga umo anatilengera Mulungu kuti tidzikhalira. Pamene Pawulo amawalimbikitsa a Efenso kuti

adzikhara moyo oyenera monga mwa mayitanidwe amene analandira (Aefenso 4:1) iye anali akusonkhanitsa pamodzi nkhani yonse ya Mulungu ndi kuwawonetsera kuti ali ndi gawo mu nkhanimo.

Mafunso okambirana:

- 1) Kodi ndi nkhani yanji ya mmene munthu amaliwonera dziko yomwe imamanga nthenje mchikhalidwe chanu?
- 2) Kodi nkhanayi yakhudza bwanji moyo wanu?
- 3) Kodi ndi kusiyana kwanji komwe munthu amakhala nako akasintha kukhara mkhristu mchikhalidwe chanumo?

1.3 - Zichitochito za mu bayibulo

Ndikofunika kuti tipeze chidziwitso choyenera cha zochitika zonse za baibulo tisanayambe kuyang'ana za nkhani yonse. Gawo ili liyesetsa kuyikiza mfundo zofunikira za nkhani za mu bayibulo mwa dongosolo linalake.

Tiyamba ndi “Pachiyambi” pamene tikudziwitsidwa za chilengedwe. Pamene iye analamula, dongosolo linachokera mu chisokonezo, kuwala kunachokera mu mdima, mtunda unachokera mu nyanja komanso moyo unachokera kunthaka. Zomera, zinyama kenako Adamu ndi Eva anabwera komaliza kwake. Iwowa anapatsidwa munda wabwino kuti awusamalire. Munda umene umayenera kuwapatsa zosowa zawo zonse pamene iwo amasangalatsana pamaso pa Mulungu amene anali nawo.

Chinthu chokhacho chimene Mulungu anawaletsa ndicho chakuti samayenera kudya chipatso chochokera mu mtengo wa kudziwitsa zabwino ndi zoyipa. Komabe iwo anakumana ndi cholengedwa chomwe chinali ndi mawonekedwe a njoka chomwe chinawanyengelerana kuti adye chipatso cha mtengowo, ndipo kumuwukira Mulungu kwawo kunayambika. Anayenera kuchoka mmundamo ndipo moyo siwunalinso chimodzimodzi. Ndithudi pamene mtundu wa anthu umachulukirachulukira udaninso ndi ziwawa zinachulukirachulukiranso.

Mulungu anakhumudwa ndi zichitochito za anthu, ndi kuwukira konse komanso kukhetsa mwazi. Pamene analephera kupilira nazo anatumiza madzi osefukira kuti akokole mtundu onse wa anthu ndipo anangosiyapo Nowa ndi banja lake komanso anasiyanso zinyama zamoyo mu chingalawamo.

Komabe kuwukira, kuponderezana ndi kukhetsa mwazi kunapitilira mpaka pamene Mulungu anawamwaza anthu onse a padziko lapansi powapatsa zilankhulo zosiyanasiyana ndi kuwapangitsa kuti asokonezane okhaokha ku Babelo.

Apa ndi pomwe tikukumana ndi Abulamu, yemwe anali wa pa ulendo, yemwe kwawo kwenikweni kunali ku Babelo koma anayitanidwa ndi Mulungu kuti apite kumalo atsopano ku dziko la Kenani. Mulungu ndipo anamusintha iye dzina mkukhara Abulahamu, “Tate wa

mitundu ya anthu,” ndipo anamulonjeza iye kuti kudzera mwa zidzukuluzake anthu onse a padziko lapansi adzadziwa mdalitso wa Mulungu. Abulahamu ndi tate wa banja latsopano lomwe lanyamula dalitso la Mulungu.

Pakupita kwa nthawi Abulahamu ndi Sara anabala mwana wamamuna dzina lake Isake, amene pakupita kwa nthawi anabereka mapasa; Yakobo ndi Esawu. Yakobo anabara ana khumi ndi awiri mothandizidwa ndi azikazi ake awiri, ndi adzakazi awirinso ndipo Mulungu anamusintha iye dzina mkukhara Isilayeli.

Ana khumi ndi mmodzi anatopa ndi kudzikudza kwa Yosefe ndi kukondera kwa Yakobo komwe amkamukondera iye ndipo mapeto ake anamugulitsa monga kapolo ndipo ananamizira kuti iye waphedwa ndi chilombo cha mthengo. Yosefe anakafika ku Ijipiti komwe anadziwa zonse: kukonderedwa ndi tsoka lomwe, anakwanilitsa zazikulu m’nyumba ya Potifara chisanamuchitikire chosalungama chomunamizira ndi kumuponya mu ndende. Mulungu anamupulumutsa iye ndi kumpanga kukhara nduna yayikulu mu dziko lonse la Ijipiti, kumene anali oyang’anira kutolera ndi kugawa zakudya pambuyo pakuwonetsedwa ndi Mulungu kuti kudzakhara zaka zisanu ndi ziwiri za masika komanso zaka zisanu ndi ziwiri za njala. Njalayi inapangitsa kuti abale ake afike ku Ijipiti ndi cholinga chofuna kupeza zakudya zimene zinapangitsa kuti ayanjanenso ndi Yosefe komanso kuti akakhazikike ku Ijipiti komwe banja lawo linakula mkukhara mtundu wa anthu.

Zaka 40 zinadutsa, ndipo tikuwona kuti kuponderezana komanso chiwawa chinabwelera. Aisilayeli anasanduka akapolo ndipo anakweza mawu kumulilira Mulungu chifukwa cha kuzunzidwa kwawo. Falawo chifukwa cha kuwawopa Aisilayeli amene anali kuchulukirachulukira analamura kuti ana onse aamuna a Ahebeli aphedwe. Mose anabadwa mu limodzi mwa mabanja ovutidwawa koma sanaphedwe pakuti anapulumutsidwa ndi mwana wamkazi weniweni wa Falawo amene anampeza Mose mu basikete ikuyandama pamadzi.

Mose anakulira m’nyumba ya chifumu koma ali ndi zaka 40 anapha munthu wa ku Ijipiti amene amazunza m’Isilayeli ndipo anathawira kuchipululu komwe anakakhara oweta ziweto kwa zaka zina 40. Komaliza kwakwe Mulungu anamuyitana kuti akapulumutse Aisilayeli ku mazunzo awo, mothandizidwa ndi Aloni yemwe anali mkulu wake. Iye anapita kwa Falawo ndipo anawonetsera zozizwa khumi kuti zikhare monga chigamulo, ndipo anamalizira ndi imfa ya ana onse oyamba kubadwa m’banja lililonse. Aisilayeli anapulumutsidwa ndi mwazi wa nkhosa ya paska yomwe banja lililonse linagwiritsa ntchito kuti liteteze khomo lake. Iwo anapulumuka ku Ijipiti ndipo anadutsa panyanja yofiira modabwitsa kwambiri pomwe aja amawapondereza aja anathera pompo pomizidwa ndi madzi.

Aisilayeli anasonkhana pa phiri la Sinayi komwe Mulungu anapanga nawo pangano ndipo iwo anavomereza kuti amutsata iye ni mtima wawo onse. Komabe panganoli lisanakhazikitsidwe Aisilayeli anayamba kuwukira, kulambira mwana wang’ombe wagolide pamodzi. Izi zinapangitsa kuti kukhare zaka 40 zosawutsa ndi kuyendayenda m’chipululu m’mene Mulungu anawalumbilira kuti palibe mmodzi mwa anthu a m’badwo umenewu amene adzalowe kumalo amene Mulungu anawalonjeza, izi zinachitika chifukwa chakusowa chikhulupiliro kwawo. Yoswa ndi Kalebe okha ndiwo anamukhulupilira Mulungu ndipo ndi amene anatsogolera m’badwo winawo kukalowa mu dziko la malonjezano.



10 Kuzindikiritsa za chiphunzitso cha m'bayibulo chokhudza mulungu

Kutsatira kwa utsogoleri wa Yoswa owatsogolera Aisilayeli kukalowa mu dzikolo analipo masiku amene Aisilayeli amkavutidwa ndi mayiko ozungulira ndipo analilira kwa Mulungu. Mulungu anawawutsira atsogoleri osiyanasiyana pakati pawo amene amawabweretsera ufulu koma kwa thawi yochepa komabe kawirikawiri Aisilayeli anayamba kulambira mafano ndipo kuvutidwa kuja kumkayambiranso. Kumapeto kwa zonse anthu anakweza mawu kwa Yehova kufuna mfumu yakuti idziwalamulira ndi choliga chofuna kufanana ndi mitundu ya anthu yomwe yawazungulira.

Mfumu yoyamba ya Isilayeli inakhara yodzikonda komanso ya mantha, chomcho Mulungu anasankha Davide amene amatchedwa kuti munthu wapamtima pa Mulungu. Lonjezo la Mulungu kwa Davide linali lakuti ufumu wake udzakhara mpaka kalekale, ngakhare kuti anali ndi zofooka. Ulamuliro wa Davide unabweretsa mtendere ndi kuyenda bwino kwa zinthu mu Isilayeli monse zimene anazipeza Solomo amene anali mwana wake. Solomo amkadziwika chifukwa cha mzeru zake ndi ulamuliro wabwino mpaka panthawi imene adzikazi ake a mitundu ina anamusokoneza mtima ndi kumuchotsa pamaso pa Mulungu.

Rehobowamu amene anali mwana wa Solomo anayamba kuwazunza anthu ndipo mapeto ake ufumuwo unagawanika, mafuko khumi anakhara kumpoto kwa Isilayeli ndipo mafuko awiri anakhara kumwera komwe tsopano kunayamba kuchedwa kuti Isilayeli ndipo kwinko kumkatchulidwa kuti Yuda. Iyi ndi nthawi yomwe Mulungu anawadzutsira iwo aneneri kuti awabweze anthuwa abwelere m'chipangano chimene Mulungu anapangana nawo.

Komabe, mafuko a kumpoto anapitiliza kulambila mafano awo ndipo anatengedwa kupita ku ukapolo ndi kuwonongedwa ndi ufumu wa Aasiliya. Mafuko a kumpoto amkatha kubwelera kwa Mulungu komabe kupembedza mafano ndi kuponderezana sizimkawatalikira ndipo nawo anatengwedwa kupita ku ukapolo ndi anthu a ku Babulo kwa zaka 70.

Pamapeto pa zaka 70 zomwe iwo anali ku ukapolo, Aisilayeli ena anabwelera ndipo anamanganso linga la Yelusalemu. Komabe munthawi yake yomweyi kupembedza mafano ndi kupondereza osawuka kumkapitilira kwinko akudikira masomphenya akulu a aneneri kuti akwanilitsidwe.

Zaka 400 zotsatira, pambuyo pa chiyembekezo, kuyembekeza, kugonja ndi kukhumudwa, liwu latsopano linamveka. "Ufumu wa Mulugu wafika." Amkatero Yesu uku akuchiritisa odwara, kumasula andede ndi kuwakwiyitsa atsogoleri a chipembedzo pokhululukira machimo komanso kusakanikirana ndi anthu a kunja, ochimwa ndi owukira. Ngakhare kuti iye anabwera ndi kutchedwa kuti Rabi (mphunzitsi) uthenga wake unali osangalatsa komanso okhumudwitsa, wa chikondi komanso oopsya ndipo a udindo anawona kuti kunali koyenera kuthana naye.

Zitatha zaka zitatu akutumikira mowonekera, Yesu anagwidwa, anayimbidwa mulandu ndipo anapezeka olakwa pamlandu onyoza Mulungu ndipo anaperekedwa mmanja mwa adindo a Chiloma kuti amupachike pamtanda. Amzake amene amakhara nawo chifupi anamusiya ndipo anaperekedwa ku imfa yopweteka kwambiri. Pa tsiku lachitatu Yesu anawuka ku akufa ndipo anawonekera kwa ophunzira ake mawulendo angapo kuwakonzekeretsa iwo ku Pentekosite, nthawi yomwe Mzimu Oyera anapelekedwa kwa iwo ndipo anayamba utumiki opanga ophunzira a Yesu.

Ntchito yawo inali yopanga ophunzira a Yesu khristu mu mtundu uliwonse wa anthu padziko lapasi mpaka panthawi yomwe Yesu adzabwerele kuti pamapeto ake adzakonze zinthu zonse zimene zinawonongedwa ndi kusokonekera ndi uchimo, ndikupanga malo atsopano amene kumwamba ndi dziko lapansi zidzalumikizane ndipo aliyense adzakhare odzipereka ku ulamuliro wake kwatunthu.

Imeneyi ndiye nkhani yakhudza bayibulo koma mwachidule. Inde pali zambiri zokhudza bayibulo kuposa zimenezi, pali mabuku asanu oyambilira amene amatchedwa kuti Pentatuchi (mabuku a chilamulo) amene akukamba za malamulo a Mulungu okhudza Aisilayeli komanso nkhani yokhudza kulowa kwawo mu dziko la malonjezano.

Pamodzi ndi mabuku a mbiri, tiliso ndi mabuku a ndakatulo ndi luntha, komanso mabuku ambiri a uneneri amene akukamba za malo osiyanasiyana ndi nthawi zosiyana za zinthu zochitika.

Zoyenera kuchita:

Zochita zanu mu sabata imeneyi ndizoti mulembe mndandanda wa zinthu monga mmene zalembedwera mmwambamu, ndipo muyike mumzera buku limodzilimodzi la m'bayibulo pamene mukuwona kuti ndipomwe akuyenera kukhara malingana ndi mlondola wa nthawi. Izi zikuthandizani kuti mukhale ndi chithunzithunzi cha chifukwa chimene buku lililonse mu bayibulomu linalembedwera, kuti likukamba za ndani komanso ndi chifukwa chanji uthenga wake uli ofunikira.

(thandizo – ngakhare kuti tchitoyi ikuwoneka yolemetsa koma pali zolembedwa zambiri zimene athu ena anachita kale zomwe zingathe kupezeka mosavuta pa makina a intaneti).

1.4 - Zitsunzo m'magawo asanu

Kufikira pano tasonkhanitsa pamodzi zina mwa zinthu zofunikira kwambiri za bayibulo, ndi kuganizira za pamene buku lililonse likuyenera kukhara pa mndandanda wa nthawi. Tikangokwanitsa zimenezi zikhara zotheka kuti tidzitha kudziwona kuti tikulidziwa bayibulo ndi uthenga wake. Palitu chiwopsyezo apa. Ifetu tikhoza kukhara ndi chidziwitso cha zochitika za mu bayibulo koma mkusakhara ndi chidziwitso cha zomwe mndandanda wa nkhanizi ukukamba. Tikhoza kumvetsetsa zomwe zinachitika koma mkusawuzindikira uthengawo.

Kodi Yesu anapanga chani pambuyo pa kuwuka kwake ku akufa, asanakwere kupita kumwamba?

Luka 24 ikukamba za kuwonekera kuwiri kumene Yesu anachita kwa ophunzira ake pambuyo pa kuwuka kwake ku akufa.

Vesi la 25 mpaka la 27 komanso la 44 mpaka la 45 akuwonetsa kuti Yesu anali ndi cholinga chodziwikiratu. Awatu anali amuna a Chiyuda amene anakula akuphunzitsidwa malemba ndipo amkadziziwa khanizi m'mitima mwawo, komano Yesu apa amkawathandizira kuzimvetsetsa. "Chilichonse chomwe chinalembedwa chokhudza ine m'mabuku a Mose, Aneneli komanso m'masalimo chikuyenera kukwanilitsidwa. **Kenako iye anawatsegula maso ndi cholinga chakuti athe kumvetsetsa Malemba"**

Mu zichitochitozi, Luka akufotokoza kuti Yesu anawonekera kwa iwo mu nyengo yokwana masiku 40 ndipo amkalankhula nawo zokhudza ufumu wa Mulungu.


Yesu amkayifotokozanso khani ya Isilayeli komano iye mwini mkukhara mwini nkhanzi, iye amkawathandizira kaganizidwe kawo zokhudza malemba m'maphunzira a bayibulo kwa masiku 40, Petulo pamene anayimilira kuti alankhule ndi anthu pa tsiku la Pentekosite, ulaliki wake umkachokera pa zinthu zimene wakhara akumva kuchokera kwa Yesu.

Yesu ndiye amene wakhara mwini nkhanzi nthawi yonse ngakhale zinali zobisika kwa anthu ambiri. Ophunzira ake anayamba kumvetsetsa kuti Yesu anali okwanilitsa chilichonse chimene chipangano chakale (malemba awo) chakhara chikulonjeza. Malembawa anali chithunzithunzi cha chowonadi chimene chawonekerano mwa Yesu (Akolose 2:17) . choncho kuti tichimvetsetse chipangano chakale bwinobwino, tikuyenera kumachiwerenga tikuponya maso pasogolo kwa Yesu komanso ndikumvetsetsa kuti ku zowona zenizeni komwe chikutilozerako kumawonekera pokhapokha kudzera mu ntchito yomwe Yesu anachita.

Tikamalimvetsera bayibulo lonse pamodzi, tikhoza kukwanitsa kufotokoza mwachidule magawo ake osiyanasiyana kumvetsetsa kuti mbali iliyonse ndi yofunikira mu nkhanimu koma imatanthawuzilidwa bwino ikayikidwa bwinolomwe pamalo oyenera mu nkhanzi yonse.

Pofuna kugwira malemba a mu chipangano Chatsopano ophunzira wina dzina lake NT Wright ananena kuti chili ngati chitsunzo cha magawo asanu. Sewero limakhara kuti ndi nkhani yomwe ikuyenera kukachitidwa monga chitsunzo chokachita pamaso pa anthu, limagawidwa mu magawo osiyanasiyana kapena tinene kuti magawo a zitsunzo. Gawo lililonse limakhara lolumikizana ndi magawo ena onse mu nkhani kukhara gawo la nkhani yonse. Koma gawo lina lililonse limakhara ndi kachitidwe kakekake komanso cholinga chake. Ngati munthu amene akutenga gawo mu chochitika cha mu gawo lachisanu la sewelolo akuyamba kuchita zinthu monga za zochitika za mugawo lachiwiri zikhoza kupangitsa kuti sewerolo likhale losokoneza kwambiri. Gawo lililonse likuyenera kuwonedwa ndi kumvetsetsedwa moyang'anira malo ake amene likupezeka mu nkhanimo.

NT Wright anakamba mwachidule magawo a seweroli motere;



Kotero ife tikuzipeza tokha mu chochitika chachisanu. Tikhoza kuwerenga bayibulo kuchokera mu buku la Machitidwe a atumwi mkumapita kutsogolo ndi kumadziwona kuti ndizofunikira kwa ife kuti tidzidziwe komabe zomwe tikuwerega mu zochitika za m'mbuyo zikuyenera kutithandizira kuwona m'mene nkhaniyo ikutambasukira koma pokhapokha tikamayimasulira kudzera mwa Yesu, mu njira imeneyi tikhoza kuyamba kusintha mmene tingawerengere ndi kumvera gawo lalikulu la bayibulo.

Mwachitsanzo, tiyeni tiwone nkhani yokhudza Davide ndi Goliati, alaliki ambiri amakonda kufotokoza nkhani ya munthu osadziwika akuyima pamaso pa chiphona ndi kuchigonjetsa mosatengera zopinga. Zimenezi zimakolezera mphamvu mkati mwathu mwakuti timafuna titadzambatuka kuti tikagonjete, koma kodi Yesu akhoza kuyikamba motani nkhani imeneyi? Bwanji zikanakhara kuti Yesuyo ndiye gwelo komanso chiphona cha nkhaniyi? Tsopano tikutha kumvetsa kuti Yesu ovulazidwa komanso ali pachiwopyezo akulimbana ndi mphamvu zowopsya za adani a Mulungu. Palibe aliyense amene akanatha kulimbana nazo mphamvuzo, koma mosayang'anira zopinga, Yesu analimbana ndi mphamvu za uchimo, imfa komanso za oyipayo ndipo anazigonjetsa kotheratu, ndi kuwasiyila abale ake kuti ayikize chipambanocho padziko lonse lapansi.

Zitsanzo zina zowonjezera

Nkhani	Kutanthawuzira nkhaniyo ngati ya payokha	Kutanthawuzira nkhaniyo ndikumuyika Yesu kukhara namandwa wake
Abulahamu ndi Isake(Gen 22)	Abulahamu anamukhulupilira Mulungu ndipo modzipereka anapereka mwana wake. Tikuyenera kukhara monga Abulahamu ndi kukhara moyo odzipereka mwachikhulupiliro.	Tikumumvetsetsa Mulungu Atate, akupereka mwana wake yekhayo pa phiri la Moliya, malo amene anatchedwa Yelusalemu. Iye anapereka nkhoa ya nsembe m'malo mwa Isake, ndi cholinga chakuti Isake akhare ndi moyo.
Mose ndi Ekisodo (Ekisodo 11)	Mose anayitanira pa Mulungu kuti awamasule anthu ake, ndipo Mulungu anamuyankha iye ndi chiweruzo kwa anthu osalungama. Mulungu adzatithandiza kulimbana ndi anthu amene akulimbana nafe.	Yesu, nkhoa ya Paska ya Mulungu anaphedwa ndipo mwazi wake unawawombola anthu ku ziphinjo za uchimo, imfa ndi oyipayo.
Yona ndi chinsomba (Yona 2)	Yona akulandira chilango chifukwa cha kusamvera, koma Mulungu naye akumuwonetsera chifundo populumutsa moyo wake kudzera mu nsomba, kudzera mu zimenezi tidziwa kuti Mulungu adzatiweruza chifukwa cha tchimo lathu komano tikuyembekezeranso chifundo chochokera kwa iye.	Msembe ya Yesu inali ya anthu ambiri ochokera ku mitundu yosiyanasiyana. Iye anasawutsidwa ndipo anabisika mu imfa koma Mulungu anamuwukitsa iye ku imfa pa tsiku lachitatu zomwe zikuwonetsera mphamvu komanso ulamuliro wake.
Davide ndi Mefibosheti (2 Sam 9)	Davide akumchitira chifundo munthu olumala, ndie nafenso tiyenera kuchitira chifundo iwo amene ali osowa.	?

**Tayeserani kumasulira nkhani ya mubokosi lomalizalo pa inu nokha.
Kodi mu nkhanimu Yesu akupezeka pati?**

Zimene takhara tikuchita pamenepa mkuyesera kutanthawuzira bayibulo mu njira imene Yesu anakatha kulilongosolera kwa ophunzira ake. Zimenezi ndi zomwe mu nthawi ya kumayambiliro kwa chikhilistu zimatchedwa kuti zikhulupiliro za atomwi. Iyi ndi mbali yofunikira kwambiri pomasulira bayibulo bwino. Titenga sabata tikuwona magawo a bayibulo kuti tiwone mmene tingawerengere ndi kumvetsetsa poyang'ana chithunzi cha nkani yayikulu, Yesu mkukhara mwini nkhani.

Funso lokambirana: Tawerengani nkhani ya Yosefe mu buku la Genesis 37-50

1) Kodi munkhanimo Yesu mukumuwona pati?

2.1 - Kulengedwa

Kuchokera m'amasiku a Charles Darwin (munthu wa za sayansi wa mu zaka za mma 1900 amene amkatsutsana ndi njira ya kasinthidwe ka zinthu za moyo), mpingo komanso dziko lapansi, analimbana kwambiri Genesis chaputa 1. Anthu okhulupilira kawirikawiri akhara akukodwa mu mtsutsano umenewu polimbana ndi mzeru za dziko lapansi zokhudza kawonedwe ka kasinthidwe ka zamoyo zikuluzikulu. Zikhoza kumawoneka ngati tikulimbirana chilungamo cha umboni wa Mulungu kapena kufuna kudziwa ngati bayibulo lili loona. Chakhara chizolowezi kwa akhristu ena mwakuti tinasiya kuliwerenga mwa mtundu wina uliwonse. Mopanda vuto timasiyana nako kudziwa a kukongola, ulemero ndi kuphunzira zokhudza Mulungu zimene gawo limeneli la malemba likhoza kutiphunzitsa. M'mene olembayo amkafotokoza zokhudza chilengedwe cha zinthu analibe malingaliro okhudza kaganizidwe ka anthu amasiku ano a za sayansi. kunena zoon, iye anatilemba ife nyimbo kapena ndakatulo kufuna kuti atizindikiritse zokhudza Mulungu, mlengi wa zonse komanso kuti tithe kuzindikira zomwe zatizungulira komanso malo athu monga anthu mu chilengedwe cha Mulungu, izi ndi zomwe zikupanga poyambira pa nkhanu yathu, komwe ife tinachokera komanso chifukwa chomwe ife tikupezekera. Chaputalacho chimatipatsa mayakho ku mafunso ofunikira kwambiri a moyo uno.

Tatiyeni tiwone zimene chaputala choyambachi chingatiphunzitse.

1) Chilengedwe chabwino cha Mulungu

Kachitidwe kake kayikidwa m'malo – madzulo ndi m'mawa, madzulo ndi m'mawa. Kenako kolasi yake “ndipo Mulungu anawona kuti zinali bwino. Bwerezaninso “zinali bwino,” kamodzi komaliza “zinali bwino kwambiri”. Pokhara kwa Mulunguyo, wopanda banga, wamphamvu zonse, mlengi wa zonse pochayang'ana chilengedwe chake mwanthunthu ndi kupeleka chigamulo chake kuti “zii bwino” ndi zinthu zopatsa chidwi. Iye amakondwera ndi chilengedwe chake, amachikonda ndipo ndi cha mtengo wapatali kwa iye. Ndipo izi zimatiwuzza zambiri zokhudza iye, zimatiwuzza zambiri zokhudza iye, ubwino osawonekera wa Mulungu akuwonekera poyera. Za kumwamba zimawonetsera ulemero wa Mulungu. Kumitambo nthawi ya usiku, nkhalango, madzi okugwa kuchokera pamwamba m'mapiri, chigwa cha m'chipululu; zonsezi zimatiwonetsera kenakake kokhudza kukongola kwake mgwirizano wake, dongosolo lake, mphamvu zake, kalongosoledwe kake ka zinthu, mzeru yake. Zonse m'mene iye anazilengera mu dongoolo lake ndi zabwino.

Ena anaphunzitsidwapo kuti dongosolo la kalengedweli ndi loyipa, mwakuti cholinga chathu ngati akhristu ndichakuti tidzachoke mu thupi lathuli ndi dziko lathuli ndi kutengedwa mkupititsidwa mu thupi losakhudzikalo kumka mu miyamba ya uzimu pamene dzikoli likudziwononga lokha ndi kulowa mchiwonongeko kwathunthu kudzera mu chigamulo cha Mulungu. Magulu atunthu anadzipatula kudzikolo

pokhudzidwa ndi chivundi cha dziko lapansi ndipo ayembekeza mkwatulo kuti tonsefe tidzatengedwe. Ena awupanga uthenga wabwino wa Mulungu kukhara okhudza kuchoka kudziko lino mkupita kukakhara kwa muyaya kumwamba tikadzafa. Izi zakuti dziko la uzimu ndi labwino koma dziko tili lino ndi loyipa zinadza ndi munthu wina ophunzira wa Chigiliki dzina lake Plato osati kuti ndi zochokera mu bayibulo.

Tikuyenera kulora kuti chidziwitso cha chilengedwe chabwino cha Mulungu chikhale umodzi mwa mwala wa maziko mu nkhani za mu bayibulo. Iye amalikonda dziko lapansi, chilengedwe chake. Iye amakonda zimene anazilenga, amasangalala nazo. Zimenzi zikutanthawuza ndi ife tomwe. Iye ndife ntchito za manja ake, chinthu chopambanira. Izi zikutanthawuzanso dziko lomwe tili lino, ife tikhoza kusangalala ndi zomwe Mulungu anazilenga, tiyeni tilore kuti chilichonse chitiwuze zambiri zokhudza iye, ndi cholinga chakuti tikhare gawo limodzi la chilengedwe chimene chimampatsa iye mayamiko.

Kamvedwe ka zinthu kotereka kamadzadza dziko lonse, pamene chikondi cha Mulungu ndi chisangalalo chake pa zomwe anazilenga zili zinthu zolimbikitsa ku ntchito zake zachipulumutso. Iye samangofuna kupulumutsa kagulu kosankhika ka anthu ayi a koma pulani yake ndi kubwezeretsa chilengedwe chonse m'malommwake kwa iye mwini kuphatikizapo mtundu wa anthu.

2) Dongosolo kuchokera ku chisokonezo

Tiyambira ndi chochitika chokhudza mdima ndi madzi owinduka. Mawuwa mu Chihebeli amatchuidwa kuti, “Tohu wa bohu,” zomwe zikutanthawuza kuti, “Opanda mawonedwe komanso opanda kanthu.” Aka ndi kawonedwe ka nthawi zakale chilengedwe chisanadze, mdima komanso chisokonezo.

Kenako Mulungu anayankhula, ndipo mawu ake ali ndi mphamvu. Anatenga masiku atatu akupanga zinthu kudzera mu liwu lake lamphamvu, kulekanitsa kuwala kuchokera mumdima, kumwamba kuchokera madzi amene ali pasi pano komanso mtunda kuchokera m'nyanja. Uyutu ndi Mulungu kubweretsa dongosolo kuchokera ku chisokonezo ndi cholinga chakuti moyo upite chitsogolo. Kenako zinamutengeranso masiku ena atatu akulidzadza dziko lake. Dzuwa, mwezi ndi nyenyezi, nsomba ndi mbalame, zamoyo za padziko ndi anthu. Tsiku ndi tsiku iye akuphwanya “tohu wa bohu” opanda mawonekedwe komanso opanda kanthu, ndipo iye anapanga ndi kulidzadza dziko lake mpaka pamene anayang'anira zonse zimene wazilekanitsa ndipo anaziwona zitadzazidwa komanso zikuchita kusangalatsa bwino, ndipo anati, “zili bwino kwambiri.”

Nthawi zonse pamene Mulungu akutakataka mu dzikoli, timawona dongosolo likuchitika kuchoka mu chisokonezo ndi cholinga chakuti moyo uchite bwino. Nthawi zonse Mulungu akaleka kutakataka timawona kuti chisokonezo chimayamba kulamulira ndipo dziko lapansi limayamba kufanana ndi ena mwa mawonekedwe ake panthawi imene linali lisanalengedwe, mwachitsanzo m'mene zinalili ndi Nowa ndi madzi osefukira kapena Mose ndi zigamulo khumi zija.

3) Mpumulo omaliza

Atatha masiku 6 pakuyikiza dongosolo ndi kulidzadza dziko, akulowa m'chilengedwe kuti apume ndi kulamula munga mfumu, kulowa mu chipinda cha mpando wake wachifumu. Ilili ndi tsiku lokhalo limene lilibe madzulo ndi m'mawa, mkutheka kuti tsiku lachisanu ndi chimodzi silimayenera kutha. Ichi ndi chithunzi cha cholinga chachikulu cha Mulungu pa chilengedwe chake, ndi kuti munthu akondwere ndi zonse zimene Mulungu anazilenga ndipo iye mwini mkukhara mwini zonse, nasangalala nawo. Mtumwi Yohane zaka zochulukira zitapita anawona masomphenya a mzinda opanda kachisi, chifukwa Mulungu ndi Yesu ali mu kachisi wake ndipo kulibenso dzuwa kapena mwezi, kulibe masana kapena usiku, kopanda m'mawa kapena madzulo, ndipo mafumu a dziko akubwera nawo ulemelero wawo kwa ilo. (Chivumbulutso 21 ndi 22) zomwe zikutanthawuza kuti chilengedwe chidzakhalidwa mwatunthu, Yesu ali karonga wa zonse, ndipo izi sizidzatha.

Funso lokabirana: kodi mukuphunzirapo chani pamene mukuwerenga nkhani yokhudza kulengedwa kwa zinthu mu Genesis 1?

2.2 – Kulengedwa kwa munthu m'chifaniziro chake

Tawona mmene Genesis 1 ikutiphunzitsira zokhudza Mulungu, zokhudza chilengedwe chake komanso zokhudza malo athu munga mtundu wa anthu mu chilengedwe chake. Zonse zitatha kulengedwa, chochitika chomaliza cha chilengedwe chake chinali kupanga anthu “m'chifaniziro chake.” Izi zikupangitsa mtundu wa anthu kukhara osiyana ndi chilengedwe chonse, ife ndi zolengedwa zokhazo zomwe zinalengedwa mu chifaniziro chake.

Ndikoyenera kufufuza zomwe zimenezi zikutanthawuza.

1) Munda wangati kachisi

Zifanifani ndi mafano

M'dziko lakale, m'mene kunali akachisi ambiri amene amamangira milungu yosiyanasiyana, chinthu chomaliza chimene chimayenera kuchitika pomaliza kumangako chinali kuyika pamalo pake chifanifani cha mtundu wa mulungu wake. Mawu okuti chifanifani ndi omwewo amane amatanthawuzilidwanso kuti “fano” mu mabayibulo athu. Chimatanthawuza kuti ndi choyimira mtundu umenewo wa mulungu. Tikachiyang'ana chimenecho timatha kuwona chithunzithunzi cha mmene mulungu wa mtundu umenewo amawonekera. Mwachitsanzo, mu Chihindu m'modzi mwa milungu yawo amatchedwa Ganeshi. Iyeyu ndi uja amawonetseredwa m'chifanifani cha mutu wa njovu. Chimodzi mwa zichitochito zake mkuchotsa zopinga, ichi m'chifukwa chake chifanifani chake chili ndi njovu.



Kuzindikiritsa za chiphunzitso cha m'bayibulo chokhudza mulungu 19

Chiletso chopanga chilichonse pofananiza ndi Mulungu

Tsopano Mulungu yemwe ali mu bayibulo anakaniza ndithu chifanifani chilichonse chimene chili chosedmedwa chomufanizira iye. Chifukwa chani? Chifukwa iye anali atadzipangira kale chifanifani chake, sanagwiritse ntchito mtengo kapena myala koma pamene analenga anthu m'chifaniziro chake. Ifeyo ndiye chifanifani chake, tikuyenera kuyimira Mulungu mu kachisi wake. Chokhumba cha Mulungu chinali chakuti anthu achulukane ndi kulidzadzazidzika dziko lapansi, ndipo tikamachita zimenezo, timakhara tikukuza kachisi ndi kuyimira Mulungu ku chilengedwe chonse.

Mtsinje ochokera mu kachisi

Kodi mudawona kuti mtsinje unatuluka mu Edeni ndi kugawikana kupanga mitsinje inayi? Ukutu kuli ngati kuyitanira kuti tituluke mu mmunda wa Edeni, tikayendere dziko ndi kubweretsa moyo ku dziko lotizungulira. Zaka zambiri zotsatira, mneneri Ezekiyeli akulira kamba ka kuwonongeka kwa kachisi ku Yelusalemu ndipo anawona masomphenya a kachisi watsopano ndi mtsinje otuluka mkati mwake. Ka khwawa kakang'ono poyamba, koma kanayendelera ndi kukulirakulira komanso nakhara ndi mphamvu, ndipo kulikonse kumene kamayendelerako kamapereka moyo ngakhare kumalo akufa, Nyanja ya mchere, kanabweretsanso moyo ku mawonekedwe abwino, kuchilengedwe, ndi mitengo yomera m'mbali mwake; Edeni anali akuyendelera ndi kukulirakulira.

Akachisi onse otsatira amawonetsera za Edeni

Iyi ndi nkhani yokhudza kachisi yemwe akuwoneka m'malemba. Kachisi ali pamalo amene kumwamba ndi dziko lapansi zimakumana, kumene miyamba ya uzimu ndi yadzikoli imakumana, kumene Mulungu ndi munthu akhoza kukumana. Edeni anali kachisi oyamba. Mulungu ndi anthu amkakhara mu ubwenzi osangalatsa, Chihema ndi kachisi zonse zinali ndi zokongoletsa zomwe zimawonetsera zikumbukiro za Edeni. Choyikapo nyali ndi nthambi zake zisanu ndi ziwiri, chokongoletsedwa ndi motuluka maluwa ndi duwa lophuka, zipilala za kachisi, zokongoletsedwa ndi pomegilaneti ndi nsonga ya duwa yowoneka ngati kakombwe. Zonsezi zimakamba za nthawi ya m'mbuyo pamene Mulungu amkakhara ndi munthu mogwirizana.

Edeni monga anagwiritsidwira ntchito ndi aneneri

Malemba amagwiritsa ntchito chithunzithunzi cha Edeni ameneyu pamene ananeri akuloseza za nthawi ya kubwezeretsedwa kwa anthu a Mulungu. Monganso ananenera Yesaya 35:1

“Chipululu ndi dziko lowuma lidzasangalala; mapululu adzakondwera ndi kuphukira. Ngati duwa la krokasi, lidzatseguka nachita masace; lidzakondwa koposa ndipo lidzafuwula ndi chisangalalo

Nkhani yokhudza mtendere ndi zinyama za kuthengo ikugwiritsidwanso. Kumbukirani Daniyele mu dzenje la mikango (Dan 6) komanso Yesu m'chipululu (Maliko 1:13)

Kachisi wamkuluyo

Chifanifani cha kachisi chikuwonekeranso mu Yelusalemu watsopano yemwe akuchita kutsika kuchokera kumwamba mu Chivumbulutso 21. Ndi wapaderadera chifukwa cha mawonekedwe ake, wampwamphwa lofanana kukula kwakwe mbali zonse, izitu zikutikumbutsa za chipinda choyeretsetsa, malo amene anali mu chihema komanso mu kachisi, amene anali oyeretsetsa amene Mulungu ndi munthu amakumana. Anali chipinda champwambwa chofanana mbali zonse, mamita 5× mamita 5× mamita 5 mu chihema muja. Mamita 10 × mamita 10 × mamita 10 mu kachisi muja ndipo mamita oposa 2 000, 000 × 2,000,000 × 2, 000, 000 mu chilengedwe chatsopano, tangoganizani kuyendetsa galimoto kuchokera ku Cape Town ndikukafika kutali kumalile a South Africa ndi dziko la Mozambique. Umenewo ndiye muyezo wa mu litali, mu lifupi ndi kutalika kwa chilengedwe chatsopano! Kachisi akukulirakulirabe, pakharekhare Mulungu adzalidzadzaza dziko lonse lapansi, miyamba ndi dziko lonse; zonsezi zidzakhara kachisi wake owona.

2) Mphamvu za kulamulira

Kukhara ndi zichitochito za m'banja la Mulungu

Chomcho ngati iwo amene analengedwa mu chifaniziro cha Mulungu, ife tamawonetsera Mulungu kuchilengedwe chonse. Mapulani a Mulungu ndi okuti chilengedwe chidziyang'ana kwa munthu ngati chikufuna kumuwona Mulungu. Zilipo zinthu zingapo zimene zimatisiyanitsa ndi zinthu zina zonse za dongosolo la zolengedwa – upangiri wathu, kuzizindikira kwathu, kuthekera kwathu kopfunzira ndi kukula, koma cholinga cheni cheni kwa amene tili chifaniziro cha Mulungufe ndi chomwe chinaperekedwa mu nkhani kuti; kuti tilamulire pa nsomba, mbalame, zinyama ndi zamoyo zonse. Mawu okuti kulamulirawa akutanthawuza kusamalira, kukhara oyang'anira m'malo mwa Mulungu. Ife atiyitanira mu zichitochito cha zochitika za mu banja la Mulungu, monga a kumbali ya gulu la otsogolera zochitika. Chidwi chachikulu chili pochita zinthuzo monga momwe Mulungu amachitira, lye ndi mwini. Anaziyanamba ndi iye, ife anatiyitanira kuti titenge nawo gawo, ndipo tikuyenera kuchita zinthu munjira imene iye amachitira. Ife tikuyenera kukhara ngati Mulungu obweretsa dongosolo kuchoka mu chisokonezo ndi cholinga chakuti moyo uchite bwino.

Kuyang'anira – kupanga uku tikusamalira

Zinthu za dziko zayikidwa m'manja mwathu. Kodi munachiwona chiyitaniro chakuti kunjira kwa munda uja kuli golide ndi zomera zonunkhira komanso myala ya mtengo wapamwamba? Zimene zijatu zinaperekedwa kwa ife. Tikhoza kugwiritsa ntchito zinthu za dziko lapansi. Zinthu zikuluzikulu zopangidwa, matayala, injini, magetsi, zamagetsi, makompyuta ozama; zonsezi ndi zotsatira za kugwiritsa ntchito kwathu kwa zinthu za dziko lapansi ndi kubweretsa dongosolo kwa izo. Komabe ntchito yathu ndi yakuti tidzisamalire zinthuzo uku tikuzigwiritsa ntchito. Tikuyenera kuwonetsetsa kuti dziko tapatsidwali likuyenera kuyenda bwino ndi kulimbikitsa moyo. Izi zikutanthawuza moyo onse, osati kagawo kakang'ono chabe ka anthu mu mbadwo wathu uno koma kwakukulukulunso kuti zinyama zathu ndi zomera zichite bwino kuti munthu aliyense kudziko kuno achite bwino, zomwe zidzachititse kuti mibado yamsogolo idzachitenso bwino. Zimenezi ndiye gawo la kuyitanidwa kwathu.

Kuyitanidwa kwa Isilayeli

Tikayang'ana mkatikati mwa mbiri, Mulungu anayitana Isilayeli kuti akhare ufumu wa ansembe (Ekisodo 19:6), mtundu watunthu umene udzayimire Mulungu kudziko lapansi, m'malo mongoyimira banja limodzi.

Chithunzithunzi chenicheni cha Mulungu

Kumapeto a zonse anatomiza munthu otchedwa Yesu Khristu, amene anali chifaniziro cheni cheni cha Mulungu kuti akhare oyimira Mulungu ku chilengedwe chonse. “Iye amene wandiwona ine wawawona Atate” (Yohane 14:9) Pawulo akunena kuti “Mwana ndi chifaniziro cha Mulungu osawonekayo” (Akolose 1:15). Tsopano tikhozano kuwona mmene Mulungu amawonekera, chifukwa chakuti tamuwona Yesu. Komanso tikhoza kuwona mmene anthu alili akakhara popanda tembelero la tchimo. Tikuwonamo chifundo ndi chilungamo, kukhulupirika, Chimwemwe, chisoni, kusangalala, kupsya mtima ndi kuwupeza mtima. Umenewu ndiye umunthu opanda banga monga momwe Mulungu anatilengera. Tikaganizira zakukhara ofafana naye Yesu timakhara kuti tikukwanira mu umunthu wathu, monga momwe Mulungu amafunira.

Ufumu watsopano wa ansembe

Iwo amene panopa ali okhulupilira mwa Yesu, amene ali “mwa Yesu”, ayitanidwa kuti akhare gawo limodzi la ntchito yoyimira Mulungu ku zolengedwa zonse. Ife ndi amene tikusamalira dzikoli ndi kupangitsa ulamuliro wake kuti utheke. Tsopano timatchedwa amsembe a chifumu (1Pet 2:9). Kotero tili ndi mawudindo awiri. Timapita kwa Mulungu kukayimira chilengedwe chake (zomwe zikutanthawuza kuti, tinayitanidwa kuti tidzipemphera), ndipo timapita kwa zolengedwa zake kukamuyimira Mulungu (zomwe zikutanthawuza kuti, monga gawo limodzi timaliwonetsa dziko mmene Mulungu alili ndi kulengeza uthenga wabwino kuti Yesu ndi Mfumu yeniyeni.

Mafunso okambirana:

1) Kodi ndi chifukwa chani kumvetsetsa zokhudza chifanizo cha Mulungu kuli kofunikira kwambiri mu maphunziro okhudza bayibulo?

2) Kodi ndi zovuta zANJI za fanizo la Mulungu pamene tikukumana ndi zinthu za moyo uno monga kusankhana mitundu, mawulumali, umphawi komanso kuchotsa pakati?

2.3 - Nsanamila za kulenga

Kufikira pano tawerenga limodzi Genesis 1 ndi 2, ndipo taye setsa kumvetsa zomwe machaputala amenewa akutiwuzza zokhudza Mulungu, chilengedwe chake ndiponso uundo wathu ngati mtundu wa anthu. Lero tiwona zina mwa zinthu zofunikira kuchokera mu ndime zimenezi.

1) Ulemu wa ntchito

Tiyeni tione pamene ntchito ikuchokera munkhaniyi, tikumuwona Mulungu akukhara oyamba kugwira ntchito. Osangokhara ntchito yake yokudza chilengedwe ayi, komano mmanja mwake - pakulima munda. Iye anapangitsa kuti mitengo ya mitundu mitundu imele, imene yonse inali yabwino kudya komanso yosangalatsa m'maso.

Adamu anachokera ku fumbi ndi kuyikidwa m'munda. Ntchito yake inali yakuti adziwusamalira. Adziwulimilira mmene Mulungu amachitira. Iyeyu amkapitiliza ntchito ya Mulungu. Zimenezi zinali zofunikira. Ntchito siyinatadze chifukwa cha kugwa kwa munthu ngati mmene anthu ena amaganizira. Zilimo mu dongosolo la kulenga, pasanabwere tembelero lililonse lisanagwe panthaka. Umu ndi mmene Mulungu anakomzera kuti anthu adzikhala. Ntchito ili ndi kufunikira kwina kwake pamoyo wa munthu. Ndi gawo limene limatithandizira ife kuti tidzidziwona kuti umunthu wathu ndi okwanira. Kukhara ndi chochita, kubalitsa, kusangalalira ntchito za manja athu. Pali ulemu wawukulu mu zimenezi, ife tili ngati Mulungu mu gawo limenelo.

Imeneyinso ndi njira imene Mulungu amatipatsira zinthu. Kupereka zakudya kwake kwalumikizika m'chilengedwe, zimabwera pamene tikugwiritsa ntchito zinthu zomwe Mulungu watipatsa pokhulupilira kuti iyeyo adzichulutsa. Kwa Adamu, Mulungu anapereka zinthu zambiri. Anampatsa mbewu zoti adzale, nthaka yabwino, komanso zoyenera kuti nthaka ikhale bwino, kuwala kwa dzuwa ndi madzi. Analinso ndi kuthekera kophunzira upangiri ndi luntha ndi cholinga chakuti zomera zake zichite bwino komanso anali nazo mphamvu kuti akwanilitse zimenezi. Tsopano iye nayika mbewu ija mu nthaka ndi chikhulupiliro kuti munthawi ya Mulungu adzazikuza ndi kudzychulukitsa ndi cholinga chakuti akhare nacho chakudya komanso ndi mbewu zina zokuti adzadzale.

Njirayi ndi yofanana, ntchito iliyonse imene timagwira pogwiritsa ntchito zipangizo zimene tili nazo upangiri wathu ndi luntha timakhara kuti tikuthandizira kupanga chinachake chimene chachulutsa mtengo wa kufunikira kwake ndipo atilora ife kuti tilandire zipangizo zambiri kuti tikhare nawo moyo komanso kuti tigwiritse ntchito. Pali ziphunzitso zambiri zosokonekera zokhudza "kukhara mwa chikhulupiliro" ngati njira yakupezera zosowa, tikuyitanidwa ku chidaliro cha chikhulupiliro kwa Mulungu Atate wathu monga mmene zinalili ndi Adamu. Ndiko kunena kuti tikuyenera kukhara obala komanso kuti zimene tikubalazo zikhare zoyenera ndi kuwapangitsa ena kuti zawo ziyende. Pawulo ndi chitsanzo chabwino cha zimenezi, pamene iye analengeza



kwa akulu a mpingo ku Efeso kuti wawapatsa chitsanzo chokuti atsature. Kudzera mu kugwira ntchito molimbika adzipezera okha zosowa zawo, zosowa za ogwira nawo ntchito, ndi anthu amene akusowekeka thandizo pakati pawo lyenso anawachenjeza anthu a mpingo wa ku Tesalonika kuti ngati wina safuna kugwira ntchito asadye. Izi zikubwera kuchokera mwa momwe amaliwonera dziko ndi kufunika kwa ntchito. Ngkhare kuti zimenezi ndi zophweka kudzikamba kusiyanana ndi kudzychita. Tiwona mu zotsatira za kugwa pa ntchito mu gawo lathu lachitatu la phunziro lathu. Komabe tiyeni tisaphonye mpata umene Mulungu anatipatsa ogwira ntchito molimbika, wa kukhara obala, wa kukhulupilira Mulungu mu zichitochito zathu ndi kukhutitsidwa mwa kusangalala ndi zipatso za zimene mwazigwilira ntchito.

Ntchito yathu ndi gawo la ntchito imene Mulungu anatipatsa munga olamulira komanso ayang'anira a chilengedwe. Osati kungotipatsa zosowa zokha koma ili ndi cholinga chachikulu chobweretsa dongosolo kuchokera mu chipwilikiti, ndi cholinga chakuti moyo uchite bwino. Taganizani za dziko la Dubai. Ndithu dziko limeneli ndi chipululu, kulibeko kalikonse kumene kuja koma mtundu wa anthu uli ndi mzeru zakuya mwakuti mu zaka zoposa 50 zokha dzikoli lachoka pongokhara chinthu wamba mkukhara mzinda olozeka padziko lonse. Taganizirani za zinyama zimene zinakhara kumalo ake omwewa mu zaka mazanamazana zapitazo ndipo sizinayambe zaganizapo zosintha malowo, ngakhare zinyama za mzeru zakuya sizinakapezeka kuti zingakonzee malo ozungulira munga mmene angapangire anthu. Izi ndi zinthu zochititsa chidwi zimene Mulungu anayikiza mwa ife.

2) Kufananiza ndi kusiyanitsa zinthu

Tikhoza kuphunzirapo zambiri kuchokera mu ubale wa Adamu ndi Eva. Tikuphunziramo zokhudza banja, kuchitira zinthu limodzi, ndipo chachikulu kwambiri tikuphunzira zokhudza Mulungu mwini wake. Mulungu amasiyanitsa zinthu zingapo zosiyanana kachitidwe, kuwala kuchokera mu mdima, madzi ndi kumwamba, mtunda ndi nyanja ndipo pomaliza pazonse munthu wa mamuna ndi wamkazi.

Analengedwa mu chifaniziro chake, mamuna ndi mkazi; ofanana kotheratu mu kufunikira kwawo komanso mu ulamuliro pamene akulamulira pa chiengedwe. Ofanana koma osiyana. Adamu sanali bwino, “Sikoyenera kuti mamuna akhare yekha”. Chifukwa? Chifukwa chakuti sakanatha kukwanilitsa cholinga cha Mulungu pa iye yekha. Amkafunikira thandizo, osati mmene zinyama zingakwanitsire kumuthandizira. Ngati mmene ng’ombe yamphamvu ingakwanitsire kukoka pulawo. Panalibe chinyama ngakhare chimodzi chimene chikanakwanitsa kuthandiza pa zomwe Adamu amasowa. Iye anali ndi mayitanidwe akuti apitilize ntchito ya Mulungu yobweretsa dongosolo kuchokera ku chisokonezo, zija timati “tohu wa bohu”, opanda mawonekedwe komanso kalikonse. Iyetu amkadziwa kupanga zinthu koma samkadziwa kulidzadza dziko. Koterolo Mulungu analenga Eva. Monga Adamu, koma osiyana kwambiri. Eva anali ndi kuthekera kosamala ndi kubala moyo. Limodzi anthuwa akhozano kupanga ndi kudzadzitsa, limodzi akhoza kukwanilitsa ntchito imene Mulungu anawapasta yakuchulukana ndi kulidzadza dziko lapansi ndi ulamuliro wa Mulungu.

Kotero kuti iwo anali ofanana kotheratu mu zonse, koma osiyana mu zichitochito, aliyense mwa ife amafuna mzake kuti tikwanilitse zimene Mulungu watipatsa kuti tipange. Pali kudalirana pakati pa mamuna ndi mkazi. Izi zikutipatsa mzeru yokhudza Mulungu, amene ali mmodzi mu utatu, kufanana kotheratu koma osiyana mu zichitochito.

Bayibulo limafananiza ubale wa pakati pa Yesu ndi Mulungu ndi ubale wapakati pa mkazi ndi mamuna wake. Mamuna ndi mutu wa mkazi wake monga zililinsu kuti Mulungu ndiye mutu wa Yesu (1 Akolinto 11:3) pali gawo la ntchito losiyana zimene siziyenera kuti tilekanitse kuti zofunika ndi ziti kapena zosafunika ndi ziti.

Pawulo anagwiritsa ntchito ubale wa Yesu ndi mpingo kuti atiwonetse mmene utsogoleri wa mmbanja ukuyenera kukhalira, monga momwe Yesu akondera mpingo ndipo anapereka moyo wake kuti awusamalire komanso kuwutetedza, chimodzimodzinso amuna akuyenera kuwonetsa chisamaliro pa moyo, ndi kudzipereka kwatunthu kwa mkazi wawo. (Eph 5:28). Imeneyi ndi njira ya utsogoleri wa Yesu, ndipo imapereka muuni ku njira imene iye amafunira kuti mabanja onse adziyendera.

Mafunso okambirana:

1) Kodi mawu okuti ‘kukhara ndi moyo kudzera m’chikhulupiliro” mumawamvetsetsa motani?

2) Kodi mzeru ya upangiri ya ubusa yomwe mukuyiwona mu njira zolengerazi ndi iti?

2.4 - Njira ya mu bayibulo yokhudzana ndi kulenga

Mu ziphunzitso zitatu zomwe taphunzira m’mbuyomu, tayang’ana mmene nkhani yokhudza kulengedwa kwa zinthu yalembedwela kwa ife mu chaputala 1 ndi 2 cha buku la Genesis potiwuza ife zokhudza Mulungu, dziko limene tikukhalamoli komanso zokhudza malo athu mu dziko lapansili. Ndikufuna ndigwiritse ntchito gawo ili kuti ndikufotokezereni pang’ono mmene njira imeneyi imagwiritsidwila ntchito pamene tiwerenga bayibulo. Kumvetsetsa msanamira zikutanthawuza kuti tikhoza kumanga nsanamira yolimba ya kumudziwa Mulungu yomwe ikhoza kukhala chilimbire ndi kusatekeseka ndi ‘mphepo zosiyanasiyana za zikhulupiliro’ zimene zimabwera ndi kumapita.

1) Mulungu m’modzi woona

Ngakhare kuti bayibulo likukamba za zolengedwa zambiri zosiyanasiyana ‘za uzimu’ mwakuti zina mwa izo zimatchedwa ‘milungu’ imene imkalambilidwa koma pali Mulungu m’modzi yekha woona, iye amene analenga dziko lapansi ndi chilichonse chomwe chatizungulira chimene timachiwona ndi mawu okha. Mtumwi Pawulo anagwiritsa ntchito malingaliro amenewa pamene analimbana ndi anthu osakhulupilira

Mulungu ku Atene, pakuyizindikira milungu yambiri imene iwo amkayilemekeza koma anawapangitsa kuti amudziwe 'Mulungu amene analenga dziko ndi zonse zili mkati mwake, Ambuye wa kumwamba ndi dziko lapansi.' Amenewa ndiwo anali maziko a uthenga wake kwa anthu a madera onse. Mulungu m'modzi ameneyu anali pamwamba pa milungu ina yonse. Iye ali nayo mphamvu, mzeru zonse ndi chidziwitso chonse, ulamuliro onse. Ndithu iye ndi yekhayo amene akuyenera malambiro athu.

2) Kulambira ndi kupembedza mafano

Njira imeneyi ya kalambilidwe ndi yomwe yayendelera mu bayibulo lonse, ndi yesero la munthu kuti alambire zinthu m'malo molambira Mulungu owona amene ali opezekeratu nthawi zonse. Kupembedza kwina konse ndi kupembedza mafano. Mtundu wa anthu unapangidwa kuti ukhare okonda, kulemekeza ndi kulambira Mulungu m'modzi yekhayo. M'menemu ndi momwe timapezera dongosolo m'miyoyo yathu. Pawulo mu kalata wake opita kwa Aloma anayamba ndi mawu amenewa. Ananena kuti chilengedwe chinawulura mmene Mulungu owona alili, koma anthu akanika kumulambira iye ndipo pakutero anasanduka akhungu zimene zinachitista kuti pakhare mitundu yonse ya chipasuko komanso chipwilikiti.

3) Ubwino wa Mulungu

Nkhani yokhudza kulenga imatizindikilitsa zokhudza Mulungu m'modzi yekha amene ali owona, yemwe ali osamalira komanso wachikondi, komanso wamphamvu ndi wamzeru. Zizindikiro za chikondizi zikhodza kuwonekera kwambiri poyerayera, mpaka pamene Yohane analemba mu imodzi ya makalata ake kuti, 'Mulungu ndi chikondi.' Ndi mmene zochita zonse komanso zotilimbikitsa zimachokera. chikhulupiliro chake mu chikhalidwe cha chifundo cha Mulungu chosasintha ndi chikondi zimene chimatilora ife kuti tidziyika chiyembekezo chathu mwa iye. Ndi chikondi cha Mulungu chimene chimatitsogolera ife ku chilungamo chake. Chifundo chake kwa iwo amene akuponderezedwa, kusawutsidwa kapena ali pachiwopsyeyo, ndi chisoni komanso chisomo chake kuti apange njira ya chilengedwe chake chosokonekerachi kuti chibwelere kukhara pa ubale ndi iye.

4) Utatu wa Mulungu

Pano, mkatikati mwa nkhani yokhudza chilengedwemo muli njira imene Mulungu akudziwika kuti tate mu umodzi wake; Tate, Mwana ndi Mzimu Oyera. Tawonatu kuti Mzimu unali kufungatira pamwamba pa madzi owinduka, tilinso ndi mawu a Mulungu akulankhula zokhudza kulenga ndi kupangitsa kuti kutheke, ndipo Atate akuyang'anira ndi kutsogolera ntchito yawo. 'Tiyeni tipange munthu mu chifaniziro chathu' anatero.

5) Nthaka

Tikuwona kuti nthaka inaperekedwa kwa anthu kuti adziyisamalira bwino. Choncho tikuwerenga mu pangano limene Mulungu anapanga kwa Isilayeli kuti akuyenera kusamalira nthaka, kuyilora kuti idzipumula mu nthawi zina, kuwonetsetsa kuti ikubala

bwino. Nthaka ikulumikizana kwambiri ndi ubale umene ulipo pakati pa mtundu wa anthu ndi Mulungu. Momwemonso nthaka nayo ikudikira monga Pawulo akunenera, kudikira kuti ana a Mulungu avumbulutsidwe. Pamene tidzawukitsidwa, kulandira ulemelero ndi kupatsidwa matupi a tsopano limene lidzakhare mpaka kalekale, chomcho dziko lidzabwezeretsedwa. Nalo lidzakhala ndi kuwukitsidwa kwake.

6) Munthu okwana

Mtundu wa anthu unapatsidwa ntchito yofunikira kotere kuti ukayang'anire ndi kulamulira dziko lapansi. Ahebeli 2:6 -8 imakamba zomwe zili mu Masalmo 8, yomwe imakamba za udindo umene unaperekedwa kwa mtundu wa anthu kuti ulamulire, koma imazindikira kuti pakadali pano sitidziwona zimenezi zikuchitika mokwanira. Olembayo kenako akutitsogolera kwa Yesu, munthu m'modzi yekhayo amene anakwanilitsa udindo wake mu umunthu, munthu mmodzi amene adzabweretse abale ake ambiri kuti adzatenge nawo gawo mu ulemelero. Amene amatithandiza mu mayesero athu chifukwa chakuti naye anakumana ni mayesero. Iye amatiwonetsera mmene umunthu weniweni umawonekera. Chomcho tikungoyenera kuyika maso athu pa iye.

Yesu mwiniwake amakonda kugwiritsa ntchito dzina lodyera lakuti, 'Munthu' (mabuku ambiri anamasulira kuti 'Mwana wa Munthu'). Iye anatenga dzina lake lodyelali mu ulosi wa mu buku la Daniyele 7, amene anawona masomphenya a mdani wamkulu wa Mulungu, akuwawononga anthu a Mulungu. Kenako Mulungu akubwera ndi kudzatenga malo ake pampando wake wachifumu, ndipo Daniyele anawona wina okhara ngati 'munthu' akuyandikira kwa Mulungu ndikupatsidwa ulamuliro, ulemelero ndi mphamvu, ndipo mitundu yonse ya dziko lapansi ikumulambira iye. Yesu amkadziwona iye mwini ali pa udindo umenewu, kuchoka mu kuzunzidwa ndi mdani wa Mulungu koma ali osankhidiwira ulemelero. Zosangalatsa mkukhara kuti mtsogolo mwa chaputalacho, mmene mngelo amkatanthawuzira masomphenya, sanali munthu mmodzi yekha ayi, koma anthu onse a Mulungu amene apatsidwa ulamuliro ndi kuti alamulire ma ufumu onse a padziko, ngati Mulungu mmene anamuuza Adamu kumayambiliro kwenikweni kwa chiyambi.

Ntchito yofunika kulemba: kodi ndi dziko la mtundu wanji limene Mulungu amkafuna kuti chikhare cholowa chathu?

3.1 - Kugwa – Adamu ndi Eva

Tawonatu gawo la chochitika choyamba cha nkhani yathu, kulengedwa kwa zinthu zonse ndi Mulungu amene anapangitsa kuti zonse zichitike ndipo amene anazipangitsa kuti zonse pamodzi zizidzigwira ntchito bwinobwino. Panopano tikulowa mu chochitika chachwiri chomwe chili 'kugwa.'

1) Chisankho

Pakatikati pa mundapo panali 'Mtengo wakudziwitsa zabwino ndi zoipa'. Mtengowu ukuwoneka kuti kungowuwona poyamba umawoneka ngati ndi zinthu zabwino zokuti utengeko ndi kudya komabe Mulungu ananena kuti, 'Usadye chipatso chake'. Komano chifukwa chani?

Mwina tikayang'ana kwambiri mkati mwa nkhani ya mu bayibulo tikhoza kumvetsetsa. Mu 1 Mafumu 3 tikupezamo nkhani ya ulamuliro watsopano akutenga udindo. Solomo ndi wachinyamata ndipo dziko lili pamapazi pake. Iye analowa mu ufumu kamba kakuti bambo akenso anali mfumu, ife apa tikupezapo kenakake ka zimene Mulungu amkafuna, anthu akuti akamuyimilire iye kudziko lonse lapansi. Zili ngati tabwerezanso chochitika chokhudza kulengedwa kwa zinthu koma panthawiyi solomo akulowa m'malo mwa Adamu. Mulungu anampatsa iye chisankho ponena kuti, 'Tapempha chilichonse chimene ukufuna ndikuchitire.' Solomo poyankha anena kuti iye akadali mwana ndipo sangathe kulamulira ndipo iye anampempha Mulungu kuti amupatse mzeru kuti adziwe 'Zabwino ndi zoipa' ichitu ndi chiganizo chomwe chija chomwe mu chihebeli chinagwiritsidwa ntchito pokamba za mtengo uja mu Genesis 3. Solomo anapambana yeseloli, chisankho chosakasaka mzeru za iye mwini kuti adzitha kudzisankhira chimene chili chabwino ndi choyipa kapena kusankha mzeru ya Mulungu ndi kuyenda mwakumumvera iye. Mulungu anasangalala ndi chisankho chake ndipo anamupatsa iye chuma chambiri komanso ulemu.

Adamu ndi Eva anali ngati makanda amene samkadziwa chabwino ndi choyipa. Mulungu amkafuna kuti iwowa aphunzire kumumvera iye, pang'ono ndi pang'ono. Koma mmalo mwake anadzisenzera udindowu kuti adzitha kuzindikira chimene chili chabwino ndi choipa, kufuna kuti akhare pa okha mosadalira Mulungu

Tiyeni tiwone mmene zinachitikira.

2) Yesero

Funso lofunikira kwambiri ndi lakuti, 'Kodi tikhoza kumukhulupilira Mulungu?' cholengedwa chachilendo m'munda muja chimene chimafotokozedwa kuti njoka, njokayo inali itapanga kale chisankho chowukira ulamuliro wa Mulungu. Inagwiritsa ntchito bodza ndi mafunso osyasyalika ndi cholinga chofuna kusuntha chikhulupiliro cha Eva mu ubwino wa Mulungu. Mapeto ake inamuuza Eva kuti, 'Mulungu amafuna kuti Evayo asakwanilitse zimene iye anakatha kukwanista kuchita. Zikanakhara kuti iye akhoza kuzipangira ziganizo za iye yekha mmalo motsatiira zimene Mulungu anamuuza akanatha kukhara ngati Mulungu mwiniwake.'

Atamvera bodzali iye anayamba kuchiyang'ana chinthu cha mayeserocho. Anachiyang'anitsitsa mwachidwi poganizira mmene chimawonekera bwino m'maso komanso polingalira kusangalatsa kwa mmene zotsatira zake zingakhalire.

3) Tchimo

Pamene Eva amkaganizira zonsezi anakhulupilira bodza ndipo chikhumbokhumbo chokhara odzilamulira chinakulirakulira mkati mwake, ndipo anabala tchimo ndipo anatenga chipatso chija ndi kudya. Ndipo za Adamu, malemba akunena kuti naye anali naye mkaziyo ndipo zachidziwikire amkangoyang'anira mwakachechete uku Eva akuputsitsidwa ndipo mwadzidzi komanso kwanthawi yoyamba mu chidziwito cha munthu, Adamu ndi Eva anamva manyazi.

Kudzipimba – iwo anayamba kudziwona mosiyana; sanakhalenso ndi chikhulupiliro mwa mmene Mulungu anawalengera, anayamba kudzizindikira ndipo amkafuna adziphimbe okha, kudzibisa kwa wina ndi mzake.

Kudzibisa kwa Mulungu – anayamba kuchita mantha ndipo anamubisala Mulungu. Mtima wa manyazi unawapangitsa iwo kudzichotsa pamaso pa Mulungu. Iwo amawopa zomwe Mulungu angaziwone ngati angawonane naye maso ndi maso.

Imfa inalowa mu dziko lapansi – Mulungu anali atawawuza kuti ngati angadye chipatsochi adzafa ndithu. Komabe Adamu ndi Eva anali akadali ndi moyo. Komabe mphamvu ya imfa inali itamasulidwa, m'magawo onse awiri; m'moyo wawo ndi mu dziko limene anawapatsa iwo kuti aliyang'anire. Imfa ndiyo mphamvu imene imawononga dziko lapansi. Imabweretsa chisokonezo pamene pali dongosolo, imabweretsa mipatuko pamene panali mgwilizano. 'Uchimo ukakula ndi kukhwima umabala imfa' (Yakobo 1:5). Zotsatira za uchimo wa Adamu ndi Eva kunali kulowa kwa imfa mu dziko lapansi. Zimenezi zikuwonekera mu zoopsya zimene zikuwonekera m'ma chaputala akudza, chiwawa, kuponderezana, madano, ndi imfa ya kuthupi zomwe zikubwera mwachangu mu dziko labwinoli, limene Mulungu analiyamikira kuti 'zili bwino'.

4) Chigamulo

Izi ndi zofunikira kwambiri mu maphunziro okhudza nkhani za mu bayibulo. Chigamulo si Mulungu opsya mtima amene akupereka chilango chake pa mtundu wa anthu osowa pogwira, koma ndi Mulungu oweruza olungama amene akugwira ntchito kuti azipangitse zinthu ziyende bwino. Iye amakhara kuti akuchita zinthu pofuna kuwongola khalidwe lowononga lomwe limabweretsa chisokonezo mu dongosolo la chilengedwe.

Ziweruzo zake nthawi zonse zimabwera ndi cholinga chofuna kubweretsa chiwombolo. Tikakamba zokhuza Eva chigamulo chake chinakhudza kwambiri udindo umene Mulungu anamupatsa kuti asamalile moyo ndi kukhara omuthangatira Adamu. Zimenezi zinachititsa kuti pabwere zotsatira pa azimayi mu mbiri ya dziko lapansi pankhani za ziwopsyeyo za ululu umene umabwera pobereka. Ili ndi gawo limene limawonetse kufooka kwathu ndi chidaliro chathu pa Mulungu. Chigamulo chake chapangitsa mtundu wa anthu kumufunafuna Mulungu ndi kuzindikira kufunikira kwa chisoni chake.

Chimodzimodzinso ndi Adamu, chigamulo chimene chinagwera iye chinakhudzanso ntchito yake, panalibenso chiyembekezo cha chikhulupiliro chakuti zomwe wadzala

30 Kuzindikiritsa za chiphunzitso cha m'bayibulo chokhudza mulungu

zikhoza kukulanso bwinobwino. Komano zimenezi zinamubweretsera iye pamalo akuti adzidalira Mulungu kuti apeze zosowa zake komanso moyo wake.

Kwa njokayo, chigamulochi sichinabweretse chiwombolo. Izi zikutiwonetsa kuti zigamulo zina za Mulungu zimakhara zomaliza. Ndinkhani yonena kuti sipakhalanso ziwonongeko zina, kuwonetsa kuti kwakwana, kwakwana. Chigamulo chake chinali chakuti njokayo idzakwawa ndi mimba, chinthu chimene chili cha manyazi kwa cholengedwa chimene chimkafuna chitakhara ngati Mulungu. Panalinso lonjezo lakuti tsiku lina mwana obadwa mwa mzimayiyu adzaphwanya mutu wa njokayo, chinthu chachidziwikire chokhudza chipambano chimene chilimkudza chimene Yesu adzampambana pa oyipayo.

5) Undende

Adamu ndi Eva anathamangitsidwa m'munda muja, komanso pamaso pa Mulungu. Iyi ndi nkhani yoyamba mwa nkhani zambiri zokamba za undende m'malemba. Aliyense mwa iwo akuwona kuti wataya chinthu chinachake chomwe chili chofunikira kwambiri, ndipo amkafunitsitsa atabwelera. Anthu ambiri lero akumanapo ndi zinthu zofanana ndi zimenezi, monga kuchotsedwa pokhara, kukhara ndi chikhulupilirop chakuti zinthu zidzayenda, osapeza chikwanilitso chakuti akudziwa kuti penapake chilipo. Zimenezi ndi zikumbutso za zomwe zinachitika ku Edeni mumtima wa munthu wina aliyense, zomwe zinapangilidwa china chake chimene sichingapezeke kwina kulikonse koma mwa Khristu yekha.

Funso lokambirana: Kodi chikhulupiliro ndi kumvera ndi zolumikizana bwanji?

3.2 – Kayini ndi Abele

Nkhani ya kugwa siyikupezeka mu chaputala 3 cha buku la Genesis chokha ayi, koma pamene nkhanayi ikupitilira, timawona kuti zinthuzi zimabwerezedwabwerezedwa. Ngati kuti zikufuna kuwonetsera china chake. Olembayo anagwiritsa ntchito zambiri mwa mfundo zofananira mu nkhani ya Kayini ndi Abele.

1) Chisankho

Munkhanimu sitinawuzidwe kuti kodi ndi chifukwa chani nsembe ya Kayini inakanidwa, pamene ya Abele inalandilidwa. Zimenezi ndi zina mwa mfundo zomwe tikhoza kuziganizira kutsogoloku mu nkhani zokhudzana ndi bayibulozi. Pakadali pano zomwe tikudziwa ndi zakuti Kayini anakwiya kwambiri. Iyinso ndi nthawi yopanga chisankho, kuchita chomwe chili choyenera kapena kuchita cholakwika. Nayenso wayima pamtengo paja, kupanga chisankho chakuti ayende monga mwa njira imene Mulungu wamukonzera kapena ayende njira imene iye mwiniwake akuyiwona kuti ndi yoyenera.

2) Yesero

Kupsya mtima kumadza ngati chotsatira cha kupembedza mafano, kumene kuli kukonda chinthu china chake koposa mmene umamukondera Mulungu. Chomwe umachikondacho chikakhara pachiwopsyezo, zotsatira zake kumakhara kupsya mtima, ndipo ntchimo limakhara lili pafupi. Mu nkhaniyi, Mulungu akulongosola za kanthu kowoneka ngati kanyama kenakake kotchedwa 'Tchimo' kamene kakubwatama pakhomu la Kayini, kumufuna iye. Monga mmene zinalili ndi njoka ija, pomupusitsa Adamu ndi Eva, kanyamakanso kakuyesera kumunyengela Kayini kuti achoke pa njira ya Mulungu. Kayini anawuzidwa kuti ayenera kukalamulira kapena kuthana nako kanyamaka.

3) Tchimo

Kayini analephera kukalamulira kanyamako, ndipo mwa kupsya mtima iye anamutengera m'mbale wake kuthengo, kumeneko iye anamupha mmbale wakeyo. Tsopano apa tikuwona kudzera mu zenizeni mmene tchimo ndi imfa zimalumikizirana. Apapa tikuwona kuyamba kwa mmene munthu adzidzachita kwa anthu amzake akakhara kuti wagonjera zofuna za chinyama chija. M'mene ziwawa zingagwiritsidwile ntchito pofuna kupeza mphamvu ndi udindo. Umu ndi mmene zimakhala pamene anthu akukana njira ya Mulungu ndi kukhara moyo odzilamulira okha.

4) Chigamulo

Komanso nthaka inatembeleredwa monga zinalili ndi Adamu, ngakhare zikuwoneka kuti tembeleroli linali lolimbana ndi m'mene Kayini anagwiritsira ntchito malo osati kuti likukamba za dziko lonse.

5) Undende

Kayini anathamangitsidwa pamaso pa Mulungu, ndipo tsogolo lake linali lakuti akhara 'munthu oyendayenda opanda mpumulo'. Komabe panalinso chifundo, pamene Kayini anayikidwa chizindikiro kuti akhare otetezedwa kwa anthu amene amafuna kumupha.

Kotero tikuwona magawo ambiri a nkhani ya kugwa kwa Adamu ndi Eva akubwerezedwa mu nkhani ya Kayini ndi Abele. Tikuwona kuti magawo oyambilira eni eni a Bayibulo akutithandiza kudziwa mmene zilili ndi anthu komanso chifukwa chomwe ifeyo tikupezekera mu nyengo imene tili panopayi.

Nthawi zonse timakumana ndi chisankho chakuti tisankhe pakati pa kukhara moyo okhulupilira ndi kudalira Mulungu, kupanga chisankho potsatira zimene iye akunena komanso zimene iye akufuna kapena kukhara modzidalira tokha, kupanga zisankho zathu potengera zimene tikuziwona kuti ndi zabwino m'maso mwathu ndi zomwe tikuwona kuti ndi zabwino kwambiri.

Zisankhozo ndi zofunikira kwambiri pokhudza mmene ifeyo tingakhalire ndi anthu amene atizungulira. Kukhara momumvera Mulungu zimatanthawuza miyoyo yathu



ikhara malingana ndi dongosolo limene iye amabweretsa, pamene kukhara moyo wa kusamvera kumabweretsa chisokonezo chomwe chinaphimba dzikoli chilengedwe chisanadze.

Funso lokambirana: Kodi ndi nkhani zina ziti zokhudza mayesero zimene zikupezeka mu bayibulo? Kodi mukuwonamo kufanana ndi zimenezi mu iliyonse mwa nkhaniyo?

3.3 – Kugwa – kuwukira ndi chigumula

Kufikira pamo tawona mapeto a kuyesedwa kokhudza munthu payekha, kuwukira ndi tchimo. Tikuwonanso Mulungu akuchitapo kanthu kufuna kuyika malire pa tchimo. Komabe pambuyo pa Kayini tikupeza kuti mmodzi mwa zidzukululu zake otchedwa Lameki akutamika kunena kuti adzambwezera wina aliyense amene anamulakwira iye. Mwakuti analilumbilira banja lake kuti iye adzafika pomupambana Kayini pofuna chitetezo chake. Mtundu wa anthu ukugwa mu nyengo za mdima.

Zimene zikutambasuka mu nkhanimu tsopano ndi zomwe dziko labwino la Mulungu likukhara pamene mtundu wa anthu ukugwera mu chiwawa ndi kuponderezedwa.

Kuwukira mmiyamba ya kuthupi komanso ku uzimu

Chaputala cha 6 chikulongosola za dziko lapansi litamuwukira Mulungu. Izi zikuwonetseredwa mbali zonse; kuthupi komanso ku uzimu.

Choyamba pakuwoneka kuti panali kuwukira pakati pa ‘ana a Mulungu’ amene anadzipezera akazi ‘mwa ana a anthu’. Mwa chikhulupiliro cha chikhalidwe cha Chiyuda izi zikutanthawuza kuti angelo amene anamuwukira Mulungu akupanga chisokonezo pa dziko lapansi pokwatirana ndi anthu, chimene chinali chimodzi mwa zifukwa zazikululu zimene zinayambitsa choipa padziko lapansi.

Mabayibulo ambiri omasulilidwa mwamakono amatambasula mawu akuti ‘ana a Mulungu’ kuti ndi mafumu amene akukwatira anthu amene ali panso pawo, kapenanso ngakhare pa anthu amene analandira chifaniziro cha umulungu kukwatiwa ndi anthu amzawo, amene ngakhare anasinthika koma anali ngati zinyama ndipo mwa iwo munalibe ‘mpweya wa Mulungu’.

Kumasulila kwina kulikonse kumene mungakonde, mosakayikira muli kumuwukira Mulungu m’magawo onse, kuthupi ndi ku uzimu komwe.

Chigamulo ndi kuwonongeka kwa chilengedwe

Kuwukiraku kunachititsa kuti pakhare chipwilikiti chachikulu, kukhetsa mwazi, kubweretsa ululu ndi kudandawula mumtima wa Mulungu. Inafika nthawi imene Mulungu ananena kuti ‘Kwakwana’. Zikuwonetsa kuti Nowa yekha ndi amene anapeza kukonderedwa pamaso pa Mulungu, koterono tikuwona zichitochito za

Mulungu zopulumutsa chilengedwe chake ku zotsatira za uchimo, ndi kuwukira uku akuchotsa mkono wake osamalira pa mbali za chilengedwe zimene zinakana ulamuliro wake. Powona zimenezi tikuwona kuwonongeka kwa chilengedwe kukuchitika, ndi kubwelera kwa madzi owinduka amene tikuwapeza pachiyambi penipeni pa nkhani, Mulungu asanabweretse dongosolo.

Nowa monga Adamu watsopano

Tikumuwona Nowa kukhara Adamu watsopano amene anapulumsidwa ndi Mulungu kuti akhare ‘chilengedwe chatsopano’ iye akukhara ndi ulamuliro pa zinyama, ndipo akudalitsidwa ndi kupatsidwa ulamuliro wakuti alidzadzaze dziko lapansi. Uyu sikuti ndi ‘Adamu watsopano’ chabe, tizindikira pamene tikupitilira munkhanimu, chilichonse chanyamura chiyembekezo cha awerenga kuti anthu a Mulungu kumapeto kwa zonse akubweretsa ulamuliro wa Mulungu ku dziko lapansi.

Chipulumutso chimatanthawuza kupulumutsa

Iyi mkutheka ndi yoyamba mwa nkhani zathu za kupulumutsa zimene tikuwerenga kuchokera m'malemba. Anthu a nkhanza opondereza akuperekedwa ku zotsatira za njira zawo za kuwukira koma Mulungu akuwonetsera chisoni pamene akupulumutsa chilengedwe ku kuponderezedwa, ndi kuwamasula mu dziko latsopano kumene angaphunzire kumutsatira njira zake ndi mtima onse.

Mapeto ofanana

Mwatsoka monga mmene zimakhallira ndi nkhani za ambiri mwa achina ‘Adamu atsopano’ zimakhara ndi mapeto ofanana, Nowa anapezeka ali wa maliseche ndipo thembelero linamugwera Hamu ndi Kenani amene anali mwana wake.

Pangano loyamba Mulungu

Apa tikupeza pangano loyamba lowonekera lomwe linapangidwa ndi Mulungu, kupangira chamoyo chilichonse kuti sadzawononganso chilengedwe chake. Zimenezi zikhara ndi kufunikira kwambiri pa nkhani yomwe ili mkudza komanso mmene Mulungu atachitire pakuthana ndi vuto la choipa mu dziko lapansi.

Funso lokambirana: kodi nkhaniyi ikutiwuzwa chani chokhudza chilengedwe chatsopano chimene Mulungu adzabweretse padziko lapansi?

3.4 – kugwa – Babeloni wamkuluyo

Tawona mmene zayendera zokhudza kuwukira Mulungu, kuyambira mmbanja mpaka ku dziko limene likukana njira za Mulungu, mapeto ake panakhara chiwawa ndi kukhetsa mwazi. Kuwukiraku kukuwonetsa kuti kwamera mizu mwa anthu pamene tikuwona kuti mu zichitochito za mu chilengedwe chatsopano, zochitika za Nowa ndi banja lake nazonso zikuyenda njira yofanana..

Mibadwo ya mayiko

Chaputala 10 cha buku la Genesis chikutiwonetsera ife za midadwo ya mayiko imene ikuchokera mwa ana a Nowa, uliwonse mwa mitunduyo yapatsidwa malo ake ndi chinenero chake, kulidzadza dziko lapansi monga momwe zinalili poyamba pamene Mulungu anawalamura Adamu ndi Eva, ulamuliro umene tsopano wamugwera Nowa. Mundandanda wa mayikowu tikupezamo munthu mmodzi amene zakambidwa zokhudza iye, ndiye Nimurodi. Iye amkadziwika kuti ndi wankhondo wamphamvu, ndipo iye anayambitsa ufumu wake wake umene umaphatikizamo Babeloni ndi Asiliya, adani awiriri akuluakulu a anthu a Mulungu amene tiwapeze kusogolo kwa nkhaniku.

Nsanja ya Babulo

Chaputala 11 chikutipatsa ife chidziwitso chokhudza chiyambi cha Babeloni, kapena kuti Babelo monga momwe mabuku ena amanenera. Ku Babeloni tikuwonako chiyambi cha ufumu wa anthu omwe mwachidziwikire ukutsutsana ndi ufumu wa Mulungu. Tikuwona ufumu oyamba umene uli ndi chinenero chimodzi, mzinda umodzi, kachisi mmodzi ndipo chovuta kwambiri ndi chakuti unamangidwa kudzera mu chisokonezo ndi kuponderezana, kudzera mwa Nimurodi, wankhondo wamphamvu amene anayambitsa ufumuwu. Umenewu sunali mzinda umene aliyense anasankha kuti adzikhara mogwirizana, koma kumene anthu amagwiritsidwa ntchito mokakamizidwa. Masomphenya a Nimurodi anali akuti adzipangire dzina lalikulu la iye mwini ndi kusunghanitsa anthu ochulukana mmene angathere. Kutsutsana mowonekera ndi lamulo la Mulungu lakuti dziko lapansi lidzadzidwe.

Ufumu oyamba wawukulu

Uwu ndi 'ufumu' oyamba kapena kuti 'ufumu wa munthu' umene ukunenedwa mu bayibulo, nkhanu yomwe ikukambidwa kwambiri mu nkhanu yonse. Ena mpaka amalikamba buku la chivumbulutso kuti ndilo buku lokamba za mizinda iwiri ikulu ikulu; Babeloni ndi Yelusalemu. Ufumu wa munthu ndi ufumu wa Mulungu. Ufumu wawukulu oyambawu ukubweretsa mitu ya nkhanu yomwe ili yofalikira mu ma ufumu onse a mu bayibulo akusunghana kulimbana ndi Mulungu kudzipangira mayina odziwika ndi kugwiritsa ntchito kukakamiza ndi kuponderezana kuti akhadzikitse mphamvu zawo.

Kumasulidwa kwa oponderzedwa

Tikumuwonanso Mulungu akuchitapo kanthu pofuna kuwabalitsa anthu. Anthu ambiri oyikira ndemanga akhoza kuziwona zimenezi ngati kuchitapo kanthu kwa Mulungu pa kuwukira kwa anthu, kupangitsa 'kusakanikirana' kwa zilankhulo. Kungokhara ngati chaputala cha 11 chimayenera kubwera pambuyo pa chaputala 10 tikatengera nthawi. Chaputalachi chikukamba za zilankhulo zonse zosiyanasiyana kukhara zotsatira za chigamulo cha Mulungu pa anthu. Komabe oyikira ndemanga ambiri akhoza kukonda kuti chaputala 10 chimasulidwe pambuyo pa chaputala 11, malingana ndi mmene olemba weniweniyo amkafunira. Akhoza kumaziwona zilankhulo zosiyanasiyana ndi zikhalidwe zomwe zakambidwa mu chaputala 10 ngati njira imene Mulungu amafuna kuti dzikoli liyendemo, ndi ubwino onse umene

kagawanidweka kangabweretse. Kotero chaputala 11 chikuwonetsa kuti Mulungu akumasula anthu oponderezedwa, amene akakamizika kukhara mu zichitochito za ku Babeloni, kukakamizidwa kulankhula chilankhulidwe chimodzi ndi kumulambira Mulungu mu njira inayake. Imeneyi ikhoza kukhara njira yabwino yomasulira pamene tikuyang'ana gawo la chiphunzitso cha bayibulo, pamene tikuwona cholinga cha Mulungu chomasula anthu oponderezedwa ngati imodzi mwa mawuthenga ofunikira a nkhanayi. Ndithudi tikupezamo kufanana kwakukulu pa tsiku la Pentekosite mu buku la machitidwe atumwi m'mene chipembedzo cha Chiyuda chapanga ufumu wawukulu umene ukutamanda za mzinda umodzi okha ndiwo (wa Yelusalemu), chilankhulo chimodzi (Chihebeli) ndi kachisi mmodzi. Zotsatira za kukhutulira mzimu zinatanthawuza kuti iwo amene anali kunja kwa Yelusalemu anamva zodabwitsa za Mulungu mu chilankhulo chawo, anakwanitsa kukumana ndi Mulungu kunja kwa kachisi ndipo dziko lonse likhara loyera osakhala Yelusalemu yekha. Zimenezi zinachititsa kuti pakhare chilolezo kwa anthu kuti 'abalalikane' ndi kupita padziko lonse ndi nkhanu yabwino ya Yesu.

Kutsogoloku tiwona mu nkhanimu kuti khamu lalikulu linasonkhana patsogolo pa mpando wachifumu wa Mulungu mu buku la Chivumbulutso chaputa 7, mmene chilankhulo chilichonse, chikhalidwe komanso mtundu uliwonse wa anthu unali ndi owuyimilira, zimene zikuwonetsa kuti zikuyenera kukhara zochititsa kuti pakhare chisangalalo mmalo mokhara chizindikiro cha chigamulo cha Mulungu pa mtundu wa anthu.

Kotero tikutha kuwona kuti ufumu wa munthu ukhara olinga kufananiza, kusinthika kamba ka zomwe zamuzungulira ndiponso kuponderezedwa kwa iwo amene sakusinthika.

Mosemphana ndi zimenezi, ufumu wa Mulungu uli mu umodzi wowonetseredwa mu kubwezeretsedwa kopitilira, kudzera mu Chisomo ndi kulowa manja.

Ntchito: Kodi lerolino chimene mukuchiwona kuti ndi zotsatira za kugwa ndi chani?

4.1 – Isilayeli – pangano ndi Abulahamu

Kuchokera ku dziko labwino limene Mulungu analilenga, tikuwona kukhara kwa munthu kodzilamula yekha kudzichotsa kwa Mulungu kwabweretsera chisokonezo pa munthu payekha, ubale wake ndi ena komanso dziko komanso mu zichitochito za anthu tikayang'ana dziko lonse. Tikudziwa kuti Mulungu sadzangoliwononga dzikoli kenako mkuyambiranso, koma kodi Mulungu adzachipulumutsa bwanji chilengedwe chake? Zimenezi ndi zomwe tikambirane mu gawo lina la nkhanayi.



Abulahamu

Abulahamu akuwonetsedwa mu chaputa 12, titangotha kuwona zokhudza Nimrodi ndi kuwona za mmene ufumu wake umayendetseredwa, ndi zosakayikitsa kuti olembayo amkafuna kusiyanitsa zinthu ziwirizi ndi cholinga chokuti njira ziwiri za kakhaliidwe ziwonekere.

Nimurodi	Abulahamu
Bwera	Pita
Chilankhulo chimodzi	Zilankhulo zambiri
Kusonkhanitsa mu kachisi mmodzi	Mangani maguwa pamene mukupita
Mangani mzinda	Chokani mumzinda
Kukhadzikika	Kukhara m'mahema
Wamphamvu	Okhara m'chiwopsyezo
Kudzipangira dzina	Anayika ulemu wake mwa Mulungu
Kuwukira	Kumvera
Kuweruzidwa	Kudalitsidwa

Kotero Mulungu anasankha banja ndi cholinga chofuna kupulumutsa chilengedwe chake, pofuna kusunga mapulani ake ogwira ntchito mwa anthu kuti alamulire dziko.

Mdalitso

Pofuna kuthana ndi zotsatira za tembelero lomwe linadza padziko lapansi, Mulungu analengeza mdalitso pa Abulahamu ndi pa iwo amene adzamudalitse iye ndiponso kwakukulukulu anawulengezanso pa dziko lonse kudzera mwa zidzukululu zake za Abulahamu. Iliku ndi lonjezo la Mulungu la kuwombola dziko lapansi ku tembelero la uchimo, ndipo iye analonjeza kuti adzakwanilitsa zimenezi kudzera mwa chidzukululu cha Abulahamu.

Pangano

Patapita nthawi pamoyo wa Abulahamu. Mu chaputa 15 cha buku la Genesis, Mulungu analankhulanso ndi iye, ulendo uno anapangana naye kapena tinene kuti mgwirizano wa zochitika. Mu mgwirizano yambiri imene imkachitika nthawi imeneyo mbali zonse ziwiri zimayenera kuchita lonjezo lake la panganolo polumbira, kotero Mulungu kumbali yake anamulonjeza Abulahamu kuti adzakhara ndi mwana komanso kuti zidzukululu zake zidzakhara zambiri, mokuti palibe amene angadzakwanitse kuziwerenga ndiponso kuti zidzukululu zake zidzakhara mdziko limene iye amkayendamo kukhara cholowa chawo. Mulungu anachita monga mwa chikhalidwe poyambitsa kudutsa

pakati pa nyama zimene zinali zitadulidwa pakati, (zimenezi zimawonetsera kuti olonjezayo adzakwanilitsa lonjezano lake kapena kuti zimene zinachitika kwa zinyamazo zidzamugwera iye). Kotero Mulungu analonjeza ndi lumbilo limene ligwire ntchito mu bayibulo lonse.

1) Mdalitso

Pawulo akufunitsitsa kuti Agalatiya amvetsetse kuti dalitso umene Mulungu analonjeza ku dziko lapansi kudzera mwa Abulhamu linali la kukhuthulira Mzimu Oyera (Agalatiya 3:14) amene kumapeto kwake adzabweretse ulemelero onse wa Mulungu pa munthu.

2) Mwana

Pawulo analiwona lonjezo lakuti 'mbewu' kapena 'chidzukululu' kuti zimatanthawuza chinthu chimodzi – Yesu (Agalatiya 3:16) Iye anali kukwanilitsidwa kwa malonjezano a Mulungu kudziko lapansi monga anamulonjezera Abulhamu.

3) Mtundu

Ngati chidzukululucho ali Yesu, osati Isake ndiye kuti mawonedwe a Pawulo anali akuti si mbadwa za Isilayeli zomwe zidzalandire malonjezanowa, koma anthu omutsata Yesu amene anabweretsedwa kuchoka m'mitundu yonse komanso makhalidwe onse.

4) Dziko

Iyi yakhara nkhani yosawutsa m'masiku ano, Abulhamu analandila gawo la dziko kukhara cholowa cha zidzukululu zake. Pawulo akuyimasuliranso nkhaniyi kunena kuti naye adzapatsidwa dziko lapansi (Aloma 4:13). Kumaliza kwake kwa malingaliro akewa pakukwanilitsa kwa magawo ena a lonjezano la Mulungu limene anapangana naye. Dziko lonse lapansi lili m'manja mwa Yesu Mfumuyo (Chiv 11:15), Kumeneku ndi komwe nkhaniyi ikupita.

Kuvomereza kwa chikhulupiliro

Abulhamu anangomva malonjezano a Mulungu amene anamulonjeza iye ndipo anamukhulupilira Mulungu. Genesis 15:6 ikulongosola za nthawi imeneyi kuti ndi nthawi yomwe kunawerengedwa kwa Abulhamu kukhara kulungama. Mau akuti, 'kulungama' akhoza kumasulidwa mosavuta kunena kuti 'kukhulupilika ku lonjezano'. Pamene mgwirizanowo unakhazikitsidwa komanso Mulungu anapanga malonjezo ake, podutsa pakati pa zinyama kukhara chizindikiro cha lumbilo la lonjezano. Abulhamu sanalonjeze china chilichonse ngakhare kuyenda pakati pa nyama zodulidwa pakatizo monga momwe Mulungu anachitira. M'malomwake anamukhulupilira Mulungu. Limenelo ndilo gawo lake lokhalo lakukwanilitsa lonjezano. Ndipo iye anatengedwa kukhara okhulupilika ku lonjezano kudzera mu chikhulupiliro chakecho. Pawulo akukamba za zimenezi mu kalata yake yopita kwa Aloma, anawafotokozera iwo kuti njira yokuti iwo atengedwe kukhara anthu okhulupirika a Mulungu inali yotseguka kwa onse kudzera mu kumukhulupilira Mulungu (Aloma 3:22).

Funso lokambirana: kodi ndi motani m'mene akhristu amakhalira panso pa mdalitso wa lonjezo lomwe Mulungu anapanga ndi Abulhamu?

4.2 - Isilayeli – Mose ndi chilamulo

Tawona kuti ifeyo tikwanilitse kuthana ndi mavuto mu chilengedwe chake chabwinochi Mulungu amasankha banja kuti apereke mdalitso kudziko lapansi, izi zikuwonetseredwa m'moyo wa Yosefe, iye amene anali chiwonetsero cha Yesu, amene anayenda moyo okanidwa komanso wa mazunzo kenako mkukapezeka kuti wakwezedwa ndi kukhara olamura ndi cholinga chofuna kupindulira mitundu ya anthu yozungulira. Zimenezi zinachititsa kuti Yakobo ndi banja lake abwere ku Ijipiti kudzakhara ndi Yosefe, kumene iwo anasanduka kukhara mtundu koma anakhazikidwa mwawukapolo pansa pa Falawo wamphamvuyo.

Nkhani yokhudza chiweruzo

Nkhani yozizwitsa ya Mose amene anapulumutsidwa ku nkhwidzi za chiwopsyeyo cha Aijipiti, kutengedwa kukakhara mu nyumba yachifumu ndi kukhara mwana wa kubanja lachifumu ndi yodziwika bwino ngakhare kwa iwo amene sanawerengeko bayibulo. Nkhani yake yokhudza kupulumutsidwa kwake m'manja mwa Falawo inawonetseredwanso pa mlingo wa dziko pamene Mulungu anapereka chigamulo kwa adani ake ndi kupulumutsa anthu ake. Falawo mfumu yayikuluyo, komanso amene anali chinthu chomwe chimapembezgedwa ndi Aijipiti. Iye anali amene anachititsa kuti anthu a Mulungu aponderezedwe ndi kuphedwa. Mulungu ndipo anabweretsa milili ndi cholinga chopereka chilango kwa milungu ya ku Ijipiti, kwakukulunso anamkantha Falawo ndi imfa ya ana oyamba kubadwa, iye ndi dziko lake lonse.

Nkhani yokhudza kuwomboledwa

Okhawa amene anamukhulupilira Mulungu ndi kukhara pansa pa mwazi wa mwana wa nkhosa osalakwa sadzayimbidwa mulandu pamaso pa Mulungu ndipo amamasulidwa ku chizunzo chawo. Nkhani ya kuwomboledwa kwa mtundu wa anthuyi inakhara gawo lalikulu la umzika wa Isilayeli. Imakambidwa mu zambiri mwa nyimbo zawo komanso amayisangalira nthawi chaka ndi chaka pa phwando la Paska. Indedi panali pa phwando limeneli pamene Yesu anasankha kuwalongosolera ophunzira ake za pangano latsopano limene amawabweretsa, usiku otsatana ndi tsiku la kufa kwake.

Pangano ndi Isilayeli

Masiku 50 otsatira pambuyo pa 'Paska' kuwomboledwa, mtundu omwe unali utangokhadzikitsidwa kumene unakumana ndi Mulungu pa phiri. Apatu tikuwona ukwati pakati pa Mulungu ndi anthu a Isilayeli. Anakwatirana kuyambira m'masiku a Abulahamu komano iyi ndi nthawi imene iwo analumikizika kwa Mulungu kudzera mu pangano. Anapanga pangano molumbilirana. Mulungu analonjeza kuti ngati iwo atakhare okhulupilika kwa Iye mwatunthu ndiye kuti iyeyo adzakhara Mulungu wawo ndipo iwo adzakhara cholowa chake chokondedwa komanso ufumu wa ansembe omuyimira iye kudziko lonse. Anthuwo anayankha nati, "Tichita zonse zomwe Ambuyeyo anena." Iyi inali nthawi yoyera, nthawi ya 'kulengedwa kwatsopano' nthawi imene Mulungu akudzilumikiza ku banja ndi cholinga chofuna kupereka mdalitso ku dziko

lonse. Tsoka ilo Mose asanatsike phiri, Aisilayeli anapezeka atadzipangira milungu ndi zifanifani zomwe amafuna kuti azidzigwadira, zichitochito zakuti Mulungu amadzitenga kukhara chigololo. Zimenenso zidzamupangitse iye kuti tsiku lina adzalekane ndi Isilayeli ngati mmene zimakhallira ndi banja.

Zimenezi zikuwonetsera chinthu chovuta kwambiri zimene zimapangitsa kuti Isilayeli ayang'anilidwe pansi pamene Mulungu akulumikizana ndi mtundu wa anthu ndi cholinga chofuna kubweretsa mdalitso ku dziko lonse lapansi komano anthuwa ndiye limodzi mwa magawo a mavutowo.

Patatha masiku 50 Paska wina wamkulu atachitika, anthu atasonkhana kuti akondwelere Pentekosite komanso kuperekedwa kwa chilamulo, tikupezaponso nthawi ina ya 'kulengedwa kwatsopano' pamene Mulungu Mzimu Oyera akubwera kwa anthu ake mkudzalumikizana nawo, kudzawathandizira momwe iwo angakhalire komanso inali nthawi yowapatsa mphamvu anthuwo kuti akhare omvera.

Chihema

Cholozera cha mu buku la Ekisodo (ngakhare kuti siyingakhare gawo la nkhani yokoma kuwerenga) ndi kukhadzikiitsanso kwa kupezeka kwa Mulungu pakati pa anthu. Pamapeto pake Mulungu ndi munthu akulumikizana kukhara pamodzi, ngakhare tikupeza kuti buku la Levitiko lili ndi malamulo amene angapangitse kuti mtundu wa anthu ochimwawu ukhoza kufika kumuyandikira Mulungu oyera. Zimenezi ndizo zikutilozera ku kulengedwa kwatsopano kumene kukuwonetseratu zokuti Mulungu ndi munthu mkukhara mu umodzi zili kutali, komano mu malamulo amenewa tikuyambano kumvetsetsa ntchito ya Yesu yotibweretsa ife pamaso pa Mulungu.

Funso lokambirana: kodi cholinga cha chilamulo mu nkhani ya Mulungu ndi chiyani?

4.3 – Isilayeli – Davide ndi ufumu

Pambuyo pa pangano la Mulungu ndi Isilayeli kudzera mwa Mose, tikuwona kusawutsika kwa Aisilayeli m'chipululu muja, kugonjetsa kopambana kudzera mwa Yoswa komanso nyengo yayitali ya chipasuko pansi pa utsogoleri wa oweruza. Pamene Isilayeli akulimbana ndi kupembedza mafano, kusamvera Mulungu komanso kukula kwa mphamvu za adani awo m'mayiko ozungulira.

Khumbo lofuna kukhara ndi mfumu

Kufikira pano munkhaniyi, Isilayeli wakhara akutsogoleredwa ndi anthu obukitsidwa ndi Mulungu, kuwayitana iwo kuti akhare okhulupirika kwa Mulungu ndi kukwanilitsa gawo lawo ngati anthu oyimira Mulungu. Inafika nthawi yomwe Aisilayeli amkafuna atakhara ngati mitundu ya anthu imene inawazungulira, kwenikweni kuti

adzitsogoleredwa ndi mfumu. Mitundu ina yozungulirayo inali ndi atsogoleri awo amene anali mafumu omwe kwa iwo amatengedwa ngati milungu, omwe anabadwa kukhara opambana onse ndipo tsogolo lawo linali lakuti adzilamulira. Komano kwa Aisilayeli iwowatu anali kale otero, anapangidwa mu chifaniziro cha Mulungu, okhara nawo mayitanidwe a ulamuliro olamulira limodzi ndi Mulungu. Kufuna kukhara ndi mfumu inali chinthu china chowukira cholinga cha Mulungu pa iwo, komanso kukana udindo wawo opatsidwa ndi Mulungu padziko lapansi.

Sawulo, chisankho cha anthu

Chisankho chawo chinali munthu amene amawoneka ngati mulungu pamaso pawo, wantali ndi wanthanana, wankhondo mwachilengedwe, munthu amene adzawatsogolera kuchoka m'mavuto awo. Mulungu anawapereka kuchisankho chawo, anafika pomudzodza Sawulo ndi mzimu wake kwakanthawi, komabe zofooka za anthu sizikhara kutali nawo ndipo zinapangitsa kuti Mulungu akane ufumu wa Sawulo.

Davide, chisankho cha Mulungu

Zikuwonetsa kuti Mulungu ali ndi kuthekera kobweretsa zabwino kuchokera mwa kuwukira kwa anthu ake. Chisankho cha Mulungu cha mfumu sichofuna munthu okhara ngati Mulungu oposa onse koma kamnyamata ka kubusa, kamene mumtima mwake ndi komulambira Mulungu. Kudzera mu moyo wa Davide tikuwonamo mfumu imene Mulungu amkayiwona nthawi yonse. Mfumu yodzichepetsa yotumikira anthu yomwe imakonda ndi kutumikira Mulungu kaye ndipo imalemekeza iye pakulamula kwake komanso mu ulamuliro wake. Chimenechi chinali chiwonetsero cha Adamu olamura amene amatumikira ngati Mulungu mwini, ndithudi Mulungu anamulonjeza kuti wina ochokera m'banja mwake adzalamulira pampando wake wachifumu mpaka kalekale (1Mbiri 17). Ichitu ndi chifukwa chimene aneneri ambiri amkayembekezera mfumu yokhara ngati Davide, imene idzalamulire ndi chilungamo komanso molungama. Koterokudzera mwa Davide tikupezamo lonjezo la umunthu owona wa Mulungu, Yesu. Mwa Davide tikuwonamo chimwemwe ndi mtendere chimene chimabwera mwa anthu amene amadzipereka mokondwera kwa olamulira weniweni wa Mulungu.

Solomo, Adamu watsopano

Mwa mwana wa Davide, amene ali Solomo chilichonse chimkawoneka kuti chakhadzikika pakuwonekera kwa Isilayeli weniweni, otsogozedwa ndi mfumu yodzichepetsa imene ingayike Mulungu patsogolo potsogolera anthu ku chiyembekezo cha moyo wawo kukhara kuwala kwa dziko lapansi. M'malo mongodalira mzeru yake, iye modzichepetsa anampempha Mulungu kuti amuwonetse kusiyanitsa kwa zabwino ndi zoyipa ndipo anamulemekeza Mulungu mu ualamuliro wake. Kuyenderedwa ndi mfumu ya ku Seba kunawonetsera chiyembekezo chimene chimawoneka kuti chimakwanilitsidwa, pamene mitundu imkabwera kudzaphunzira ndi kuwona chimene Mulungu ali.

Nkhani yakale yomwe ija

Ngakhare kuti panali lonjezo la tsiku latsopano la anthu a Mulungu, ndi cholinga chatsopano cha kuwonetsera Mulungu mowona kudziko lonse lapansi koma tikuwona

kuti; onse Davide ndi Solomo ali ndi zofooka zazikulu. Davide anagwa nalo yesero la 'kuwona' ndi 'kutenga' chimene amkachikhumbira, zimenezi zinamugwetsera mu chigololo, kupha ndi mavuto a m'banja amene adzamuwononge Davide kwambiri. Naye Solomo anapezeka kuti yesero logwera mu kupembedza mafano linali lovuta kwa iye kuti alikane, ndipo zimenezi zinapangitsa kuti pakhare kumuwukira Mulungu ndi kuwapondereza anthu. Mapeto ake ufumu unagawikana ndipo zinapangitsa kuti mitundu ya kumpoto isokonekere ndi kutengedwa kupita ku ukapolo ku mayiko. Chiyembekezo cha mtundu wa anthu, ngakhaleenso cha dziko lapansi tsopano chili mu bwinja.

Nyimbo, mzeru ndi uneneli

Ngakhare kuti anali olephera, awiri onse Davide ndi Solomo anasiya chuma chamtengo wapatali cha nyimbo ndi mzeru zomwe zinapangitsa kusintha miyoyo ya anthu m'mibado yotsatira pambuyo pawo. Ndipo ngakhare lero ndakatulo za Davide zimalimbikitsa nyimbo zathu pamene tikupembedza Mulungu, mzeru ya Solomo imatithandizira kumvetsetsa m'mene tingakwanitsire kukhara m'moyo uno komanso zolembe zawo zatithandizira kuzindikira iye amene Mulungu analonjeza kuti adzabwera ndi kukhara mapeto a nkhani yonse ya Mulungu; Yesu mfumu yeniyeni.

Funso lokambirana: kodi tingagwiritse ntchito bwanji zolembe za mzeru pamene tikuwalalikirira anthu?

4.4 – Isilayeli – Aneneri ndi chiyembekezo

Anthu amene Mulungu anawayitana kuti akhare ufumu wa ansembe alephera kukhara osiyana ndi a kudziko, akukhara moyo opembedza mafano, kuponderezedwa komanso pansi pa mphamvu ya tembelero. Munthawi imeneyi ndi pamene Mulungu anawukitsa azimuna ndi azimayi kuti abweze Isilayeli kukhara chenicheni chimene Mulungu anamuyitanira.

Udindo wa mneneri

M'malo mongoloseza za mtsogolo (nthawi zambiri timasokonezeka nazo izi) aneneri amene Mulungu anawabukitsa anali ngati oyimira mulandu yokhudza mgwirizano, kuwalozera anthu a ku Isilayeli ku chipangano chimene anachita, ndi kuwazindikiritsa mavuto amene angawagwere ngati angapitilize kuwukira kwawo. Koteri Eliya anachenjeza kuti mvula siigwa, Yesaya anawachenjeza zokhudza ankondo amphamvu a ku Asiliya. Yelemiya anawachenjeza kuti Ababeloni atsara pang'ono kuwakantha. Aneneri onsewa akungowerenga kuchokera mu chilamulo cha Mose ndi kusankhamo malo ofunikira amene Mulungu amkawawonetsera pamene Isilayeli amkayendelera kupembedza mafano ndi kupondereza ofooka amene anali pakati pawo. Komabe mkatikati mwa kunenera kwawo, Mulungu analukiramo mapulani ake aakulu a dziko lapansi, makamaka iye amene adzabweretse ulamuliro wake ndi mdalitso wake ku mitundu yonse ya anthu.

Undende

Mutuwu sunatalikanepo nafe munkhanimu, ndipo pamenepa tikuwona zotsatira zake zonse. Isilayeli sanakhulupilike ku chipangano, ndipo choyamba Asiliya, kenako anthu a ku Babulo anabwera ndi kuwatenga anthu kuwachotsa mdziko la malonjezano Iija. Ngakhalenso kachisi, malo a kupezeka kwa Mulungu anawonongedwa. Ezekiyele anawona kupezeka kwa Mulungu kukuchoka mkachisi ndipo Yelemiya anawona undende wa ku Babulo akutha zaka 70. Tsono Daniyele anawonetsera mmene munthu angakhalire okhulupirika pamene iye anali ku undende mu dziko la eni magawo onse; kudzipereka kwake kwa olamulira komanso kusunga miyambo yawo.

Kubwezeretsedwa

Chinthu china pambali pa machenjezo a chiwonongeko chinali masomphenya a aneneri okhudza kubwezeretsedwa komanso nthawi ya kupangitsa zinthu kukhara zatsopano, pamene Isilayeli adzabwererenso pamalo ake mu zolinga za Mulungu ndi kulamulira mayiko. Yesaya akunenera zokhudza Mfumu Sayilasi yomwe ikubuka mkudzamanganso Yelusalemu, izi ndi ndendende momwe zinachitikira. Hagayi ndi Zakaliya analumikizitsana ndi Ezara ndi Nehemiya kuwalimbikitsa iwo amene anabwera kuchokera ku undende kumanganso mzinda komanso kubwezeretsa kachisi. Komabe kubwezeretsedwa komwe anthu amayembekezera sikunathekebe, ndipo tikuwona chipangano chakale chikutha ndi mneneri Malaki akulira kudandawula nkhani ya mavuto akale omwe aja okhudza mafano ndi kuponderezana.

Chiyembekezo

Ngakhare kuti panali mavuto amene Isilayeli amakumana nawo, panali mlozo wa chiyembekezo umene iwo anayendelera kuwukakamira. Mneneli Daniyele anawona ma ufumu anayi akubuka amene adzapondereze Isilayeli ndipo ukazadza ufumu wachinayiwo ndi pamene ufumu wa Mulungu udzabweredi ndi kulamulira. Anawona zaka 70 za undende, ndipo padzakhaladi zaka 70 kuchulutsa ndi 7 kuti zikhare chiyeretso ku choyipa.

Ndipo zaka 490 zotsatira, panthawi ya ulamuliro wa ufumu wachinayi, chiyembekezo chimkakulirakulira kuti Mulungu akuchitanso chinachake, ndiponso kuti ufumu wake watsara pang'ono kukhadzikitsidwa. Mulungu akhoza kuchitano zomwe anachitapo m'buyomu ndi kumasula anthu ake undende wawo ndi kuwabwezeretsa iwo kukhara mtundu umene udzakhare mdalitso ku dziko lonse. Zichitochito zayikidwa m'malo.

Ntchito yofunika kulemba: Kodi Ayuda amkayembekeza chani munthawi ya Yesu komanso ndi chifukwa chani zimakhara chomcho?

5.1 – Yesu – Mfumu ilimkudza

Pulani ya Mulungu yofuna kuyanjanitsa dziko lapansi kwa iye mwini kudzera mu banja ikuwoneka kuti yalephereka, pamene anthu a Isilayeli akuvutika kuti akwanilitse mayitanidwe awo okhara kuwala kwa dziko lapansi. Komabe, monga tawonera munkhani tangomaliza kumeneyo, chiyembekezo chakuti Mulungu watsara pang'ono kuchita chatsopano chinayambapo.

Pali milozo itatu ya chiyembekezo pakati pa Ayuda a mu zaka 100 zoyambilira:

Mesiya – Iye amene adzabweretse ufumu wa Mulungu ndi kugonjetsa adani onse.

Otumikira – Munthu amene adzathane ndi ntchimo lomwe linapangitsa kuti anthu atengedwe kukhara mu undende pansi pa anthu achilendo.

Mulungu mwini – chiyembekezo chawo chakuti Mulungu adzabweleranso ku kachisi ndi kubwezeretsa malo awo kukhara olamula pakati pa mitundu.

Kuwerenga kwawo kwa Buku la Daniyele kunawapangitsa iwo kukhulupilira kuti Mulungu anali atatsara pang'ono kubweretsa ufumu wake pa dziko ndi kugwetsa ma ufumu ena onse a dziko lapansi.

Mabuku onse a Uthenga wabwino onse analembedwa olembayo ali ndi chiyembekezo chimenechi m'malingaliro ake, buku lililonse likukamba makambidwe ake ake kuti Yesu ndi kukwanilitsa kowona kwa chilichonse chimene iwo amkachiyembekeza. Tiyeni tiwone mayambiliro a buku lililonse la uthenga wabwino kuti tithe kuwona mmene olembawo akufotokozera nkhanayi mu njira zawo zosiyanasiyana.

Mateyu

Mndandanda wa mibadwo – Mateyo akuyamba nkhani yake ndi mbiri ya mndandanda wa makolo a Yesu, akukambamo za Abulahamu komanso Davide ngati anthu ofunikira mu mndandandawu. Iwowa ndi makolo awiri amene ananyamula malonjezano a Mulungu okhudza zidzukululu zawo ndipo akutenga gawo lofunikira kwambiri mu nkhani yokhudza Isilayeli.

Mayina – Mateyo anawonetsetsa mayina a Yesu, amene anali ofunikira mu dziko la Ayuda. Loyamba ndiye dzina lakuti Yesu, likuwonetsera cholinga chake chowamasula anthu ku machimo, zomwe zikuwonetsera mbali zonse za Mesiya komanso kutumikira kwake. Lachiwiri ndiye Imanuweli, lochokera mu mawu a uneneri wa Yesaya amene amawonetsera poyera kuti iye ndi 'Mulungu nafe.'

Mitundu – Nkhani yoyamba ya Mateyo ikukamba za amzeru achifumu amene anachokera kummawa kubwera kudzapereka ulemu kamba ka kubadwa kwa mfumu yatsopano ya Isilayeli, kukumbutsa kuti lonjezo la Mesiya linali lokuti iye adzakhara mfumu padziko lonse lapansi.



Maliko

Chiyambi – Maliko sanataye nthawi koma kufotokoza kuti kodi Yesu ameneyu ndi ndani pakunena kuti iye ndiye Mesiya, mwana wa Mulungu.

Wamthenga – Anakambanso za gawo limene Yohane m'batizi anatenga polambula njira ya Yesu, pogwira mawu amene analankhula Yesaya ndi Malaki kuti onsewa akulonjeza za munthu yemwe adzabwere kudzakonza njira Mulungu mwini asanabwelere ku Yelusalemu.

Umboni wa Atate – Maliko anachita changu kubweretsa nkhani yokhudza liwu la Mulungu lotsimikiza za Yesu kunena kuti, 'Mwana wanga, yemwe ndimamukonda. Mwa iwe ndikondwera.' Kuwonetsera malo amene analowa Yesu kukhara Isilayeli weniweni, iye amene anamusangalatsa Mulungu.

Uthenga wabwino – Maliko akufunistsa kuwapangitsa owerenga ake kuti adziwe uthenga wa uzimu 'uthenga wabwino' umene unali ndi china chake chofunika mwapaderadera munthawiyo, chimene chimatanthawuza 'uthenga wabwino wa mfumu yatsopano'.

Luka

Olowa ufumu wa Davide – Luka akukamba za kuyenderedwa ndi angelo pakulengeza kwa Maliya kuti mwana wake adzakhara olamulira wa nthawi zonse mu ufumu wa Davide mpaka kalekale, ndipo nyimbo ya Maliya inakamba za mmene ufumuwu udzawagwilire mkono osawuka ndi osowa.

Umboni wa angelo – Angelo analalika kwa abusa a nkhoa kuti 'Mpulumutsi' komanso kuti 'Mesiya ambuye' wabadwa ku Yelusalemu.

Lero – Luka akulemba za chiphunzitso choyamba cha Yesu, pamene anatenga mawu ochokera mu Yesaya 61 okamba za chaka cha mamasulidwe akulu a Mulungu, pamene ufulu ndi kubwenzeretsedwa kumafika kwa onse ndipo analengeza kuyamba kwake kwa zimenezi kuchokera tsiku limenelo.

Yohane

Mawu – Awerengi a Chigiliki a buku la Yohane anakamvetsetsa mwanthawi yomweyo pamene iye anagwiritsa ntchito mawu akuti 'mau', mphamvu ya kupereka moyo ya dziko lapansi, mlengi wa zonse ndiponso kunena kuti anasandulika thupi ndi kukhara pakati pawo. Mulungu mwini wake anabwera kwa anthu ake.

Mulungu mwana – Iye amkawonetsera Mulungu, kuwonetsera kwa anthu onse cheni cheni chimene iye ali.

Nkhosa ya Mulungu – Yohane akulumikizansitsa mwana wa nkhoa wa Paska ndi Yesu kuyambira kumayambiliro, iye amene adzaliwombole dziko lapansi ku mphamvu za ntchimo.

Funso lokambirana: Kodi mu nkhani yabwino kapena kuti uthenga wabwino malingana ndi momwe Yesu amkanenera mu buku la Maliko 1: 14 mpaka 15 muli zotani?

5.2 - Yesu – kukonzedwanso kwa Isilayeli

Yesu anafika mu zochitikazi mwa mphamvu, akulengeza nkhani yakuti ulamuliro wa Mulungu wafika, ndi kuwonetsera mmene ufumuwo umawonekera, kudzera mu kuchiritsa odwala, kumasula ogwidwa ndi ziwanda komanso kuwaphunzitsa anthu zokhudza ufumu omwe uli mkudza. Mwachidziwikire, zimenezi zinapangitsa kuti pakhare mafunso ochuluka pakati pa anthu. Kodi ufumuwu udzakhara otani? Kodi anthu adzidzachita motani? Kodi ndi ndani adzakhoze kukhara gawo limodzi ndi ufumuwo? Olemba uthenga wabwino akuthandizira kuyankha mafunsowa potiwonetsera m'mene Yesu anafikira kudzakhara opitiliza ndi okwanilitsa nkhanayi kufika pamepa.

Isilayeli weni weni

Yesu akuwoneka kuti akuyiyambiranso nkhani yokhudza Isilayeli. Kuyambira nthawi ya ubatizo, pamene Mulungu anasimba za iye kuti ndi mwana wake (mau amene amatchulidwa nawo Isilayeli mmbuyomu), iye anatuluka m'madzi ndi kutengedwa kupita kuchipululu kwa masiku 40 kumene anakumana ndi mayesero. Kuchokera kuchipululuko anakwera kupita pa phiri ndipo pamenepo anaphunzitsa katanthawuzidwe ka iye ka madalitso ndi matembelero. Kenako anasankha ophunzira 12 amene akhare omutsatira, a chifupi naye. Chilichonse mwa zochitikazi ndi chozindikilika kufuma mu nkhani ya Isilayeli. Yesu anali akukonzanso Isilayeli, iye anapambana m'madela amene Isilayeli analephera. Iye anali okhulupilika ku chipangano pamene Isilayeli anali osamvera.

Yesu anazizimutsa anthu amene akuwatchula kuti ndi gawo limodzi la Isilayeli watsopano, anasankha anthu otayika, anthu ochimwa odziwikiratu, anthu osaphunzira ndi anthu okonda ndale ndipo anawakana atsogoleri a chipembedzo.

Kachisi weniweni

Olemba wa uthenga wabwino, Yohane analunjika makamaka pa Yesu pomukamba kuti ndi malo amene kumwamba ndi dziko lapansi zimakumana, kachisi weniweni. Mau anasandulika thupi ndipo anakhara pakati pathu (Yohane 14:6). Iye anali njira, choonadi ndi moyo. Palibe yemwe amafika kwa Atate ngati sadzera mwa iye (Yohane 14:6). Chimene kachisi wakhara akupanga kwa nthawi yayitali tsopano Yesu akuchichita. Amathanso kulengeza kukhululukira machimo zimene zinali zotheka kudzera mu nsembe za ku kachisi zokha. Pamene Yesu anafuula ndi mawu okwera kuti, 'Ngati alipo amene ali ndi ludzu, muloreni adze amwe.' (Yohane 7:37) Iye ankakamba za chithunzithunzi cha kachisi mu Ezekiyeli 47 amene anali ndi madzi amoyo oyendelera kuchokera mkati mwake.

Sabata lenileni

Machiritso ambiri a Yesu ndi kumasula kwake kumachitika pa Sabata, zimene zimapangitsa kuti adzitsogoleri a chipembedzo akwiye. Komabe kwa iwo amene anali ndi maso akupenya iye amkalengeza kwa iwo chinthu chofunikira kwambiri. Sabata linali litafika mwa munthu. Zonse zimene Sabata limayenera kukamba, kupuma kutchito zonse (Tsiku la Sabata) kumasulidwa kwa akopolo (chaka cha Sabata), kukhululukira ngongole zonse komanso kubwezeretsedwa kwa malo amene analandidwa (chaka cha Jubili) zimkalodzera kutchito ya Yesu. 'Ngati wina wa inu wathodwa adze kwa ine ndipo ndidzamupumulitsa', Yesu anatero. Sabata nthawi yonseyi linali chikwangwani cha ntchito za Yesu.

Chilamulo chenicheni

Akhilisitu ambiri amasokonezeka ndi chilamulo makamaka akamamva zimene Yesu analankhula kuti palibe liwu ngakhare limodzi la mu chilamulo limene lidzachoke mpaka 'chilichonse chitakwanilitsidwa' (Mateyo 5:18) magulu a zikhulupiliro za chikhristu akhadzikitsidwa pa machitachita a kusunga chilamulo monga mmene malamulo khumi anakambira mwachidule pomasulira ndime zimenezi. Chenjezo la Yesu lakuti 'pokhapokha kulungama kwanu kutaposa kwa Afalisi, ndithu sungathe kulowa mu ufumu wakumwamba,' zapangitsa ambiri mwa akhristu kukhara odzitsata kwambiri kuposa afalisi tikakamba nkhani ya chilamulo, pang'onopang'ono akubwelera ku chipembedzo cha Chiyuda. Zimenezi zitipangitse kubwelera pambuyo ndi kufunsa chenicheni chimene Yesu amkatanthawuza mu ndimezi.

'Musaganize kuti ndabwera kudzathetsa chilamulo kapena uneneri; sindinabwere kudzathetsa zimenezo, koma ndabwera kudzakwanilitsa'. (Mateyo 5:17). Iyi ndi vesi lofunika kwambiri. Tiyeni tiyambe kaye ndi aneneri monga chotithandizira kuzindikira chimene Yesu amatanthawuza. Mawu a mu chipangano chakale anadzadzandi mawu a aneneri' amene akukwanilitsidwa mwa Yesu. Ambiri mwa mawuneneri amenewa akhoza kumasulilidwa bwino tikamawona kuti kukwanilitsidwa kwake kuli m'moyo wa Yesu. Isanafike nthawi imeneyo, timakhoza kumakhara tikudabwa kuti kodi mawuwa akutanthawuza chani kweni kweni kapena ngati mawuwa analidi a uneneri. Ndi pokhapokha tikawawona akukwanilitsidwa mwa Yesu ndi pamene timatha kuzindikira zomwe amatanthawuza.

Tsopano tiyeni tiwone gawo la nkhani ya chilamulo. Mamvekedwe ake okhare chimodzimodzi ndiye zitithandiza. Chilamulo chimapereka malamulo osiyanasiyana a makhalidwe komanso chikhalidwe, koma ndi pokhapokha tikawawona akuwonekera mwa Yesu ndi pamene timamvetsetsa zomwe akutanthawuza. Zimenezi ndi zimene zimapangitsa kuti Yesu adzitha kuwasanthulira kamvedwe ka chilamulo. "Munamva kuti kunanenedwa... koma ndikuuzani " Yesu akukonza mmene ifeyo timawamvera malamulo ndikupangitsa kuti tiwonemo iye mwini. Amkawonetsera zenizeni zimene malamulowo amatanthawuza. Ichitu ndi chifukwa chomwe Yesu mwiniwake amatha kuwomba mkota mawu a chilamulo mosavuta, 'monga kukonda Mulungu ndi kukonda ena' chimenechi ndi chomwe chinali khumbo lake lalikulu lomwe linali muuni mu

ziphunzitso zonse zimene amawaphunzitsa anthu amene amamutsata, komanso zonse zimene iye amachita. Yesu ndi amene anali chilamulo chenicheni, kuyitanidwa kwake sikunali kokuti athane nalo lamulo koma kuti awonetse zomwe malamulo amalozera, ndi kukhalamo mu chilamulocho mokwanira kudzera mu chikondi, kuchita chifundo, kupemphera komanso kutumikira.

Modabwitsa, kupezeka m'moyo kwa Yesu zinali chipwilikiti. Ena amkazikonda zomwe iye amalankhula ndipo amkazichita, ndipo anachilandira chiphunzitso chake. Ena amkamutenga kukhara chiwopyezo ku zikhulupiro zawo zimene anazigwiritsa kwa nthawi yayitali ndi mawudindo.

Funso lokambirana: Kodi ndi chifukwa chani Yesu amadedwa kwambiri ndi atsoholeri a chipembedzo?

5.3 – Yesu – Ziphunzitso ndi machenjezo

Iyi ndi nthawi yofunikira kwambiri mu mbiri ya Isilayeli, nthawi ya kutembenuka kwa zinthu. Malonjezano onse amene akhara nawo chiyambire amafikano pokwanilitsidwa. Chinachake chimachitika mu m'badwo wawo chimene chiwakonzenso anthu amene Mulungu anawasankha kuti afikitse mdalitso wake kudziko onse, komano anthuwa makamaka adindo amakana kumuvomereza Yesu kapena uthenga wake.

Yesu amkawaphunzitsa iwo kudzera m'mafanizo

Nthawi zambiri timaganiza kuti Yesu amagwiritsa ntchito mafanizo kapena nkhani zimene zingawonetse mfundo imene iye amaphunzitsa, kapena kulithandiza gulu kuti likumbukire mau ake. Zoonza zake ndi zotsemphana kwambiri ndi zimenezi. Ophunzira ake anayamba amufunsapo chifukwa chimene iye amakondera kuphunzitsa m'mafanizo, ndipo pakuyankha zimenezi iye anagwiritsa ntchito zomwe Yesaya ananena, “Mudzakhara mukumvabe koma osamvetsetsa” (Mateyo 13:14). Ziphunzitso za Yesu zinali zothuvuka komanso zowukira. Amkayambitsa mavuto mosavuta kulikonse kumene amapita, akulankhula momwe anachitira polankhula za ufumu watsopano komanso mfumu yatsopano ikubwera kwa anthu ake. Iye amkagwiritsa ntchito mafanizo pofuna kuzembayitsa zomwe amafuna kunena ndi cholinga chakuti mu ziphunzitso zake zomwe amaphunzitsa poyera okhawo amene anali ndi makutu akumva amumvetsetse iye apo bii anakagwidwa m'mawa omwe.

Chimenechi ndi chimodzi mwa mafungulo othandizira kumvetsetsa ziphunzitso za Yesu, kwenikweni zimakhudza anthu amene iye amkalankhula nawo, malingana ndi malo amene amapezeka. Mukangomvetsetsa zomwe zimatanthawuza kwa iwo mukhoza kuyamba kuganizira m'mene mungazigwiritsire ntchito m'moyo wanu kapena wa iwo amene mukuwaphunzitsa.



Mwachitsanzo tiyeni tiyiwone nkhani yodziwika bwino ya mwana osochera yomwe ikupezeka mu buku la Luka 15. Ambiri mwa ife talimbikitsidwapo chifukwa cha chikondi cha tate uja pomulandiranso mwana wamng'ono owukira uja. Ena anaganizira gawo la mwana wamkulu uja munkhaniyi. Chimene tingaphonye ndi malo amene Yesu akupezeka pophonzitsa chiphunzitsochi. Iwe wazisonkhanitsira gulu lalikulu, komanso walankhula zinthu zovuta zokhudza dipo lomutsata iye (Luka 14: 26 – 33) panali chiwopsyezo chakuti sangamulabade kapenanso akhoza kumukana, (Luka 14: 24 -25). Panalinso kasakaniza wa anthu 'ochimwa'amene amamumvera mwachidwi komanso afalisi akumutsutsa iye, Yesu anawawuza nkhani zitatu zokhudza chinthu chimene chinasowa ndipo chinapezekanso, zomwe zinali zosangalatsa kwa mwiniwake. Ndi zosakayikitsa kuti zimenezi zimakamba za iwo amene anali otayika mu Isilayeli, amene anali atapambuka kapena kukana pulani ya Atate pa iwo ngati mtundu. Yesu amakamba momveka bwino kuti mwini anthuwo akufinitsitsa kuwapeza iwo, pamtengo wawukulu kwambiri. Nkhani yake yomaliza ili ndi kusintha, pamene tikumuwona mwana wamkuluyo amene anatsara ndi bambo ake akukwiya chifukwa chakuti mng'ono wake wabwera ndipo anakana kukadya nawo phwando. Izizitu ndi zachidziwikire kuti chinali chidzuzulo kwa afalisi amene amadana ndi kuphatikizidwa kwa ochimwa amene Yesu amasonkhanitsa, nawonsotu ndi osochera ndipo ali kunja kwa phwando koma atate amawayitana iwo kuti akakhare nawo. Yesu anayiyenjekeza nkhaniyi m'malele posapereka mathero ake. Tikakhara kuti tikutha kumvetsetsa nkhani yomwe yamanga nthenje munkhani timakwanitsa kuwona zimene Yesu amaphunzitsa komanso kuti ndi chifukwa chani amaphunzitsa, tsopano tikhoza kuyamba kuzukuta zomwe zimenezi zikutanthawuza kwa ife komanso ku magulu a anthu amene Mulungu akuwasonkhanitsa pamodzi, komanso kuwopsya kwa kuwayang'anira pasi anthu ena.

Yesu anawachenjeza Aisilayeli

Tsopano pakuti tamvetsetsa ubwino oyang'ana pamene nkhani ikuchokera tikhozano kulingalira za ena mwa machenjezo a Yesu kwa Ayuda. Zimenezi ndi ndime monga Mateyo 24, Maliko 13 ndi Luka 21. Ndime zimenezi nthawi zambiri zimakhara ndi mitu monga, 'Zizindikiro za kumapeto kwa nthawi', zimene mwachidziwikire zimatipangitsa kuti ife tidziganiza kuti Yesu akukamba za kumapeto kwa dziko. Komano tiyeni tiwonenso pamalo pamene pakuchoka nkhani.

Tawerengani Maliko 13

- 1) Kodi funso limene Yesu akuyankha ndi liti? (muwone vesi la 4)
- 2) Kodi mapeto amene iye akukamba mu vesi la 7 ndi ati?
- 3) Kodi ndi mlozo wanji wa nthawi umene Yesu akupereka ku zinthu zimene iye akuzikamba? (Tawerengani vesi la 30)
- 4) Kodi Yesu akukamba zochokera pati mu vesi 24 mpaka 25? Kodi pamenepo pakukambidwa nkhani zotani?
- 5) Mu vesi la 26, kodi Yesu akutenga mawu ochokera pati? Pali pali zotani pamenepo?
- 6) Kodi mukuwona kuti Yesu pamenepa akukamba zokhudza chani?

Funso lokambirana: Kodi zikutanthawuza chani zakuti Yesu adzawabatiza anthu ndi Mzimu Oyera komanso ndi moto (Mateyu 3:11)?

5.4 - Yesu – Kupachikidwa pamtanda

Imeneyi inali nthawi imene inali m'malingaliro a Yesu nthawi zonse, kunali kukwanilitsa kwa nkhani imene wakhara akuyikhadzikitsanso. Gawo lake lokhara monga wantchito, Mesiya komanso Mulungu zonsezi zikudza pa iye mu chinthu chochitika chimodzi chodziperekachi. Ngakhare kuti Ayuda amkayembekeza zonsezi iwo sanayambe aganizirapo zakuti zidzakhara mwa munthu mmodzi.

Otumikira

Yesaya anamuwona Isilayeli kukhara wantchito wa Mulungu. Obweretsa kuwala kwa amitundu. Komabe zikuwoneka kuti iye amamuwona wantchitoyu kukhara munthu mmodzi iye amene anavutidwa mosalungama, ndipo anadzitengera kulakwa kwa dziko lapansi, ngati mmene zimakhallira patsiku la mwambo ochotsa machimo, mbuzi imkachotsa machimo, kuwachotsa pakati pa anthu motenso wantchitoyu amayenera kuchotsa machimo, mazunzo ndi matenda ndi kuvutika mumtima kwa anthu, ngakhare mu zaka zonse za chizunzo Isilayeli sanakwanitse kuchotsa uchimo. Amafunikira wantchito amene adzawatenge machimowo kuwachotsa pakati pawo mmalo mwa iwo. Yesaya analosera kuti wantchitoyo adzawona mapeto a ntchito yake ndipo adzakhutitsidwa. Mathero a tchimo, manyazi, matenda, chisoni ndi kuvutika.

Mesiya

Yesu anasankha mwambo wa Paska kuti alankhule za tanthawuzo la imfa yake. Chipulumutso chimene iye amabweretsa chimatanthawuza kumasulidwa kwakukulu kwa anthu ake, pamene iye analimbana ndi kugonjetsa zimphamvu zimene zinaliyika dziko mu ukapolo. 'Tsopano kalonga wa dzikoli athamangitsidwa' (Yohane 12:31). Iye anadziwonetsera kwa anthu mu dzina la nkhoa yamphongo imene mwazi wake unakhetsedwa ndi cholinga chokuti chigamulo cha dziko lapansi chodza malingana ndi kuwukira chiwafikire anthu amene ayika chikhulupiliro chawo mwa iye. Anakonzanso zikhulupiliro za zaka zachikhalire za miyambo yomwe imachitika pa chakudya cha pa Paska. Mmalo mwakwe anayikiza thupi ndi mwazi wake kukhara choyenereza. Omutsata ameyenera kugwiritsa ntchito chakudyachi kuti akumbutsane m'mene Yesu anawonongera mphamvu ya tchimo, imfa komanso oyipayo, ndi kukhazikitsa pangano latsopano limene Mulungu anapanga ndi anthu ake ndi cholinga chakuti achotse tchimo lawo ndi kulemba malamulo ake m'mitima yawo. (Yelemiya 31: 32 -34).

Kulongedwa

Yesu anayiwona nthawi imeneyi kukhara nthawi ya kukwezedwa. 'Ola lafika lakuti mwana wa munthu akwezedwe' (Yohane 12:23). 'Koma ine ndikadzakwezedwa, ndidzadzitengera anthu onse kwa ine' (Yohane 12:32). Mau amene Yesu anagwiritsa ntchito ponena kuti, 'kukwezedwa' ndi omwe amagwiritsidwa ntchito polonga ufumu. Umu ndi mmene Yesu amkakuwonera kupachikidwa kwake pamtanda, njira imene ikumpangitsa iye kupatsidwa dzina loposa mayina onse. Amene analemba uthenga wabwino anakamba zambiri za ichi. Akupeleka gawo lalikulu la chidwi chawo ku

kuwomba mkota zokhudza kupachikidwa pamtandako. Iwo akukamba kwambiri za mmene zichitochito za Aloma zomwe anachita pomuwonetsera Yesu kukhara mfumu, anamuveka iye zovala zapepo, anamuyendetsa m'misewu ya m'mizinda mwachipambano. Zoona zenizeni sizinasunthike mwa iwo, pamene iwo akuwona zimene olamura aliyense wa dziko lapansi wa nthawi imeneyo sanathe kuziwona, zakuti kumeneku kunali kulongedwa kwa Yesu kupita mu ulemelero. Yesu mwini wakeyo amkadziwa, anazivomereza, ngakhare kuti kafedwe kake tikatengera mu umuthu kunali kochititsa mantha. Ameneyu anali Yesu kubwera kudzalamulira. Ameneyu anali Yesu kuwonetsera zimene ulamuliro wake udzawonekere. Yesu anawayitanira otsatira ake kuti achite mofanana, anyamule mitanda yawo potsata chitsanzo chake, ndipo ndikukhara olamura mu njira yake yomweyi.

Zaka zotsatira pa moyo wa mpingo unakumana ndi zopinga zochuluka ndi kutayika kwa zinthu koma pambali pa zimenezo, chilimbikitso chachikulu, kulimba mtima kwakukulu, ndi kupita chitsogolo kwa ufumu wa Mulungu pamene ophunzira a Yesu anayamba kutsata zochita za Yesu, anapereka miyoyo yawo, pakumvetsetsa kuti kudzera mu zichitochito zimenezi, ulemelero wawukulu udzakwanilitsidwa.

Zochita: Kodi ndi chifukwa chani Yesu amayenera kufa?

6.1 – Kulengedwa kwatsopano – kuwukitsidwa kwa Yesu

Kumapeto kwake tafikano ku mathero a nkhani. Chiyembekezo chimene chinalipo kuzungulira Mesiya amene Ayuda amamuyembekeza, zodabwitsa zake ndi zakuti chinakwanilitsidwa mwa Yesu. Chiyembekezo china pakati pa Ayuda chinali chakuti pamapeto a nthawi Mulungu adzachitapo kanthu kuti alibwezeretse dziko kukhara loyenera. Nthawiyo ikadzafika anthu olungama adzawukitsidwa ndipo Mulungu adzabweretsa chilengedwe chatsopano chomwe chidzakhare ndi kumwamba kwatsopano komanso ndi dziko lapansi latsopano.

Kuwukitsidwa kwa Yesu

Yesu mwiniwake amkanena mosabisa zokhudza zimene zidzachitike. Malemba anali odzadza ndi zithunzithunzi za masawuko ndi kukwezedwa. Ophunzira eni akewo amkayembekeza kuwukitsidwa kwa onse patsiku la chiweruzo chomaliza. Komano chokhumudwitsa kwa iwo chinali chakuti, Yesu anawukitsidwa mkukhara ndi moyo mkatikati mwa mbili. Kulengedwa kwatsopano kwayambika mkatikati mwa chilengedwe chakale.

Thupi lowukitsidwa

Ndife okondeledwa kuti tili ndi kachidutswa ka chizindikiro cha mmene chilengedwe chatsopano chidzakhaliye polingalira za thupi la Yesu owukitsidwayo. Apatu tikuwona kachiduswa kwa mapeto a nkhani. Miyamba ya kuthupi ndi ya uzimu kumapeto kwake yalumikizana pamodzi. Palibe chikayiko chilichonse chakuti thupi la Yesu

linali la kuthupi, ophunzira ake anamugwirapo, anadya naye, anaziwona zipyera za kupachikidwa kwake pamtanda. Komabe iyeyo analinso ku uzimu. Zimawoneka kuti amatha kuwonekera ndi kusowa mmene angafunire, amatha kuwayendera ophunzira ake iwo atadzitsekera mu chipinda, amatha kusowa ophunzira ena onse akuwona. Nthawi zina amatha kuzizimbayitsa mwakuti anthu amalephera kumuzindikira kenako mkuwalora ena kuti amuzindikire. Kudzera mu thupi la Yesu tikutha kuwonamo chithunzithunzi cha momwe matupi athu adzakhaliira (1Yohane 3:2), komanso mmene chilengedwe chonse chidzakhaliira (Aloma 8:21). Ifetu sitili ndi tsogolo mu thupi lopanda mawonekedwe koma la kuthupi ndithu ku dziko lowoneka ndi maso. Matupi athu adzafanana ndi omwe tili nawo panopa. Adzidzatha kutizindikira ndiponso tikhozanso kudzakhala nazo zina mwa zipsyera zimene tili nazo moyo uno. Komabe zipsyerazo zidzasinthika ndipo chachikulu ndi chakuti zidzakhara ndi ulemelero, ndipo dzidzapangitsa kuti pakhare chifukwa chinanso chotamandira. Mwanjira ina, chithu chilichonse chidzasinthika. Chiwalo chilichonse chimene chinawonongeka ndi tchimo komanso kuwukira chidzakhara chitakonzedwa, chitawomboledwa ndi kusinthika kukhara mu cholinga chake chenicheni.

Kukwera kwa Yesu

Luka anafotokoza kuti pambuyo pa mawu ake omaliza kwa ophunzira ake, mtambo unatsika pa iye ndi kumuphimba kuti iwo asamuwone. Iyi ikuwoneka ngati nthawi ya Daniyele 7, pamene mwana wa munthu anatengedwa kumka mmitambo kukayandikira mpando wa chifumu wa iye wa masiku akale. Inali nthawi imeneyi imene kumapeto kwa zonse Yesu anapatsidwa ulamuliro wake limodzi ndi mpando wachifumu wa Mulungu Atate, mitundu yonse ikupereka malambiro ndi kugonjera kwa iye.

Ndi nthawi yake koma sizinati

Izi ndi zofunika kuzimvetsetsa mu chipangano chatsopano, chomwe chikuyesetsa kuti chimveke pa mfundo yakuti Yesu wakwezedwa kuyikidwa malo olemekeseka kwambiri mu dziko lonse komanso wapatsidwa ulamuliro onse, komabe, panthawiyitu panangokhara Ayuda owerengeka amene anazikhulupiliradi zimenezi ndi kuchitapo kanthu ngati kuti mfumu yatsopano yakhadzikitsidwa. Kwa wina aliyense padziko lapansili zinthu zimkapitilira kuchitika mmene zimakhaliira ngati kuti palibe chomwe chachitika. Pawulo anatenga nthawi kulongosolako za zimenezi mu buku la Akolinto 15:25 'Pakuti iye akuyenera kukhara nawo ulamuliro mpaka atawayika adani ake onse pansi pamapazi ake'. Zoona zake ndi zokuti Yesu akulamulira ngakhare panopa, ngakhare kuti anthu ambiri ndi mawukulu savomereza kapena kudzipereka ku ulamuliro wake. Komabe ngakhare mkatikati mwa chiwukiro cholimbana naye, 'iyeyo akukwanitsabe kupangitsa kuti zinthu zonse zigwire ntchito mu umodzi kuti zichitire ubwino kwa iwo amene amamukonda.' (Aloma 8:28). Ulamuliro wake ungokulirakulira, pamene anthu ochulukirachulukira akudzipereka kwa iye mokondwera. Iye monga anthu ake tili nawo mwayi opemphera ndi kuchita zinthu kuti tibweretse zochuluka ku ulamuliro wake padziko lonse lapansi, mpaka kumapeto kwa zonse iye atadzabweranso ndi kusintha chinachilichonse ndipo chisoni chilichonse chidzakhara bodza' (JRR Tolkien).).

Funso lokambirana: Kodi kuwukitsidwa ndi kukwezedwa kwa Yesu kupita kumwamba kukukwaniritsa chani mu nkhani za m'bayibulo?

6.2 - Chilengedwe chatsopano – kutumizidwa kwa Mzimu Oyera

Isilayeli analephera mayitanidwe ake okhara oyimira Mulungu chifukwa chakuti iwo anali mbali imodzi la vuto mmalo mokhara gawo la mayankho. Iwo anali nawo malamulo, mapangano, kachisi, aneneri ngakhaleenso ndi chidwi chawo chonse, panalibe chimene chimasowa mwa iwo kuti akwanilitsedi kubweretsa dalitso la Mulungu ku dziko lapansi.

Kupachikidwa kwa Yesu kumatanthawuza kuti dipo la kuyipa konse laperekedwa, undende unali utathetsedwa, komanso tchimo, imfa ndi oyipayo sizinalinso ndi ulamuliro.

Kuwukitsidwa kwa Yesu kumatanthawuza kuwonetsa chilungamo kwa Mulungu kuti chilichonse chomwe iye analankhula chinali choona, kunena kuti anali atayipambana imfa, komanso kuti chilengedwe chatsopano chayambapo.

Kukwera kwa Yesu kumatanthawuza kuti iye watenga ulamuliro wake. Ntchito yake yoyamba inali yakuti iye atumize Mzimu wake Oyera kwa anthu omutsata iye. Phunziroli likuyang'ana kuti ndi chifukwa chani izi zinali zofunikira kwambiri chonchi mu nkaniyi.

Mdalitso wa Abulahamu

Kumbukirani pulani ya Mulungu ya chipulumutso, imene anayilengeza kwa Abulahamu, pamene anamulonjeza kuti kudzero mwa iye, mitundu yonse ya padziko lapansi idzadalitsidwa. Pawulo analengeza ku mpingo wa ku Galatiya umene umkapotozedwa kuti usiye kukhulupilira uthenga wabwino ndi kuyambiranso kutsatira chilamulo cha Mose, powuzidwa kuti lonjezanoli linali litakwanilitsidwa kudzero mu Mphatso ya kulandira Mzimu Oyera. Mawu amenewatu ndi mawu a mphamvu. 'Iye anatiwombola ife ndi cholinga chakuti mdalitso umene unaperekedwa kwa Abulahamu ufikire anthu a mitundu kudzero mwa Khristu Yesu, ndi cholinga chakuti kudzero mu chikhulupiliro tikakhoze kulandira lonjezano la Mzimu.' (Gen 3:14).

Mpesa obala zipatso

Mzimu ndi mfungulo wa zinthu zonse pakukwanilitsa zolinga za Mulungu. Nkhani yonse ikuwonesta kuti ngakhare anthu abwino kwambiri pakati pa anthu sangakwanitse chimene Mulungu wawayikizira. Isilayeli anali mpesa umene umabala zipatso zoyipa nthawi zonse (Isa 5). Yesu anafunafuna chipatso koma sanapeze kalikose (Mat 21:43). Chilamulo sichinali yankho – 'chilamulo chinalibe mphamvu mwakuti chimafooka ndi thupi' (Aloma 8:3) Thupi lakhara lili lamphamvu kwa ife nthawi zonse ngakhare titayesetsa bwanji, ngakhare titalinga zabwino bwanji (Aloma 7: 18 -19). Komabe Mzimu umatibweretsera ife mphamvu zatsopano ndi cholinga chakuti tikhoze kukhara mosiyana ndi kubala zipatso zimene Mulungu akuzifuna (Agalatiya 5:22 -23).

Kubwelera kwa Mulungu Mkachisi

Tawona kuti panali chiyembekezo chakuti Mulungu adzabweranso mkachisi amene anachokamo nthawi ya undende wa ku Babulo itangotsara pang'ono. Olemba uthenga wabwino anawonetsera kuti Yesu mwini ndiye anali kachisi watsopano, ndipo mmenemu ndi momwe Mulungu amabwelelera. Kuwonjezera pamenepo atumwi anabwera mkudzazindikira kuti kachisi tsopano ali mwa anthu amene amamutsatira Yesu, iwo amene anadzazidwa ndi Mzimu Oyera ndi iwo amene anasandulika kukhara mu gawo limeneli, kupezeka kwa Mulungu kukhozano kuzindikirika padziko lapansi (Aefenso 2 – 21 -22).

Ulamuliro olamulira pa chilengedwe

Adamu ndi Eva anapatsidwa udindo oyang'anira chilengedwe ndi kuchichitira umboni wakuchiwonetsera mmene Mulungu alili. Mu kuwukira kwawo iwo anataya chinachake cha dongosolo loteloro ndipo ndi kudzera mwa Yesu yekha ndi momwe udindowu unabwezeretsedwa. Yesu powaphunzitsa ophunzira ake pambuyo pakuwuka ku akufa kunapangitsa iwo kufunsa ngatidi kubwenzeretsedwa komaliza kwa ulamulirowu kuchitiki posakhalitsa (Machitidwe 1:6), zimene Yesu powayankha anawawuza kuti sizinali zoyenera kwa iwo kuti azidziwe koma kuti posakhalitsa Mzimu awadzadza iwo ndi mphamvu ndipo adzakhalanso mboni zake, kuwonetsera kudzikoka za mmene Mulungu alili (Machitidwe 1:8).

Ufumu wa Mulungu

Machitidwe 2: 42 – 47 ikupereka chithunzi cha momwe msonkhano wa mpingo ku Yelusalemu unalili. Pamenepa tikuwona zambiri zokhudza zimene chilamulo ndi aneneri amkalodzera, zimene iwo amkawona mu Isilayeli okwanilitsidwayo koma zimene sanaziwone nawo. Uwu ndiye unyinjira wa anthu a Mulungu, amene akukhara ndi mphamvu ya Mzimu Oyera. Zimene zinali zosatheka mmbuyomu zija tsopano ndi zotheka. Ulamuliro wa Mulungu unawoneka, pamene unayendelera mochulukira kwa anthu osowa, umodzi weniweni unawonekera, zozizwa zimkachitika ndipo anthu ochuluka 'amapulumsidwa'.

Cholinga cha Yesu chikukuzidwa

Zikuwonekeratu kuchokera mu buku la Machitidwe kuti ntchito zimene Yesu anaziyaamba (Machitidwe 1:1) zinayamba kuchitidwa ndi otsatira ake. Yesu anali atawawuza kuti, 'Monga momwe Atate ananditumira, nanenso ndikutumani inu' (Yohane 20:21), pamene anawawuzira iwo kuwonetsera mphamvu za Mzimu amene anali akubwera. Chomcho tikuwona nkhanu zabwino zikukwanilitsidwa. Zimene Mulungu amamulonjeza Abulahamu, zimene anaziwonetsera kudzera mwa Yesu tsopano amazitumiza kuti zidzadzize dziko kudzera mwa omutsata Yesu odzadzidwa ndi Mzimu Oyera, kubweretsa chikondi chake, uthenga wakwe wa kuyanjanitsa komanso mphamvu zake zomasula ku undende.

Funso lokambirana: Tawerengani Machitidwe 19 – ndi chifukwa chani Pawulo akufunitsitsa kudziwa zokhudza chomwe akudziwapo zokhudza Mzimu Oyera?

6.3 – Chilengedwe chatsopano – uthenga wa nkhani yabwino

Yesu anawapatsa otsatira ake udindo umene ukuwonetsera udindo umene unaperekedwa kwa Adamu ndi Eva, kwa Nowa, kwa Abulahamu, kwa Davide komanso kwa aneneri osawerengeka. Iye anawawuza kuti apite kudziko lonse, kuti akapange ophunzira mwa mitundu yonse, kuwabatiza ndi kuwaphunzitsa iwo kuti amvere zonse zimene iye anawaphunzitsa. Uthenga wa chilengedwe chatsopano ukulidzadzadzika dziko lapansi.

Nkhani yabwino ikugwira ntchito

Nkhani ya buku la Machitidwe ikutiwonetsa mmene bukuli limkamvekera kwa atumwi oyambilira pamene amkazingulira mu dziko lomwe tikulidziwali, akulalikira uthenga umene anapatsidwa ndi kukhadzikitsa magulu amene chidwi chawo chinali pa Yesu ndiponso odzadzidwa ndi Mzimu Oyera. Maguluwa anakhadzikitsa kachitidwe ka zinthu zomwe zinali zochokera mu ziphunzitso za Yesu. Machitidwe 2:42 ikunena kuti iwo anali odzipereka ku:

- **ziphunzitso za atumwi** – mosakayika konse zimenezi zimachokera mu malemba a Chiyuda, komano zinayamba kumveka mwatsopano kumanso kudalilika pamene iwo anawona kukwaniritsidwa kwake mwa Yesu.
- **Mgwirizano** – palibepo m'mbuyo monsemu pamene magulu anadzuka ndikukhara ogwirizana komanso kusamalirana koma likuchokera kumbiri za moyo zosiyanasiyana, magawo onse m'chikhalidwe kapenanso m'makhalidwe a kudziko.
- **kugawana mkate** – Nthawi zambiri amadya limodzi ndi kukondwelera chipambano cha Yesu uku akumbutsana wina ndi mzake za momwe zimenezi zinakhudza miyoyo yawo.
- **Pemphero** – amkayimba ndi kupemphera kudzera mu Masalimo, koma tsopano ndi chidziwitso chatsopano ndi kuzizwa ndi Mulungu amene amkamulambira..

Uthenga wabwino ukulengezedwa

Muzochitika zimenezi ndi pamene atumwi anapeza mpata olengeza 'vangeli' uthenga wabwino. Awatu anali mawu amene amagwiritsa ntchito Aloma panthawi imene amalengeza kulongedwa ufumu kwa Augusto kukhara Kayisala komanso olamulira wa ufumu wawo. Amkatuma olengeza awo kuti akalengeze za uthenga wabwino wakuti Augusto, 'mwana wa mulungu' wakhara 'mfumu ya dziko lapansi'. Ndi chifukwa chake sizinali zodabwitsa kuti uthenga wa atumwi unachititsa chipwilikiti. Kuwona kwa khanizi mwachidule m'ma ulaliki omwe unalembedwa mu buku la Machitidwe akuwonetsa zinthu zofananira ku ma ulaliki awo, ngakhare kuti amalalikira ku magulu osiyana.

- Yesu ndi kukwanilitsa kwa malonjezano amene ananenedwa m'malemba
- Moyo wa Yesu unali odzadzadzika ndi ntchito zabwino ndi machilitso
- Yesu anapachikidwa malingana ndi zolinga za Mulungu
- Yesu anawukitsidwa ndi kukwezedwa monga mfumu yoon
- Yesu anatumiza Mzimu wake Oyera
- Yesu adzabweranso ngati oweruza kudzabwezeretsa dziko lapansi
- Kotero lapani, khulupilirani ndipo mubatzidwe, khalani mbali ya mfumu yoon
- Landirani chikhululuko ndi malonjezano a Mzimu



Kuvutika ndi kulamulira

Limodzi ndi mayitanidwe olengeza za mfumu yatsopano komanso yoona, okhara mu ufumu osiyana tsopanolino mkatikati mwa ufumu wakale olamulidwa ndi munthu, panali chilungamo cha zoonza zenizeni za kutsutsidwa komanso kuvutika kumene Yesu anali atawafotokonzera ndi zimene iwo akuyenera kuchita pa zimenezi. Iwo amayenera kuwakonda adani awo, kuwakhulukira iwo amene awalakwira ndi kuchitira zabwino aliyense. Atumwi anachimvetsetsa kuti gawo lina la mayitanidwe awo kunali kukanidwa, mazunzo, ndi masawutso. Kwa iwo zimenezi kunali kugawana mazunzo a Yesu. Ndithudi, zonsezi kunali gawo la kubweranso kudzalamulira monga momwe Yesu anawalonjezera. Yohane adzazikamba zimenezi bwinolomwe mu mawu oyamba a mu buku la Chivumbulutso. 'Ine Yohane m'bale wanu komanso okhara nanu limodzi m'mazunzo ndi mu ufumu komanso kuleza mtima ndi kupilira zili za ife mwa Yesu' (Chivumbulutso 1:9). Kubwera kudzalamulira ndi kulowa ufumu zikutanthawuza kuthana ndi chisalungamo cha dziko lapansi mu njira yomweyo imene Yesu anachitira, pakuvutika ndi kukana kubwera m'mbuyo. Zimenezi ndi zimene tikudziwona mwa mtumwi Pawulo mu buku la Machitidwe, pamene amalengeza za mfumu yatsopano mu ufumu onse wa Chiloma mpaka atachitira umboni mkati mweni mweni mwa ufumuwo, ku Loma kwenikweniko.

Makalata olembewa ndi atumwi opita ku mipingo yosiyanasiyana ali ndi zilimbikitso zina ngati zimenezi kuwonetsera zimene Mulungu wachita powalumikizansitsa pamodzi kuchokera mu magawo a moyo osiyanasiyana, komanso kukhara nawo mayitanidwe amene analandira munjira yoyenelera.

Kwakukulu tikupezanso mu buku la Chivumbulutso zokhudza mavuto osiyanasiyana amene mpingo ukuyenera kukumana nawo mu nkondo yake yothana ndi mawukulu a za uzimu ndi mphamvu za kudziko lapansi, komanso pali chiyembekezo chinachake chakuti Mulungu adzabweretsa kwa ife tonse kulumikizana kwa chisangalalo kwa kumwamba ndi dziko lapansi kudzera mu zomwe takumana nazo.

Funso lokambirana: Kodi uthenga wabwino wa masiku ano ungafananizidwe bwANJI ndi kulengeza kwa atumwi?

6.4 - Chilengedwe chatsopano – kubwezeretsedwa kwa zinthu zonse

Tikukhara mu nthawi zakuti zambiri zokhudza kukwanilitsidwa kwa nkhanayi zatheka. Lonjezo limene Mulungu analonjeza dziko lapansi, lomwe analengeza kudzera mwa Abulahanu, kumapeto kwake lafikano. Mfumu yeniyeni ya ufumu wa Mulungu osatha uja yavumbulutsidwa. Tikhoza kukhara a mu chilengedwe chatsopano pongokulupilira mwa Mfumu yoona amene ali Yesu amene Mulungu anamuwukitsa ku akufa ndi kumpatsa iye dzina loposa mayina onse. Tikhoza kulandira Mzimu wake ngati chikole komanso chitsimikizo cha zonse zimene Mulungu adzachite mu chilengedwe. Tsopano watonkhanitsa pamodzi ngati magulu amene ali odzadzidwa ndi Mzimu Oyera kuti

tiwonetsere ulamuliro wa Mulungu ku chilengedwe chonse ndi kupititsa uthenga wa ulamuliro wake kwa anthu a mitundu yonse padziko lapansi. Nangano kodi nkhanayi ikutha bwanji?

Pamepepa ndi pamene timapeza nkhanu zambiri zosiyanasiyana. Mkwatulo, mileniyamu, mazunzo aakulu, sabata yomaliza ya Daniyele, ndi Alimagedo. Ndi zovuta kuyikapo mulomo pa mfundo zosiyanasiyana zimene zikukamba za mathedwe osiyanasiyana a chiphunzitso cha 'masiku otsiriza', koma muli zina zofunikira kuzidziwa pamene tikulingalira zimene bayibulo likunena zokhudza mapeto a nkhanu.

1) Kumbukirani nkhanu yayikulu

Takharatu masabata angapo tikuyang'ana za mmene nkhanayi ingalumikizani pamodzi komanso mmene ikulimbikitsidwila mbali ina iliyonse. Chinthu china chake chikafika ngati kusintha kwakukulu munkhani, chimene sichikumikizana bwino bwino ndi nkhanayo, samalani nacho makamaka chikakhara kuti chikuchokera mu chinthu chimodzi chokha. Chiphunzitso cha mkwatulo chikhoza kukhara chitsanzo chimodzi mwa izo. Ichi ndi chiphunzitso chimene chimanena kuti pakubweranso kwa Yesu iye adzabwera ndikuwatenga okhulupilira onse kuchoka padziko lapansi ndipo akakhara kumwamba ndi iye mpaka kalekale. Penapake chiphunzitsochi chasiya lemba mu nkhanu yayikulumo yokamba zakuti Mulungu adzawombola chilengedwe chake chabwinochi, osati kuchitaya ayi, komanso kuti iye akugwiritsa ntchito anthu ake kuti agwire ntchitoyi, osati kuwachotsamo.

Mofanana, ngati chiphunzitso china cha masiku otsiriza chikuwoneka kuti chikutibweza 'm'mbuyo' munkhanayi, nachonso chikuyenera kukayikiridwa. Chitsanzo cha zimenezi ndicho chiphunzitso chimene chimalongosola kuti kachisi wa Chiyuda adzakhadzikitsidwanso m'masiku omaliza malingana ndi ndime ya Ezekiyeli 40 mpaka 48. Komabe ngati zimenezi zikuyenera kudzabwera, kodi kachisi wooneka ndi masoyo adzakhara ndi ntchito yanji? Kodi msembe ndi zantchito yanji? Ndithudi, zimenezi sizithandizira kupititsa khanayi chitsogolo koma zikutibweza m'mbuyo mwa nkhanu, kotero tiyenera kufunafuna mamasulidwe osiyana a masomphenya a Ezekiel.

2) Kumbukirani kuwukitsidwa kwa Yesu

Chinthu chachidziwikire mu nkhanu yayikulu ya chilengedweyi chikupezeka mu thupi pa Yesu lowukitsidwa. Limeneli ndi mtundu wa thupi limene tidzakhare nalo komanso mtundu wa dziko limene ife tidzakhalemo mwakuti ngakhaleenso ntchito zathu mwanjira ina zidzachitira umboni mu kuwukitsidwa kwathu.

3) Dziwani kuti si zonse zimene zili momwe zilili

Tikuyenera kudziwa kuti mabuku a uneneli monga Daniyele, Zakaliya ndi Chivumbulutsa (mabuku atatuwa amagwiritsidwa ntchito kwambiri polosera zichitochito za kumapeto) ndi amene amavumbulutsa za mtsogolo. Kuvumbulutsa kumatanthawuza kuvundukula ndipo limagwiritsidwa ntchito pofuna kupereka mawonedwe a kumwamba pa zinthu za dziko lapansi, osati kutengedwa mmene zikunenedwera. Chitsanzo chabwino cha zimenezi ndi uneneri wa Yesaya okhudza chigamulo pa Babulo (Yesaya 13) m'mene akunena zokhudza dzuwa, mwezi ndi nyenyezi kuti zidzachita mdima. Kumwamba kudzanjenjemera ndipo dziko lidzasuntha pamalo pake. Kuwonongedwa kwa ufumu

wa Babulo kobwera ndi Apelezi kunachitika mu chaka 539 Mesiya asanabadwe. Ichitu chinali chochitika chachikulu ndiponso choopsya ku mayiko onse, kusintha kwa ulamuliro ndi chiwawa chomwe chinalipo. Komabe palibe chilichonse mwa zomwe analosera Yesaya chinachitika mmene zinamvekera, kotero tikuyenera kukhara a mzeru pamene chilankhulo chokamba zakutsogolo chikugwiritsidwa ntchito.

4) Kumbukirani kuti 'malemba onse ndi... Ofunikira'

Ngati tili ndi mawonedwe akuti buku la Chivumbulutso ndi uneneri umene wadzadza ndi kulosera zokhudza chimaliziro, ndiye kuti tikunena kuti bukuli lidzakhara ndi phindu kwa m'bado umodzi okha umene udzakhalepo udzakumane nazo zinthu zimenezi. Kwa ena onse mu mbiri ndiye kuti bukuli linali lopanda ntchito. Tsoka ilo mmenemu ndi mmene akhristu ambiri amaliwonera bukulo lerolino. Iwo amaganiza kuti tikadzakhara mu mbado omaliza ndi pomwe zidzakhare zachidziwikire, 'Apo bii sindidzililabada chifukwa chakuti ndi losamveka komanso loopsya'. Ndithu Mulungu anali ndi mapulani ochuluka okuti bukuli likwanilitse osati kungothandiza mbado umodzi okha! Buku la Chivumbulutso likhoza kuwerengedwa ngati kalata imene ikuwulura za mmene akhristu oyambilira amayenera kuthanani ndi chizunzo mmanja mwa akuluakulu a Aloma ndi Ayuda. Komanso za mmene mbado uliwonse wa anthu okhulupilira ungakhalire okhulupirika kwa Yesu pakatikati pa dziko limene lakana kuvomereza ulamuliro wa Yesu, komanso m'mene okhulupilirawo adzagonjetsere. Mukadzangoyamba kumvetsetsa mmene malembawa amagwilira ntchito mudzapezamo matanthawuzo ambiri komanso chilimbikitso, ndi kukwanitsa kulimbana ndi mavuto oyesera kukakamiza zochitika za padziko mu zolembedwa zokamba za ulosizi.

Mapeto a nkhani

Ngakhare zambiri sizimamvetsetseka, buku la Chivumbulutso likupereka chithunzithunzi cha kumene chilengedwe chikupita. Monga momwe chiyembekezo chilipo, tikuwonamo chithunzithunzi cha chilengedwe choyamba koma tsopano chakwanilitsidwa (Chivumbulutso 21 mpaka 22)

- Sikudzakhalano imfa kapena kulira maliro, kulira kapena ululu (Chivumbulutso 21:4) chilinganizo chakale cha mphamvu ya imfa chasinthika kwatunthu ndipo chilichonse chimene chinali mu dongosolo limenelo chawonongedwa.
- Sikudzakhalanso kachisi chifukwa chakuti Ambuye Mulungu ndi nkhoa yawo ali kachisi mwawo (Chivumbulutso 21:22) kumwamba ndi dziko lapansi tsopano zalumikizana.
- Sikudzalanso dzuwa kapena mwezi pakuti ulemelero wa Mulungu udzapereka kuwala ndipo mwana wa nkhoa ndi amene ali nyali yake. (Chivumbulutso 21:23). Dzuwa ndi mwezi zinapatsidwa ulamuliro kuti zilamulire kumwamba, kuwongolera usana ndi usiku. Zinali zizindikiro za mfumu yoona ya kumwamba ndipo tsopano sizikufunikanso, pakuti Mulungu mwini wavumbulutsidwa. Sipadzakhalanso usiku ndipo sipadzakhalanso kusokonekera kwa kupezeka kwa Mulungu.
- Iwo adzalamulira mpaka muyaya (chivumbulutso 22:5) – pamapeto pake ulamuliro umene unaperekedwa kwa Adamu ndi Eva pamene iwo akulamulira dziko lonse mu umodzi wawo oona pakati pa iwo ndi Mulungu.

Ntchito: Kodi mukhoza kuyilongosola bwanji nkhani yayikulu ya bayibulo?

7.1 – Kuyikambanso nkhaniyo

Panopano tayikamba nkhani ya bayibulo mwatsatanetsatane. Imeneyitu ndi nkhani imene ikufunikira kuyiphunzira bwino, komanso imene pamapeto pake idzayamba kusintha miyoyo yathu ndi mawerengedwe athu. Eyetu, ndikotheka kuyikamba nkhaninyi mu njira zambiri zosiyanasiyana, potsindika mbali zosiyanasiyana, makamaka kwa overa osiyanasiyana. Sabata ino tiwona nkhani yonseyi mu magawo atatu osiyanasiyana. Inde pali njira zambiri zolowezero nkhani ya mu bayibulo, koma njira zitatu zimenezi ndi zomwe zikuwoneka kuti ndi zofunikira kwambiri mu malingaliro a atumwi pamene iwo amkalemba chipangano chatsopano.

Nkhani yokhudza chilengedwe

Chaputala 1 – Ufumu wa mmunda

Nkhani ya kulengedwa kwa zinthu imatiwonetsera ife za Mulungu kuti ndi olamulira wa padziko lonse lapansi. Palibe chikayiko chilichonse pamene iye abweretsa dongosolo mu chisokonezo, ndi kuwuzira mpweya mu fumbi, kuwonetsa kuti ndithudi iye ndi amene ali olamulira. Ndi nthawi yochititsa chidwi kwambiri pamene iye akuyika chifanizo chake pa anthu ndi kuwapata iwo ulamuliro wake kuti adziyang'anira chilengedwe chake ndi kulidzadza dziko lapansi ndi ulamuliro wake. Anthu anakhara oyimira Mulungu padziko lapansi, pogwira ntchito mogwirizana ndi Mulungu. Mgwirizanowu unagona m'chikondi ndi kumvera kodzera m'chikhulupiliro mwa olenga, mwanjira ina zimenezi ndi zimene bayibulo limazitchura kuti kupembedza. Ufumu wa mmunda unapangidwa kuti ukule mpaka dziko lonse lapansi litayikizidwa pansi pa ulamuliro wa Mulungu.

Chaputala 2 – othandizira kulamulira aja akuwukira

M'malo mogwira ntchito limodzi ndi Mulungu mu mgwirizano wawo modzichepetsa, koma mtundu wa anthu unasankha kumvera mau awo, kulambira zinthu m'malo molambira Mulungu komano unatengeka ndi chisankho chodzisankhira zabwino kapena zoyipa ndi kukhara pawokha mosadalira Mulungu. Zotsatira pamoyo wawo komanso pachilengedwe chimene iwo amachiyang'anirachi zinali zowononga, pamene nsanje, madano, ndewu ndi kuponderezana kunalowa ndi kutenga gawo m'dziko.

Chaputala 3 – pulani ya Mulungu yopulumutsira ikuyambika

Mulungu analowelera kudzera mu moyo wa Abulahamu, analonjeza zobweretsa mdalitso wake kudziko lonse lapansi kudzera mwa Abulahamu ndi zidzukululu zake. Zomwe Abulahamu amayenera kuchita ndi kukhulupilira lonjezo la Mulungu ndi kuwonetsera kumvera kodzera mu chikhulupiliro chake chomwecho chimene chinali choyenera kuti akhare pa mgwirizano ndi Mulungu. Nthawi zonse pamene kumvera kofananaku kukuwonekera mwa chidzukululu cha Abulahamu, ubwino ndi zopeza za ulamuliro wa Mulungu zimawonekera. Yosefe amkakhara moteromo ndipo anapulumutsa mitundu yathunthu ku njala. Mose anakhara moyo oterowo ndipo anawatsogolera Aisilayeli kuchoka mu ukapolo. Yoswa naye amkakhara moyo umenewu ndipo anafikitsa ana a Isilayeli kuwalowetsa mu dziko limene Mulungu anawalonjeza.

Pachimake pa nkhani ya Isilayeli panabwera Davide Mfumuyo, munthu oweta nkhoa osati mkumuyerekeza – wa ndakatulo, yemwe anakhara ngati chitsanzo cha olamulira odzichepetsa okhara mumgwirizano ndi Mulungu wakukhara ndi chikhulupiliro chodalira pa iye. Mulungu analankhula mu nthawi yake imeneyi za zokhudza olowa ufumu wa Davide yemwe adzalamulire mpaka kalekale, amene adzabweretse zopeza za ulamuliro wa Mulungu wa chilungamo ndi mtendere osangokhara ku Isilayeli kokha, koma ku dziko lonse lapansi.

Komabe Aisilayeli nthawi zonse amawoneka kuti amatsata kuwukira kwa makolo awo, amamvera mawu awo, kulambira milungu ina ndi kusankha njira yawoyawo mmalo motsata njira ya Mulungu. Zimenezi zinawapangitsa kugwera mu nyengo za m'chipululu, ku ziwawa komano kupondereza anthu ofooka ndipo mapeto ake kupita ku ukapolo. Kumeneko ndi kumene Mulungu anachotseratu ulamuliro wawo ndipo anakhara m'mayiko a chilendo. Ngakhare pakubwelera kwawo kudziko lakwawo amkapezeka kuti nthawi ndi nthawi amakhara pansi pa ulamuliro oponderezedwa mmanja mwa olamulira ena ndipo samkakwanilitsa kusangalalira zabwino ndi zotatira za kukhara ndi moyo mogwirizana ndi Mulungu ndi ulamuliro wake.

Chaputala 4 – Mfumu yabwera

Kwa zaka zambiri, ngakhare munthawi yawo yonse ya ukapolo ndi ya kuponderezedwa, aneneri anawona tsiku limene mfumu yeniyeni ya ufumuwu itadzabwere, ndi kubwera ndi zabwino zonse komanso zoyenera za ulamuliro wa Mulungu. Anthu a Isilayeli anadzadzidwa ndi chiyembekezo cha nthawi ya kubwera kwa mfumu imeneyi. Komabe pamene Yesu anabwera zinali ngati mfumu yosiyana kwambiri ndi mfumu imene amayiyembekezera. Kubadwa kwake kunali limodzi ndi ziweto, anakakamizika kuthawa ngati munthu othawa nkondo komano anakulila mu dera losokonekera chikhaliidwe. Uthenga wake umkadabwitsa anthu achuma ndi amphawi omwe ndipo amkachezera ngakhare osawuka ndi anthu otayika. Iye anakana kukhara mfumu malingana ndi chiyembekezo cha anthu, koma mwakhama amakhara akulalikira zokhudza ufumu watsopano umene anthu apansi amatengedwa kukhara apamwamba, ufumu umene chikondi ndi chikhululuko chimapambana mphamvu komanso kumene chuma chokhara mu mgwirizano ndi Mulungu chimapangitsa kuti zinthu zina zimene amazilemekeza anthu zikhare zopanda ntchito komanso zopanda pake.

Chipambano chake chenicheni chinadza panthawi yake yokhomedwa pamtanda, pamene iye anadzitengera yekha zotsatira zonse za kuwukira kwa dziko lapansi, ndi kulowa mu imfa ndi kumugonjetsa iye amene amapondereza mtundu wonse wa anthu – oyipayo. Kuwuka kwake kunali kuvomerezedwa kukhara pamalo monga mfumu yoona komano ambuye wa zonse.

Chaputala 5 – anthu a mu ufumu

Iwo amene adzipereka kulumikizana ndi Yesu mfumu yoonayo, alowa mu ufumuwu ndipo akukhara pansi pa ulamuliro wake, kukhulupilira, kumvera ndi kupatsidwa mphamvu mwa Mzimu Oyera. Iwowatu akubweretsa ulamuliro wa Mulungu padziko lonse lapansi. Yesu anawatumiza omutsatira kuti apite kudziko lonse lapansi akalalike uthenga wakuti Yesu ndiye mfumu yoona, ndi kuchiwonetsa chilengedwe chonse ukoma onse ndi zopeza zoyenera zimene zimabwera ndi ufumu umenewu.

Tikudziwa kuti Yesu adzabwera tsiku linalake ndi kubwezeretsa chilengedwechi mokwanila kukhara pansu pa ulamuliro wake, kuwononga choipa ndi kusintha mbali iliyonse kuti ikhare yatunthu ndi kukhara malingana ndi zolinga zake.

Funso lokambirana: Kodi makalata a Chipangano Chatsopano akuwongoleledwa motani ndi kawonedwe kameneka ka ufumu wa Mulungu?

7.2 – Kuyikambanso nkhani – nkhani yokhudza kachisi

Chaputala 1 – kachisi oyamba

Nkhanu yokhudza kulengedwa kwa zinthu imakhara yokwana ngati tikuyikamba limodzi ndi nkhanu ya munda umene Mulungu ndi munthu akukhara limodzi mu umodzi wabwino. Kumwamba ndi dziko lapansi ndi zolumikizana ndiponso sizinasiyane. Ameneyu ndi kachisi oyamba, ndipo Adamu ndi Eva anali amsembe oyamba, amene amamuyang'anira kachisi ndi kuyimira Mulungu kudziko lapansi. Udindo wa mtundu wa anthu ndi kubweretsa dongosolo la mtundu omwewo kudziko lonse lapansi ndi cholinga chakuti moyo uyende bwino komano kuti kupezeka kwa Mulungu kuyendelere pema paliponse.

Chaputala 2

Pamene anthu amene ali mumgwirizano ndi Mulungu aganiza zokhara modzilamula okha mosadalira Mulungu, dongosolo lonse la kumwamba limagwedezeka. Adamu ndi Eva anathamangitsidwa m'munda ndipo panalibenso kuthekera kobwelera. Kumwamba ndi dziko lapansi kunali kolekana tsopano ndipo sipakuwoneka njira imene munthu angapeze kuti amufikire Mulungu. Popanda kupezeka kwa Mulungu mtundu wa anthu umayamba kufanana ndi zinyama ngati mmene zimachitira pamene zikukhara china ndi chimzake, zimaponderezana komanso kuchitirana nkhanza mu zichitochito za zikhalidwe zake.

Chaputala 3 – kulumikizanso

Lonjezano la Mulungu kwa Abulahamu linali lakuti kudzera mwa iye Mulungu adzadalitsa mitundu yonse ya padziko lapansi. Tinazindikira pakupita kwa nthawi kuti lonjezanoli likudza kudzera mwa Mzimu Oyera, kupezeka kwenikweni kwa Mulungu. Yakobo yemwe anali chidzukululu cha Abulahamu anakumana ndi Mulungu zimene zinamupangitsa kudabwa ngati kuti wapunthwa pachipata cha Edeni (Genesis 28:17), 'chipata cha kumwamba'.

Mose anakumana ndi Mulungu pa chitsamba choyaka moto, kenako pa phiri loyaka moto, kumene anamuchondera Mulungu kuti asawachokere anthu, zimene zinamupangita Mulungu kulonjeza kuti iye apezeka pakati pawo (Ekisodo 33:14). Ndithudi, anthu a Isilayeli anatchedwa ufumu wa ansembe, mtundu watunthu umene ukhare chizindikiro cha Mulungu kudziko lapansi.



Kuzindikiritsa za chiphunzitso cha m'bayibulo chokhudza mulungu 6/

Komabe kupezeka kwa Mulungu kumapezeka pa 'Likasa Iya Yehova' lokha limene limasungidwa mu Chihema chimene Aisilayeli amkanyamula nthawi imene amkazungulira m'chipululu muja. Anthu ochepa okha ndi amene analoledwapo kulowa mu chipinda choyeretsetsa m'mene Likasalo limkasungidwa, kuteleku kupezeka kwa Mulungu sikunapezeka mu unyinjira wa anthu.

Davide patapita nthawi anapereka lamulo lokuti kachisi wa Ayuda amangidwe, amene Solomo yemwe anali mwana wake wamamuna anazamangadi. Komabe ngakhare Solomo mwini wakeyo anazindikira munthawi yomweyo kuti nyumba chabe, ngakhare itakula motani siyingathe kusunga Mulungu Wamphamvuzonse (2mbiri 6:18). Kachisiyu anakhara chizindikiro cha lonjezano la Mulungu kwa Aisilayeli lakuti iwo ndi anthu ake ndipo adzakhara pakati pawo mpaka kalekale. Zimenezi ndi zomwe zinawapangitsa iwo kukhara apadera pakati pa mawufumu onse a padziko lapansi.

Komabe Ezekiyeli mneneri anawona masomphenya a ulemelero wa Mulungu ukuchoka mu kachisi ndipo mosakhalitsa anthu a ku Babulo anawonnga kachisi ndipo anawatenga Aisilayeli kuwatulutsa mu dziko lawolo. Izi kwa Aisilayeli zinawonetsera kuti Mulungu wachoka padziko. Ngakhare kachisi atamangidwanso, chipinda choyeretsetsa chinakhalabe chopanda kanthu ndipo iwo amkadikira kuti kupezeka kwa Mulungu kubwelere ndi kukhara pakati pa anthu ake ngati mmene amkapangira m'mbuyomu.

Aneneli anawona ndipo analengeza kuti ndithu Mulungu adzabwelera ku kachisi wake ndipo adzabwezeretsa mtunduwa ku ulemelero wake wakale, Hagayi ananena kuti kachisi watsopanoyo adzakhara ndi ulemelero wawukulu kuposa wa kachisi wapanyu (Hagai 2:9). Ezekiyeli anawona kachisi wamkulu ndi mtsinje wakutuluka mkati mwake umene umabweretsa moyo kwa mitundu yonse ya padziko. Habakkuk analiwona dziko lonse lapansi litadzadzidwa ndi ulemelero wa Ambuye. Lonjezano linali lakuti tsiku lina lake kumwamba ndi dziko lapansi kudzalumikizana.

Chaputa 4 – kachisi weniweni

Yesu analengezedwa ndi Yohane kuti iye ndiye mawu amene anasandulika kukhara thupi ndi kukhara (chihema) pakati pathu. Zoonadi Yesu ndiye amene anali kachisi weni weni amene zinthu zonse zimkaloza kwa iye. Mwa iye anthu ndi Mulungu analumikizidwanso moona. Mu kachisi ameneyu anthu akutha kukumana ndi Mulungu, kulandira kuchoka kwa Mulungu, kupezamo chikhululuko, mamasulidwe ndi kubwezeretsedwa. Pathawi ya kufa kwake katani limene limatchinga malo opatulika kwambiri linang'ambika kuyambira kumwamba mpaka pasi ndipo chimene chimkabidwa chija sichinabidwanso.

Chaputa 5 – Kachisi wamoyo

Chilengedwe chatsopano chimene chinalengezedwa kudzera mwa Yesu chinayamba kuyendelera paliponse. Choyamba, anthu amene amkayenda naye Yesu anasonkhana pamodzi, anthu okwana 120 mwa iwo analandira kupezeka kwa Mulungu mu njira yatsopano pamene iwo anadzadzidwa ndi Mzimu Oyera. Kumwamba kunali kukulowa mu dziko lapansi. Kachisi anali akukula. Pasanapite nthawi anthu enanso ochuluka ku Yerusalemu anayambano kumva kupezeka kwa Mulungu mu miyoyo yawo kudzera mwa Mzimu Oyera. Ndipo atumwi anatenga uthengawo kumka nawo kunja kwa malire a dziko la Isilayeli, kwa anthu omwe anachita nawo malire ndipo anazizwa atawona kuti kupezeka kwa Mulungu kukuwadzadza iwonso. Pamene Yesu anawatuma

ophunzira ake kuti apite kudziko lonse lapansi ndi kukapanga ophunzira a mitundu yonse zimatanthawuza kuti kachisi wa Mulungu adzikhara akukulirakulira, mpaka tsiku limene Yesu adzabwelera ndi kusintha zinthu zonse ndi cholinga chakuti kumwamba ndi dziko lapansi zidzakhare zolumikizana kwatunthu kachikenanso, koma panopa kulumikizanakukudzakhara mpaka kalekale.

Funso lokambirana: Kodi makalata a Chipangano Chatsopano amakulitsidwa bwanji malinga ndi nkhani ya kachisi?

7.3 – Kuyikambanso nkhani – Nkhani yokhudza Pangano

Chaputala 1: Mgwirizano woyamba

Pamene Mulungu analenga dziko lake labwino, anayika munthu kukhala olamulila pa zinthu zonse. Izi zinachitika potengera mgwirizano omwe unalipo pakati pa Mulungu komanso Adamu ndi Eva, powawonetsa iwo mmene angasamalire chilengedwe ndikuwapatsanso malamulo pazomwe akuyenera kuchita komanso kusachita. Pa mgwirizano umenewu mmundamo zinthu zimakayenda bwino ndipo anthu anapatsidwa lamulo loti apite ndikuti adzadzize dziko lonse.

Chaputala 2: Mgirizano ukusweka

Pamene anadya chipatso cha mumtengo odziwitsa zabwino ndi zoipa, anadzipanga kukhala osadalira pa Mulungu ndi kuphwanya mgwirizano umene Mulungu anali atapangana nawo. Pamene munthu anakhara pa yekha osadalira kulumulidwa ndi Mulungu, ndi kudzisankhira kulekanitsa zabwino ndi zoyipa pa iwo okha, dziko lomwe anapatsidwa kuti adziliyang'anira lija linawonongeka ndipo linakhara ndi makhalidwe a chiwawa, mantha ndi kuponderezana.

Chaputala 3 – Lonjezo la Mulungu la kuchiza dziko

Njira ya Mulungu yochizira dziko lapansi ndi kudzera mu pangano, choyamba anapangana ndi Abulahamu kenako kwa zidzukululu zake. Pangano ndimgwirizano okhazikika pakati pa mbali ziwiri ndipo silimayenera kuphwanyidwa. Gawo la Mulungu linali lakumudalitsa Abulahamu, kumupatsa zidzukululu ndi malo olidalitsira dziko lapansi kudzera mwa iye. Mbali ya Abulahamu ku panganolikunali kungomukhulupilira Mulungu. Zonse zimene Abulahamu anachita kuti amusangalatse Mulungu zinadzera mu chikhulupiliro chimenechi.

Pamene Mose anawatsogolera kuchoka ku Ijipiti, iwo anakumana ndi Mulungu pa phiri la Haleb, ndipo kumenekonso Mulungu anapanga nawo pangano, panopano anapanga ndi mtundu onse. Zimenezitu zinali ngati ukwati pamene mbali zonse zinalonjeza kukhara zokhulupirika kwa wina ndi mzake. Kwa Aisilayeli zimenezi zimatanthawuza kuti akuyenera kutsata malamulo ambiri amene anaperekedwa kwa iwo ndi cholinga chakuti iwo apatulidwe kukhara mtundu. Komabe patapita nthawi Yesu anafotokoza malamulowo mwachidule ponena kuti, 'Udzikonda Mulungu

ndi mtima wako onse komanso udzikonda mzako mmene udzikondera.' Isilayeli anayitanidwa kukhara kuwala kwa mitundu, kuliwonetsa dziko mmene lingakhalire mumgwirizano ndi Mulungu.

Komabe iwo anaphwanya pangano lomwe Mulungu anapangana nawo, zomwe zinawapangitsa aneneri kuti adzigwiritsa ntchito mau monga, hule, mkazi wadama ndi kutha kwa banja. Zimenezi zinakathera mu kutengedwa kwawo kupita ku Babeloni ku ukapolo, chizindikiro chowoneka ndi maso chakuti iwo anaphwanya lonjezano lomwe anapanga ndi Mulungu.

Komabe aneneri anawona kuti pangano latopano likubwera. Mkatikati mwa undende, Yelemiya analankhula zopanga pangano latsopano ndi anthu ake limene chilamulo chidzalembedwe m'mitima ya anthu. Ezekiyeli akunena za nthawi imene Mulungu adzachotse mtima wa mwala ndi kuyikiza mtima wa mnofu zomwe zidasunthike ndi kumumvera Mulungu ndi mzimu watsopano.

Chaputala 4 – pangano likuvumbulutsidwa

Yesu atakhara kuti adye chakudya cha Paska pamodzi ndi ophunzira ake usiku wakuti mawa lake afa anawapatsa iwo pangano latsopano limene Mulungu amkapanga. Iwo samayeneranso kusangalalira zimene Mulungu anapanga pakumumasula Isilayeli mu ukapolo ku Aijipiti koma amayenerano kumakumbukira imfa yake ndi kumasulidwa kwawo kwa oyipa amene anali atakula mphamvu pa iwo.

Chaputa 5 – Pangano latsopano ndi pangano lomwe lija

Atumwi motsogozedwa ndi Mzimu anayamba kumvetsetsa zokhudza zimenezi, chifukwa mkosatheka Mulungu kupanga lonjezo ndi kusalikwanilitsa, anamvetsetsanso kuti malonjezano onse amene Mulungu anapanga ndi amodzi ndipo ndi ofanana. Kapena kuti tilankhule mwachindunji, pangano latsopano mwa Yesu ndi kukwanilitsa kwa mapangano ena onse amene Mulungu anapanga.

Anthu ake adzazidwa ndi Mzimu Oyera motero ali pa ubale wabwino ndi Mulungu pamene iwo achita mayitanidwe awo obweretsa ulamuliro wake kuchilengedwe chonse.

Lonjezano lake kwa Abulahamu lakuti adzampatsa zidzukululu zambiri, dziko komanso mdalitso ku mitundu yonse kwakwanilitsidwa pamene otsatira a Yesu miyandamiyanda atumizidwa kudzikola lapansi kuti akafikitse mdalitso wa Mzimu wa Mulungu ku mitundu yonse.

Mgwirizano wake ndi Mose ndi anthu a Isilayeli ndi 'zithunzithunzi' ndi zikwangwani kuwonetsera chikhalidwe cha Mulungu ndi njira zake, zomwe zikuwonekera mwa Yesu. Otsatira wina aliyense wa Yesu ali ndi pangano lokhazikika, losagwedezeke komanso la moyo onse lomwe anapangana ndi Mulungu. Mbali ya Mulungu mu mgwirizanowu ndi yakuti iye adzakhara Mulungu wathu komanso sadzatisiya. Tidzakhara naye moyo wathu onse, mu imfa mpaka mu kuwukitsidwa kwathu ndi kufika nthawi ya kumwamba ndi dziko lapansi latsopano ndi kungokhulupilira.

Funso lokambirana: Kodi makalata a chipangano chatsopano akutambasulidwa bwanji potengera nkhani ya chipangano?

7.4 - Kuyilongosolanso nkhani – Aefenso munkhani yonse ya mu bayibulo

Mu magawo atatu amene tadutsawo tawona njira zitatatu zomwe tingakhoze kuyilongosola nkhani ya mu bayibulo. Palitu njira zina zimene tingakhoze kugwiritsa ntchito, koma tagwiritsa ntchito njira zozizwika kwambiri. Lero tikuganizira zokhudza ubwino wakusunga nkhani pamtima, nkhani ya bayibulo pamene tikuwerenga ndime za mu bayibulo, makamaka mu chipangano chatsopano. Mau akuti kusanthula amagwiritsidwa ntchito ndi alaliki komanso ophunzira zokhudza Mulungu. Zimangofunika kudzifunsa kuti kodi ndi chani chimene olemba weniweniyo amafuna kutanthawuza?

Kuliyankha funso limeneli kutithandiza ife kenako kutithandiza kumvetsetsa mmene tingazigwiritsire ntchito zimene tawerenga mu ndimeyo kwa ife komanso kwa iwo amene tikuwaphunzitsa.

Kuti tiyankhe funsoli tikuyenera kumvetsa izi:

- **Pamene pachoka nkhani** - Kodi chikhalidwe cha nthawi imeneyo makamaka nyengo zokhudza anthu amenne akukambidwawo chinali chotani?
- **Chimachitika ndi chani** - Kodi chimene chinamuchititsa olembayo kutumiza kalatayi ndi chani?
- **Nkhani** - Kodi ndi nkhani zANJI za mu bayibulo zimene olembayo amazidziwa pamene akugwiritsa ntchito mau osiyanasiyana ndi ziganizo?

Mayankho amafunso oyamba awiriwo amapezeka kwenikweni pa kusanthula bayibulo kwabwino zimene zikuwonjezera mapeji okamba za chiyambi ndi nkhani zamkatimu za mu buku lina lililonse. Mukhozanso kupeza uthenga ngati umenewu. Mukhozanso kuzipeza zopezekeratu pa makina a intaneti. Komabe, funso lachitatu, lokhudza nkhaninyi ndi limene latitengera masabata ambiri pano tikulimbana nalo kuti timvetsetse.

Tiyeni tiwone Aefenso chaputala 1 kuti tiwone mmene Pawulo akugwiritsira ntchito ziganizo zimene zikuwonetsa kuti iliyonse mwa nkhani imene tayikambirana ilinso m'malingaliro ake. Zimenezi zitipatsa mafungulo owonjezera kuti tikwanitse kumvetsetsa chilichonse chimene amkalinga mmene iye amalemba kalatayi.

Aefenso 1:3

Mdalitsa (nkhani yokhudza pangano) - Tikutha kumvetsa kuti Pawulo anawona kukwanilitsidwa kwa pangano la Mulungu ndi Abulahamu likugwira ntchito m'moyo wa anthu okhulupilira a ku Efenso. Dalitsoli sikuti ndi la iwo okha ayi koma lakuti iwo adzabweretse dalitsa kudzikola lapansi.

Miyamba (nkhani yokhudza kachisi) - Tsopano kumwamba ndi kotheka kwa iwo amene ali mwa khristu.

Aefenso 1:4

Kusankhidwa / kusankhidwiratu (nkhani ya Pangano) - Mulungu anasankha anthu amene iye adzabweretsere dalitsa lake kudzikola lonse lapansi. Nkhani yokhudzana ndi kusankhidwa ikukamba kwambiri zokhudza kupatsidwa ntchito yofunika kugwira kusiyana ndi kukhara mkati kapena kunja kwa kukonderedwa ndi Mulungu.



72 Kuzindikiritsa za chiphunzitso cha m'bayibulo chokhudza mulungu

Oyera komanso opanda chilema – (nkhani yokhudza kachisi) - Kumwamba ndi dziko lapansi kungakumane pokhapokha dziko lapansi litayeretsedwa kukhara ngati kumwamba. Ifeyo tsono tili ndi mayeretsedwe m'malingaliro athu amene anatheka kudzera mwa Yesu.

Aefenso 1:5

Anatikonzeratu (Nkhani ndi pangano) - Mulungu anapanga lonjezano lokhazikika kuti abweretse anthu mu banja lake.

Aefenso 1:7

Kuwomboledwa (nkhani ya ufumu) - anthu anali akapolo mu ufumu wa mdima koma tsopano awomboledwa, kupulumutsidwa andi kumasulidwa.

Aefenso 1:9

Chinsinsi cha chifuniro chake (nkhani ya kachisi) - chifuniro cha Mulungu chawululidwa mmene iye adzabweretsa zonse za kumwamba ndi za padziko lapansi pansi pa ulamuliro wa Yesu.

Aefenso 1:13

Mzimu Oyera (Nkhani yokhudza kachisi) - Kumwamba kwalumikizana ndi dziko lapansi popereka Mzimu Oyera, amene ali chikole chomutsimikizira okhulupilira za kudzazidwa kwa cholowa chathu.

Aefenso 1: 17 -18

Maso a mtima wanu akuwunikiridwa (nkhani yokhudza pangano) - kukwanilitsidwa kwa lonjezano la Mulungu kuti adzawapatsa anthu mtima wa mnofu ndipo kuti anthu onse adzamudziwa iye.

Aefenso 1:19

Mphamvu yayikulu yosafananizidwa (nkhani ya ufumu) - Yesu anakwezedwa kukhara wapamwamba koposa mphamvu zonse, ndipo ife tapatsidwa malo a ulamuliro limodzi ndi iye, kulidzadza dziko lonse lapansi kukhara monga thupi lake.

Aefenso 1 mwachidule - Tikuwona nkhani ya kachisi ikukhazikika kwambiri m'malingaliro a Pawulo, pamene iye akuwonetsera chithunzi chachikulu chakuti Mulungu akulumikizitsa kumwamba ndi dziko lapansi pamodzi, kukhara pansi pa ulamuliro wa khristu (Ch 1:10). Zimenezi zikuchitika panopa mu mpingo, kudzera mu mphamvu ya Mzimu mwa ife (Ch1:14), pamene tikulamura pamodzi naye (Ch 1:23). Iye adzapitiliza kuzindikira m'mene Mulungu akumangira mpingo wake kukhara kachisi, mmene Mulungu akukhara kudzera mu Mzimu wake (Ch 2:21 -22), ndiponso mmene mgwirizano wa kumwamba ndi dziko lapansi ukuwonetseredwa mwa ife potilumikizitsa ndi magulu osiyanasiyana a chikhalidwe (Ch 3:6) chimene tikuyenera kuteteza (Ch 4:3). Cholinga chathu ndi chakuti tikule ndi kuwonetsera Yesu kwatunthu (Ch 4:15 -16), kukhara odzazidwa ndi Mzimu kusiyana ndi kukhara mmene ena onse a kudziko akuchitira (Ch 5:18).

Ntchito: Tatangani ndime ina mu kalata ndikupanga phunziro lofanana.

8.1 – Kupanga phunziro lanu lokhuza kuphunzira zokhudza Mulungu

Mawu oyamba

Nthawi zina anthu adzakufunsani kuti, 'Kodi bayibulo limanena zotani zokhudza,’ kapena mukufuna kuphunzitsa zokhudza phunziro linalake. Mmalo mongosankha mavesi apa kapena apo, tikuwona kuti mkoyenera kuti tiwone mmene mutu wa nkhani umapangidwira ndi nkhani yochokera mu bayibulo.

Msanamira za malamulo a zonse

Msanamira ya chilengedwe - Kodi ndi chani chimene mukuwonamo chokhudza chilengedwe mu mutu wa nkhani yanuyo? Kodi zimenezo zikukuwuzani zotani zokhudza malingaliro a Mulungu?

Msanamira ya kugwa - Kodi ndi chani chimene chikukhudza kugwa mu mutu wa nkhani yanu?

Msanamira yokhudza Isilayeli - Kodi mutu wa nkhani yanuyo ikutambasulidwa bwanji mu nkhani ya Isilayeli? Kodi zimenezi zikukuwuzani chani chokhudza malingaliro a Mulungu pa zochitika zokhudza kugwa?

Msanamira yokhudza Yesu - Kodi yesu akuwonetsera bwanji kukwanilitsa kwa nkhaniyi? Kodi iye akukwanilitsa zotani zokhudza nkhaniyi?

Chilengedwe chatsopano - Kodi mpingo wa chipangano chatsopano umapanga bwanji za nkhani imeneyi? Kodi mutu wa nkhaniyi umawoneka bwanji pakukamba za kukwanilitsa za chilengedwe chatsopano?

Tiyeni tigwiritse ntchito msanamira zimenezi pamene tikuyang'ana zokhudza 'Kodi bayibulo likukamba chani pa nkhani yokhudza Sabata?

Chilengedwe: Munkhani yokhudzana ndi chilengedwe, tikuwona kuti Mulungu anapumula pa tsiku la chisanu ndi chiwiri (kapena loweruka malingana ndi kamvedwe kathu ka zinthu lero lino). Mulungu analeka kaye zonse mkusangalalira zinthu zimene wazipanga. Tikuwona kuti Sabata linali lofunikira kwa chilengedwe chonse. Tikuwonamo kuti masiku ena onse amkakambidwa kuti, 'madzulo' ndi 'mmawa', koma sabata silinapatsidwe malire zomwe zikhoza kutanthawuza kuti tsiku la chisanu ndi chiwiri ndilomwe linali lofunikira, tsiku limene tidzalidziwe.

Kugwa: Zichitochito za munthu zofuna kukhara osadalira Mulungu zimabweretsa imfa kudziko lapansi, ndipo anthu anathamangitsidwa pamaso pa Mulungu. Nthaka inatembeleredwa kotero kupuma kumene Adamu ndi Eva anali nako m'munda wa Edeni kunasowa.

Isilayeli: Sabata linakhadzikitsidwa ngati gawo limodzi la pangano lomwe linapangidwa pakati pa Mose ndi Isilayeli, mbali zonse munjira yokukhalira ngati Mulungu, komanso kusangalira ufulu umene anali nawo, umene unaperekedwa pakumasulidwa mu ukapolo wa ku Ijipiti. Zichitochito za nthawi zonsezi zinali chikumbutso cha zonse zimene Mulungu anawachitira iwo komanso chikhadzikitso cha sabata iliyonse chakuti chikhulupiliro chawo chonse chinali mwa Mulungu, amene amawapatsa zosowa zawo.

Malamulo a Mose nawo anali ndi malamulo okhudza Sabata la dziko zaka zisanu ndi ziwiri zilizonse, kuwonetsera kufunikira kwakuti chilengedwe chonse chidziwe mpumulo umene Mulungu amapereka, kumenekunso kunali kuwakumbutsa anthu a ku Isilayeli kuti Mulungu mwiniwake ndiye amene amawapatsa zosowa zawo. Molumikizana ndi sabata ya Mulungu uliwonse komanso sabata ya chaka panalinso chaka cha jubili, sabata la masabata. Panthawi ya nthawi yofunikira ya chaka cha sabatachi, akapolo amkamasulidwa, ngongole zimkathetsedwa komanso malo onse amabwezedwa kwa eni ake eni eni.

Yesu: Zichitochito za Yesu pa tsiku la sabata zinali zosokoneza kwa akulu a chipembezo. Iye amawoneka ngati kuti amadela chikhaliidwe chodziwika bwino cha Sabata, amadziyikira kumbuyo pamene iwo anadya tiligu m'minda muja, ndipo anafika pomachiza ndi kumasula anthu pa sabata komanso kugwiritsa ntchito mikumano ya mphamvu pakuwaphunzitsa Afalisi kuti akwanitse kumvetsetsa kuti chofunikira cheni cheni cha Sabata chinali choposa zinthu zimene munthu analetsedwa kuchita zokha. Kutsimikiza kwake kukuwonetsa kuti zikukhudzana ndi ufulu umene amapatsidwa anthu pa tsiku la jubili; pakupereka mpumulo kwa othodwa ndi kubwezeretsedwa kwa iwo amene amadziwa kuti akufunikira kutero.

Chilengedwe chatsopano: Malingana ndi mmene zinalili ndi mpingo wa mu chipangano chatsopano, sabata limene amakhara akulikondwelera kwa nthawi yayitali linabwera kudzera mwa munthu otchedwa Yesu. Iwo anapeza mpumulo mwa Mulungu komanso ufulu weniweni. Monga okhulupilira amakumana pamodzi pa 'tsiku a Ambuye' (la Mulungu), kuti agawane mkate limodzi, kukumbukira imfa ndi kuwuka kwa Yesu. Ena amkatsatabe Sabata ngati mmene zimakhala m'mbuyomo, koma ena amaliwona tsiku lililonse kukhara lofunikira. Magulu a mipingo anadzikhazikitsa okha pa chilamulo cha sabata ya chilungamo, ufulu, kukhululuka, kulowa manja ndi kulandira kukonderedwa kochokera kwa Mulungu. Chiyembekezo chawo chinali mu kubwera kwa Yesu kudzalibwezeretsa dziko ku mpumulo wake wa chilengedwe. Pamene dziko lonse la pansi lidzadzadze ndi kupezeka kwa Mulungu.

Funso lokambirana: Kodi mungaphunzitse bwanji za sabata mu dela la anthu amene mumawaphunzitsa?

8.2 – Kupanga phunziro lanu lokhudza kuphunzira zokhudza Mulungu

Lero tibwereza zichitochito zopanga mutu wa nkhani, kulekana ndi kungoyang’ana pa chindunji cha chilungamo.

Ndalama ndi chisamaliro

Chilengedwe: Kuchokera mu nkhani ya chilengedwe tikuwonamo kuti zinthu zonse zinachokera kwa Mulungu. Iye amapereka mbewu, mvula, dzuwa ndi nthaka yabwino, ndipo ndi iye yemweyo amapereka mphamvu ndi upangiri kwa mlimi.

Komabe tikuwona kuti zopatsidwazo zimabwera pakakhara kuti munthu ndi Mulungu akugwira ntchito mu umodzi komanso mwa mgwirizano. Pamene munthu akumvera kuyitanidwa kwake ndi Mulungu kuti apite kudziko lonse akabweretse dongosolo kudziko komanso chikhulupiro ndi kumvera. Zimenezi zimabweretsa zopereka za Mulungu ndi chimwemwe cha chisangalalo ndi kukwanilitsa kwa iwo amene akugwira ntchito mogwirizana ndi Mulungu.

Kugwa: Pamene Adamu ndi Eva anamuukira Mulungu, chimodzi mwa zotsatira zake ndi chakuti ntchito zinayamba kukhara zopweteka. Khama lathu loposalo silimatibweretsera mayankho abwino omwe timayembekezera. Komabe izi zikutanthawuza kuti tsopano munthu akhoza kukhara odalira pa Mulungu.

Isilayeli: Madalitso amene Isilayeli amawamvetsetsa kwenikweni amakhudza chuma ndi za kuthupi, zomwe zimawoneka mu njira ya ndalama, ziweto malo ndi banja. Chilamulo cha Mose chinakambapo za malamulo okhudzana ndi kupereka, makamaka nkhani yokhudzana ndi kupereka chachikhumi, zichitochito zopereka limodzi mwa magawo khumi pa zinthu zimene mumapeza. Zimenezi zimathandizira mu magawo angapo, kuphatikizapo

- Kupezetsa thandizo pa zosowa za ansembe
- Kupereka kwa amphawi
- Kusungira za madyelero komanso zikondwelero

Kupereka chakhumi kumathandizanso kuphunzitsa kupereka molowa manja ndi kuwathandiza iwo kuzindikira kudalira pa Mulungu ngati yemwe amawapatsa zonse. Mwanjira ina lamulo limaphunzitsa kuti iwo amene amasunga pangano adzakhara ndi zokolera zambiri, banja labwino komanso chitetezo ku zoipa.

Zolembe za mzeru nazo zimakambanso za zabwino zambiri zimene zimaperekedwa, polumikizanso kugwira ntchito molimbika, moyo olungama komanso kulowa manja kukhara mphoto ya pamoyo ndi kuchita bwino pamoyo. Zimaphunzitsanso zokhudza kuyipa kwa chuma komanso mmene chuma chingalowere m’moyo ndi kusandulika kukhara fano. Zimawonetseranso phunziro lokhudza anthu olungama koma osawuka ndi a chuma osalungama.

Yesu: Yesu anakambapo zambiri zokhudza ndalama koma amawonetsa kuti akutembenuza kufunikira kwake ndi kuwuzondoza. Iye ananena momveka bwino

kuti Mulungu ndiye opereka wamkulukulu ndipo, molowa manja iye ndi amene amayang'anira chilengedwe chake, koma ndalama mwa iyo yokha ikuwoneka kuti ndi kanthu kakang'ono kapena kanthu kotchinga kuti munthu asasangalalire moyo wake mu ufumu wa Mulungu. Kuwomba mkota kwa chiphunzitsochi kukhoza kupezeka mu buku la Luka chaputala 16 m'mene iye anafananiza chuma cha kudziko ndi chuma cha munthu wina chimene amangokwaniritsa kuchiyang'anira mkumachita kuti kuli chuma chenicheni chimene chidzapezeka mu ufumu wa Mulungu zimene sizikugwirizanso ndi ndalama komanso zinthuzo ndi zanu ndithu. Paliponse pamene timapeza otsatira a Yesu akukamba chuma m'malemba, zimangotchulidwa kamba ka chidwi chawo cha kufuna kupereka zomwe ali nazo. Iwo ndi amene Yesu amawayitana kuti amutsate koma chifukwa cha chuma chawocho amakana kuyitanidwako.

Chilengedwe chatsopano: Mpingo oyambilira unapezadi chuma chowonachi (moyo okhara ndi Mulungu, ubale woona, chisangalalo ngakhare mu masawutso) mochuluka mwakuti amkaziwona zosavuta kupereka chuma chawo molowa manja ngati ena ali ndi chosowa. Iwo amkawasamalira osawuka komanso amene ali osowa. Atsogoleri a mpingo anaphunzitsidwa kukhara chitsanzo kwa anthu pogwira ntchito molimbika ndi cholinga chakuti adzitha kudzithandiza okha ndi kuthandizanso ena amene sangathe kuzipezera zosowa zawo. Kupereka chachikhumi sikunatchulidwe, koma kupereka molowa manja kwa iwo amene sangathe kudzipezera okha thandizo m'madera awo kapena akamva kuti panali zosowa ku mpingo omwe unali kutali. Anthu okhawa amene amalandira malipiro nthawi ndi nthawi kuchokera kumpingo anali amene amagwira ntchito ya utumwi kupita kumalo ena atsopano. Kwa iwo amene anali ndi udindo olalikira m'mpingo ikuluikulu ndi amayi amasiye amene amapemphera komanso kugwira ntchito molimbika pofuna kuthandiza anthu a mipingo ya mudera. Kumeneku ndi kumvetsetsa kwabwino kwa m'mene zinthu zilili panthawi ino pakhani yokhudza ndalama ndi zopereka zokhudza zakudya. Mulungu akuperekabe koma pali udindo pa membala aliyense mu mpingo wakuti adzigwira ntchito molimbika ndi kukhara opereka, ndi cholinga chakuti akhoza kukhara msanamira ya Mulungu pofuna kudalitsa ena kudzera mu kupereka kwawo molowa manja.

Mwina kumwamba ndi dziko lapansi latsopano zidzatipatsa ife mpata wakubwelera ndi kuyamba kubzala ndi kukolola zakudya zathu, monga ngati mmene zimakhaliira mu Edeni, ngakhare kuti malemba sanakambe zambiri zokhudza zimenezi.

Zochita: Pezani mutu wina umene mukhoza kuwuzukuta mu njira imeneyi?

8.3 – Kufukukula zambiri

Tayang'ana za mmene nkhani yayikulu ya bayibulo ingasinthire momwe ndime iliyonse yomwe tikuwerenga ingamvekere, komanso mmene zikhulupiliro zingasonkhanidwe pakuwona kaphukidwe ka ina mwa mitu ya mu nkhani yonse. Gawo limeneli likuyang'ana za mmene tingaziwonere mbali zosiyanasiyana za mu bayibulo

kwenikweni za mmene tingapezere molumikizana mu nkhani yayikulumo zimene zingatipatse ife kumvetsetsa kozama malemba amene tikuwaphunzira.

Kuyang'ana nkhani yomwe yalongosoledwa

Kulongosola nkhani ndi mmene ifeyo timayilongosolera nkhani ya m'malemba. Pali nkhani zina mu bayibulo zimene zikhoza kukhara zovuta kuzimva makamaka pamene anthu amene timawadziwa kuti ndi osankhika a Mulungu akupanga zinthu zimene tikuwona kuti ndi zosayenera. Mwachitsanzo, zikutheka bwanji kuti Yakobo anakwatira akazi anayi osiyana kuti apezeke kuti wapanga banja? Ndipo Mulungu akuwoneka kuti alibe nazo vuto! Kuwerenga nkhani ngati imeneyi kwapangitsa kuti pachitike zinthu za dama zosiyanasiyana. Kotero nkhani ya mu bayibulo imayenera kuti iwerengedwe munjira yakuti mukhoza kutsata nkhani yonse ndi kudziwa chimene chimachitika. Nthawi zambiri bayibulo siliyikapo mulomo pankhani ya zolondola ndi zolakwika pa zinthu zimene zikuchitika, kotero munthu amakhara kuti wasiysidwa kuti athe kudzisankhira yekha ngati ziganizo zimene anthu amapanga zili za mzeru kapena zopusa. Kwa Yakobo (ndi mawubale onse a mitala mu bayibulo) timamva zopweteketsa mutu ndi kuvutika mumtima kamba ka mawubale amene sawonetsera pulani ya Mulungu mu chilengedwe.

Kotero mudziwerenga nkhani yokwana, ndipo mudziyilora kuti ilankhule nanu, mudziganizra za zomwe mungaphunzire mu zofooka zawo, kapena kupeza chilimbikitso mu chikhulupiliro chawo. Bayibulo linalembedwa monga zolembedwa zokuti tizilingaliramo, zimene zikutanthawuza kuti olembawo amkayembekeza kuti owerenga adziwerenga ndi kuwerenganso nkhanizo; kupezamo mzeru zatsopano ndi matanthawuzo pamene iwo amalingalira za mawu ena ake, nkhani, zichitochito zobwerezedwa ndi manambala amene anawawona mumalo ena m'malemba.

Mawu obwereza: Mawu ena amakhazikika pamene tiwerenga nkhani zonse za mu bayibulo ndipo amalumikizanita nkhanizi ku nkhani imodzi yayikuluyo. Mwachitsanzo, mawu onena kuti 'chidzukululu' amagwiritsidwa ntchito mmagawo ufunikira kwambiri. Tikumuwona Eva akulonjezedwa 'chizukululu' chimene chidzaphwanye mutu wa njokayo. Abulahamu anamumva Mulungu akumulonjeza zokhudza 'chidzukululu' chimene chidzabweretse Madalitso ake kwa amitundu. Yesaya ananenera zokhudza mwana amene adzatenge ulamuliro wa ufumu wa Mulungu osatha. Mabuku a uthenga wabwino amakamba za mbili ya chidzukululu chake chikubwera kudziko lapansi. Mu buku la Chivumbulutso 'chidzukululu' chinathawitsidwa ku chilombo ndipo chidzukululucho chinategedwa kuti chikalumulire limodzi ndi Mulungu. Mawu amenewa akumangilira ndime zimenezi munkhani imodzi yayikuluyo ndipo amatithandizira kumvetsetsa kufunikira kwa iliyonse mwa nkhanizo.

Zichitochito zobwerezedwa: Nthawi zina timawona zinthu zinazake munkhani zimene zimabweredwa kwambiri. Mwachitsanzo, madzi owinduka amatchulidwa kawirikawiri. Timawona zokhudza madzi amenewa dziko lapansi lisanalengedwe panthawi imene dziko linali lopanda kanthu komanso lopanda mawonekedwe. Akuwonekeranso munkhani yokhudza chigumula pamene Mulungu anachotsa dzanja lake losunga pa chilengedwe chake ndipo dziko lapansi linabweleranso kuchisokonezo. Mose



anatsogolera Aisilayeli kudutsa pamadzi amapereka chithandizo chowakola, ndipo Yoswa naye anawatsogolera anthu kuwoloka mtsinje wa Yolodani ndi kulowa mu dziko la malonjezano. Pamenepa pakhoza kukhara pomwe chiwonetsero cha ubatizo kukhara gawo lofunikira kwambiri la nkhani. Koyamba ndi Yohane m'batizi kenako ndi Yesu. Mu buku la Chivumbulutso pali nyanja ya galasi mu chipinda chimene muli mpando wa chifumu, madzi sakuwindukanso kapena kukokoma, koma akupumula kwatunthu.

Manambala obwerezedwa: Pali manambala ena amene amabwerezedwa mu nkhani zosiyanasiyana ndipo akhoza kumawoneka kuti akulumikizana. Nambala 40 ndi chitsanzo chabwino kwambiri, kwenikweni pofuna kufotokozera chiyesero cha chikhulupiliro. Kotero tikupeza Nowa mu chingalawa m'masiku 40 amene mvula inagwa usiku ndi usana, Isilayeli anayendayenda m'chipululu zaka 40 komanso Yesu m'chipululu masiku 40. Nambala ya 7 nayonso ndi yokondedwa.

Kuwona zokhudza ndakatulo:

Ndakatulo zikupezeka paliponse mu bayibulo, mu magawo a nkhani zolongosola zinthu, mabuku a ndakatulo komanso mu Masalimo. Olemba amagwiritsa ntchito kwambiri mikuluwiko, ndipo nthawi zambiri amazilumikizansitsa ndi zinthu za mu mbiri ndi cholinga chofuna kuyifotokoza bwino mfundo yawo. Mwachitsanzo tikuwona mneneri Yesaya (Yesaya 17:12 -13) kufananiza mitundu yowukira ndi madzi owinduka amene tawawona pamwambapa. Zimenezi zikuthandiza owerenga kuti amvetsetse chisokonezo ndi kusakhazikika kumene iwo anapangitsa, komanso ndi mmene iwo adzathawire kupita kutali ndi mawu a Mulungu ngati mmene madzi a mu Nyanja yofiira anachitira pamene Mose analamura.

Ngati olemba bukuli akukamba za maluwa m'munda, ndi zachidziwikire amakhara akukamba za m'munda wa Edeni ndi mapulani akuti Mulungu adzayenera kubwezeretsa zinthu zonse zimene zinasowa m'mundamo. Mofananira, akamakamba za minga ndi mitungwiza imakhara ili njira yokambira za chilango chomwe chikudza pa mtundu.

Kuyang'ana za mabuku a zinsinsi zovumbulutsidwa

Amenewa ndi mabuku monga Zakaliya, gawo lachiwiri la buku la Daniyele, ndi buku lodziwika bwino 'Chivumbulutso'. Mabuku onsewa ali ndi zifanifani zikulu zikulu zimene pachiyambi zikhoza kukhara zosokoneza. Kuwululidwa kumatanthawuza kuti 'kuvundukula' ngati kuti kudzera mu zithuzithunzi zimenezi timatha kupezamo chiduswa cha chidziwitso cha cholinga cha Mulungu. Kawirikawiri zifanifani zomwe zinagwiritsidwa ntchito mmabukuwa zinayamba zagwiritsidwapo ntchito penapake kotero njira yabwino yokuti tithe kuzizindikira ndi kupita pamalo amene zinagwiritsidwa ntchito poyamba. Buku la Chivumbulutso linadzadza ndi zifanifani komanso zokamba zosiyanasiyana zomwe zinakambidwa mu chipangano chakale. Choncho ife tikuyenera kutengapo nthawi ndithu kuwerenga zimenezi, mwinanso tikuyenera kugwiritsa ntchito mabuku ena ofotokozera za bayibulo kuti tikwanilitse kumvetsetsa zimene zikuvumbulutsidwa.

Mwachitsanzo, pali zosamvetsetseka zomwe zimayendelera zokhudza zilombo za mu buku la Chivumbulutso. Kodi zimachokera kuti?

Kuchokera mu kuwerenga kwathu kochokera mu bayibulo tikhoza kukamba zinthu zotsatirazi:

- Zilombo zinapangidwa limodzi ndi anthu pa tsiku la chisanu ndi chimodzi, koma sizinapatsidwe chifaniziro cha Mulungu monga mmene anthu anapatsidwira.
- Anthu nthawi zambiri akhoza kukhara moyo ngati chilombo makamaka akamuwukira Mulungu.
- Mneneri Daniyele anawona ma ufumu a dziko lapansi m'mafanizidwe a zilombo, zikukhara momuwukira Mulungu ndi kuwononga anthu a Mulungu.
- Buku la chivumbulutso linagwiritsa ntchito chithunzithunzi chomwechi, komanso chinthunzithunzi cha madzi osefukira, ulendo wa Aisilayeli komanso kupititsidwa ku ukapolo ku mayiko ena. Uthenga wake ndi wakuti anthu eni eni a Mulungu kumapeto kwake adzawonekerabe kudzera mu chizunzo ndipo adzalamura limodzi ndi Yesu.

Zimenezi zikhoza kumawoneka kuti zikusokoneza kwambiri. Gawo la phunziro limemeli likuyenera kukupatsani njira zina zowonjezera kuti mupitilize kuwerenga ndi kukulimbikitsani kuti mupitilize kuphunzira ndi kukula. Chachikulu ndi chakuti bayibulo limayenera kulimvetsetsa monga mwa unyinjiki. Mkosavutatu kwa mwana kuti amvetsetse nkhani yayikuluyi komano mmene inu mukuwerenga ndi mmenenso mumamvetsetsa kuti pali zambiri zimene mukuyenera kudzimvetsetsa bwinolomwe, komanso kuti kodi timafunana motani pakufunika kwa kugawana maganizo athu, mafunso ndi malingaliro.

Funso lokambirana: Tapezani mikuluwiko ina imene ikubwerezedwa mu bayibulo.

8.4 – Kukonzanso zinthu zonse mokhudzana ndi nkhani

Tafikano kumapeto kwa maphunziro athu, pali chiyembekezo chakuti mwapeza zinthu zina zofunikira zowerengera, kumvetsetsa ndi kugwiritsa ntchito zomwe mwapeza mu bayibulo. Gawo ili ndi la munthu pa yekha kamba kakuti likubweretsa pamodzi chinachake chokhudza ine pa ulendo okhudza kufufuza powerenga bayibulo ngati nkhani imodzi yayikulu komanso mmene inasinthira kumvetsetsa kwanga kwa zinthu pa zomwe Mulungu akuchita komanso mmene ingandikhuzire.

Kukonzanso kaganizidwe kathu

Mozungulira kulalikira uthenga wabwino - Tikuyenera tiwulanditse uthenga ofunikira kwambiri umene unalankhulidwa chikhalire, umene mwanjira ina unatayika kapena

kusokonezedwa mu zikhalidwe zambiri za chikhilisu. Uthenga wabwino ndi nkhani yayikulu koposa, kuposa mmene ife timayidziwira. Yesu ndiye Mfumu yoona ya onse ndipo aliyense amene amadzipereka ku ulamuliro wake amalandilidwa mu banja la Mulungu. Uthenga wathu wa chipulumutso siwukungokhudza kupulumuka kudziko ndi uchimo wake okha ndi chilango chili mkudza. Komanso ndi okhudza kupulumutsidwa ndi Mulungu kumphamvu zimene zatigwira ife ukapolo, kotero uthengawo umabweretsa chiyembekezo ndi machilitso ku chilengedwe chimene Mulungu amachikonda.

Anthu okhulupilira ndi chilengedwe chatsopano - Kumwambatu si malo ena ake akutali mmwambamu, kutali kwenikweni. Monga okhulupilira, ifetu tatenga kale gawo mu chilengedwe chatsopano. Kumwamba ndi dziko lapansi zalumikizana mwa ife. Chidziwitso chimenechi chasintha kapempheredwe kanga, mmene ineyo ndimalambilira, mmene ine mwini ndimaziganizilira komanso ziphingo zimene ndimakumana nazo. Tsopano si zongokhudza ine ndekha, kuyesetsa kuchita zabwino kwambiri. Ndikhoza kudziwano kupezeka kwa mphamvu ya Mulungu kulikonse komwe ndinagapite.

Chikondi mmalo mongosunga chilamulo - Ngakhare kuti mipingo yambiri imawoneka kuti ili ndi chidwi kwambiri ndi mawonekedwe akunja ndi zomwe ungachite kapena sungathe kuchita monga mkhristu, nkhani yomwe tili nayo kwenikweni ndi yokhudza kukula mu chikondi chathu. Ichi ndi chizindikiro cha kukula kwa mkhristu ndipo ndi mulungu umene Mulungu amawoneka kuti amakhara nawo chidwi, ndiye nafenso tikuyenera kutero.

Mpingo ndi ofunika mu cholinga cha Mulungu - Mulungu anasankha kudziwonetsera yekha kudzera mu magulu eni eni a pamoyo wa munthu, kuwonetsera mphamvu za Mzimu Oyera pakusinthira moyo ndi cholinga chakuti ukhare olowa manja mopitilira, okhululuka, wachifundo ndi kusamala za ena, izi si chinthu chimene chimangochitika. Tikufunika anthu ena mmiyoyo yanthu amene amatikonda, amatitsogolera, kutidzudzula, kutipemphelera ndi kutilimbikitsa. Timawafunanso iwo amene sali monga ife, amene ndi a chikhalidwe chosiyana ndi chathu komanso okulira mu mtundu wina wa zochitika, amene akhoza kutsutsana naye, kapena kutikhumudwitsa ngakhalenso kutida. Anthu amenewa ndi anthu a mtengo wapatali amene Mulungu amawagwiritsa ntchito kuti atikuze.

Kumbukirani, chikondi ndi chizindikiro cha kukula, ndipo ndichosavuta kuwakonda iwo amene amatikonda ife, ngakhaletu anthu osakhulupilira nawonso amakonda anthu amene amawakonda. Mpingo weniweni umene ukugwira ntchito malingana ndi pulani ya Mulungu umakhalanso ndi mikangano, kusiyana maganizo kapena kachitidwe ka zinthu kosiyana ndi machitidwe ake. Koma ukhozanso kukhara malo amene anthu othodwa amakondedwa ndi kuchilitsidwa, kumene zikhalidwe zosiyanasiyana zimaloredwa ndi kukondweleredwa ndiponso kumene anthu owonelera amadabwa kuti gulu la anthu osiyanasiyana oterowo amathanso kukondana

Chidwi chathu si mpingo ayi koma ufumu - Ndi mmene timawulemekezera mpingo tikamasonkhana, tikhoza kupusisidwa poganiza kuti tikuyenera kuchita chotheka kuti mpingo ukhare ndi ulemelero mmene tingathere. Komano cholinga chenicheni si chimenencho. Mpingo ulipo ndi cholinga chogwira ntchito molingana ndi Mulungu ndi cholinga chofuna chilengedwe chonse pansi pa ulamliro wa khristu. Cholinga cheni cheni ndi ufumu. Chimenechi ndicho choyenera kuti ife tidzipereke kwatunthu kuchimenechi. Ufumu umakula anthu akachilitsidwa ndi kumasulidwa komanso akakhara ndi cholinga chokhara uthenga wabwino kwa anthu oyandikana nawo komanso mmisonkhano.

Kusintha kalalikidwe kathu

Funso lomwe limakhara mmutu mwanga nthawi zonse ndi lakuti, 'Kodi Yesu ndiye chipambano?' nthawi zambiri timapanga misonkhano yathu ya kumpingo kukhara yotikhuza ife tokha. Timayimba nyimbo zimene zikukamba mmene ife timalimbikilira komanso mmene timawukondera mpingo. Tikhoza kulalikira mawuthenga amene amalimbikitsa anthu kusiya ntchimo, kukhara odzipereka kwambiri kwa Mulungu, kukhara odzipereka ku zolinga za Mulungu. Tikhoza kuchititsa anthu akamaweruka kukhara akudzimva kuti zilibwino chifukwa cha kudzipereka kwawo kapena akudziwona kuti iwo ndi olephera ndi kudziwona operewera kuti sangakwanitse kuchita moyenera pamoyo wawo wa chikhristu. Mwanjira ina iliyonseyo, kuwaweruka anthu ndi malingaliro okuti ayesetse zimabala zipatso zochepa za Mulungu. Kulalikira kwathu kumayenera kuti kudziwonetsera Yesu kukhara kalonga yekhayo amene ali weni weni. Yesu yekha ndi amene angapulumutse iwo amene asochera. Yekhayo amene anamumvera Mulungu mowona ndi yekhayo amene angapangitse kuti Mzimu Oyera adzadze miyoyo yathu ndi kubalira Mulungu zipatso mkati mwathu. Timachita bwino kawirikawiri tikamawawelutsa anthu titawalalikira ndi chizwizo chatsopano cha chimene Yesu ali komanso cha zimene Yesu wawachitira, ndiponso za zimene iye akuchita m'miyoyo komanso mwa iwo amene amamukhulupilira iye.

Kulinganizanso mipingo yathu

Mipingo nthawi zambiri imaliwona dziko ngati mdani wawo, ndipo nthawi zambiri imayesetsa kusafuna kutenga nawo gawo mu zochitika zake ndi dziko. Kuliwona dziko monga momwe Mulungu amalilonera, chilengedwe chabwino chomwe chikufunikira chiwombolo, zikhoza kutithandiza kuti tifikire njira yathu ndi kukhara opereka chikhumbokhumbo kwa anthu. Sitidzakhara ndi mantha akukhala opakidwa ndi tchimo koma tidzaziwona tokha kukhara njira za chifundo cha Mulungu chofikira kwa anthu amene akuwufunitsitsa uthenga wabwino. Ife tayitanidwa kuti tiyambe kulisinthira dziko latizungulirali, kukhara moyo umene ukuwonetsera zimene zikubwera kutsogolo mmalo mowonetsera moyo umene ife tikudutsamo.

Munjira imeneyi, pali mayitanidwe akulu ochokera kwa Mulungu kuti ife tiwayang'anire iwo amene ali osowa, kupita kwa iwo amene ali ovutika, kuwamenyera ufulu wa chilungamo iwo amene akuponderezedwa. Ife sitinayambe tayitanidwa kuti tikhare anthu amene amasamala za miyoyo ya anthu ngakhale kukhara ndi chidwi cha pamatupi awo. Zimenezi ndithu zikhoza kubweretsa chisokonezo makamaka kwa

anthu amene amapindula kudzera mu kuwapondereza anthu. Gawo lina la kulamulira kwathu ndi Khristu ndi lakuti tidutse m'amasawutso ndi iye, kudzera mu kukanidwa, kuzunzidwa, ndi kuvutidwa kowonekeratu. Komabe pakulamulira kwathu ndi iye timayamba kulikonda dziko mmene iye amalikondera, ngakhare ndi amene amatizunza.

Kukonzanso zolinga za utumiki wathu

Cholinga chathu si kukuza mipingo yathu kapena kukhara otchuka m'midzi ndi m'mizinda yathu. Cholinga chathu ndi chakuti tibweretse ufumu wa Mulungu ku dziko lonse lapansi kumene panopa kulibe. Zimenezi zikuyenera kukhara m'miyoyo yathuyi, m'mabanja mwathu, m'malo amene timagwirako ntchito, m'madera athu komanso kudziko lililonse ndi mitundu ya anthu padziko pano. Mu zimenezi ndi momwe chidwi chathu chimayenera kuchokera, ngakhare zili ndi dipo lovuta komanso zosawutsa. Palibe magulu akuluakulu a anthu amene sanamvepo nkhani yabwino yakuti Yesu ndiye Mfumu yeniyeni komanso kuti iwowo akhoza kulowa mu ulemelero ndi kupeza nawo zabwino za mu ufumu wake. Iwo sanawonepo mpingo ukuwonetsera umboni wamoyo okhudza zimenezi. Mulungu akufunafuna iwo amene akhoza kupanga ubale ndi iye pamene iye akufunafuna nkhoa zosochera ndi kuzibwezeretsa kwawo. Cholinga chake ndi chimene chikuyenera kukula kuposa cholinga chathu.

Chiyembekezo chomaliza

Chiyembekezo cha pamtima panga ndi chakuti kudzera mu maphunzirowa, mwakula ndi kuyamba kumukonda Yesu kwambiri mu zozizwa zake ndi mu ulemelero wake. Ndipemphero langa kuti mwa inu mukhara osangalala kuzilumikizitsa mu nkhani imene Mulungu akulemba panopa pamene akubweretsa zinthu zonse pamodzi kukhara panso pa ulamuliro wa Khristu.

Funso lomaliza: Kodi mwaphunzirapo chani mu maphunziro amenewa?

Zomwe mwatolapo

Zomwe mwatolapo

Zomwe mwatolapo



Colin Nicholas ali pa banja, anakwatirana ndi Pam, ndipo ali ndi ana atatu. Panopa akukhara ku South Africa, ndipo akutsogolera maphunziro ku bungwe lotchedwa Issachar Alliance, bungwe lakulumikizansitsa opanga ophunzira ndi a zichitochito zodzala mipingo.

Kupanga ndi masanjidwe ndi Pepperfish.co.uk
*Pepperfish kupereka ntchito zopangira mabizinesi,
zachifundo ndi mipingo padziko lonse lapansi.*

